



MAZIKO A DZIKO LA UFULU

(FOUNDATION OF A FREE SOCIETY)

MLEMBI : EAMONN BUTLER

Maziko a dziko la ufulu

MAZIKO A DZIKO LA UFULU

(Foundations of a free society)



Montfort Media - Balaka

Maziko a dziko la ufulu
MAZIKO A DZIKO LA UFULU

Lolembedwa ndi

Eamonn Butler

Wotanthauzira:

John Nyangulu

Wozukuta:

Prescot Chilewani

Cover Design:

Gray Velemu

ISBN:- 978-99908-0-815-5

Printed in 2020

ZAMKATIMU

Mlembi wa bukuli	v
Mawu otsogolera olembedwa ndi Ali Salman	vi
Kuthokoza	ix
Chidule	x
1 CHIYAMBI	1
Cholinga cha bukuli	1
Kalembedwe ka bukuli	2
2 UBWINO WA UFULU PA CHUMA NDI MAKHALIDWE	4
Dziko la ufulu	4
Nkhani ya ufulu pa makhalidwe	7
Nkhani ya ufulu pa chuma	15
3 NSANAMIRA ZA DZIKO LA UFULU	27
Dziko lopanda boma	27
N'chifukwa ninji boma liyenera kupatsidwa malire	29
Njira zoikira boma malire	40
Kuika malamulo	45
4 KUFANANA NDI KUSIYANA	49
Kufanana m'dziko la ufulu	49
Mitundu ya kufanana	50
Kufanana pa zotsatira	56
Kufanana ndi chilungamo	61
Kuwononga kwina kwa chikhulupiriro chakuti anthu ayenera kuthandizidwa mofanana	65
5 UFULU OCHITA MALONDA	69
Ntchito zachuma zam'misika ya ufulu	69
Mmene ungatukukire pachuma	72
Mmene misika imayendera	79
Malonda pakati pa mayiko	84

Maziko a dziko la ufulu

6	KATUNDU NDI CHILUNGAMO	88
	Katundu wa anthu osati boma	88
	Malamulo a chilungamo	92
	Mphamvu ya lamulo	98
	Ufulu wa anthu	103
7	DZIKO LOSAKAKAMIZIKA	106
	Kulamula popanda malamulo	106
	Kulolerana	109
	Vuto la khalidwe la kusadzikonda	119
8	KUPEREKA UMWINI KWA ANTHU OIMA PAOKHA NDI KULUMIKIZANA KWA MAYIKO ONSE	124
	Kusamuka kwa anthu ndi luso lamakono	124
	Kupititsa patsogolo dziko la ufulu	125
	Kugwira ntchito kwa ufulu wa katundu	127
	Ntchito zotumikira anthu popanda boma	135
	Kulumikizana kwa mayiko onse ndi malonda	142
	Kufunika kwa mtendere	146
9	NKHANI YONSE MWACHIDULE	149
	Nkhani ya ufulu	149
	Boma lokhala ndi malire	149
	Kufanana kwakukulu	150
	Ufulu pa zachuma	150
	Chilungamo ndi mphamvu ya lamulo	151
	Dziko losakakamizika	152
	Dziko lapansi la ufulu	153
	Zokhudza IEA	154

MAZIKO A DZIKO LA UFULU

Mlembi wa bukuli

Eamonn Butler ndi mkulu wa bungwe la Adam Smith, lomwe ndi-lodziwika bwino pokonza ndondomeko zoyendetsera zinthu. Anachita maphunziro aukachenjede pa kayendetsedwe ka chuma, kaganizidwe kozama komanso m'mene anthu amaganizira, ndikutenganso digiri ya PhD pa sukulu yaukachenjede ya St Andrews m'chaka cha 1978. M'zaka zam'ma 1970 anagwirapo ntchito ku Nyumba ya Malamulo yaku United States, komanso ankaphunzitsa phunziro la kaganizidwe kozama pa sukulu ya ukachenjede ya Hillside mdera la Michigan, asanabwerere ku UK kukathandizira kukhazikitsa bungwe la Adam Smith. M'chaka cha 2012, Edinburg Business School inamupatsa digiri ya ulemu ngati katswiri pa zolembalemba. Pakadali pano iyeyu ndi Mlembi wa bungwe la Mont Pelerin.

Eamonn ndi mlembi wa mabuku a akatswiri pa nkhani za kayendetsedwe ka chuma monga Milton Friedman, F. A. Hayek ndi Ludwig von Mises omwe akudziwika kumene komanso buku lotsogolera pa Sukulu ya kayendetsedwe ka chuma ya Austrian School of Economics. Ku IEA, walembako mabuku otsogolera okhudza Adam Smith, Ludwig von Mises komanso mfundo zokhudza kusankha kwa anthu. Iyeyu analemba nawo buku la mbiri yoteteza malipiro ndi mitengo ya zinthu, komanso mabuku ambiri okhudza mphamvu ya kaganizidwe kaubongo. Mabuku ake omwe walemba posachedwapa omwe apereka chikoka kwa anthu ndi monga: *The Best Book on the Market*, *The Rotten State of Britain* ndi *The Alternative Manifesto* ndipo kawirikawiri amakhala akulemba kunyumba zosindikiza ndi kuulutsa mawu.

Maziko a dziko la ufulu

Mawu otsogolera

Nthawi zambiri mavuto azachuma ndi zandale akhala akudzetsa mpungwepungwe pa nkhani za ufulu. Munthawi ya kulowa pansi kwakukulu pa nkhani za chuma ndi mafakitole, mayiko onse ochita bwino anateteza malonda pokweza misonkho. Mchitidwe wongodzidzimukirawu unangowonjezereka. Izi zinakuza mpungwepungwe pa ndale komanso malo ndi kupititsa patsogolo mavuto azachuma. Kudza kwa maulamuliro olimbikitsa kuchitira zinthu pamodzi kuna-pondereza ufulu wapachiweniweni, pandale ndi chuma pa mayiko okwana theka a padziko lonse lapansi.

Posachedwapa, upandu wa pa 9/11 komanso mmene dziko la Amereka lidachitira pobwezera zinapangitsa kuti mfundo zikuluzikulu zikhazikitsidwe zomwe zimapondereza ufulu pofuna kulimbitsa chitetezo. Chimodzimodzi, mavuto azachuma padziko lonse omwe anayamba mchaka cha 2008, omwe anayambira m'dziko la Amereka, anatsatananso ndi kuchuluka kwa ziletso, malamulo oyenera kutsatidwa komanso zitetezo. M'malo modalira mfundo yopereka ufulu pochita malonda, maboma mbali zonse za nyanja yayikulu ya Atlantic agwiritsa ntchito ndalama zambiri zamisonkho pofuna kupulumutsa mabizinezi omwe samachita bwino.

Zoopseza ufulu zilipo ndithu. Theka la theka la mzaka zana lapitalo, dziko lonse linayamba kutsatira mfundo zochita zinthu poyera komanso mosabisa m'mayiko a mugwirizano wa Soviet ndipo kenaka anakondwera ndi kugwa kwa chipupa chogawanitsa dziko la Berlin. Zobetchera zatsopano zadza tsopano zomwe zili kufuna kuima pawokha kwa maiko ku Ulaya komanso magulu ofuna kusintha zinthu m'mayiko a kuchigawo chapakati kummawa. Ngati zimenezi siziunikiridwa bwino zidzachepetsa ufulu. Ku Ulaya, mchitidwe wa mayiko wofuna kudziimira paokha, ngakhaleenso kusankhana mitundu ukuchitika ngakhale ufulu pa ndale uli wochulukirapo. – ufulu wodzilamulira ulipo ndithu. M'mayiko a mchigawo Chapakati Kum'mawa, mchitidwe wofuna kusintha zinthu motsogoleredwa ndi chipembedzo ukukula - choncho nkhani za malonda ngakhaleenso ndale sizikuyenda bwino.

Maziko a dziko la ufulu

Ngakhale mavutowa ali chomwechi, anthu zaka zino ali ndi ufulu munjira zambiri kusiyana ndi anzawo omwe anakhalapo zaka zana zapitazo. Kupita patsogolo pa luso la kufalitsa mauthenga ndi kulumikizana kachotsa zotchinga zonse. Mwachitsanzo, m'dziko la China, Li Chengpeng ndi mlembi wodziwika bwino komanso amapereka ndemanga zake pa kakhaliidwe ka anthu: tsamba lake la pa intaneti lotchedwa Sina Weibo limatsatidwa ndi anthu pafupifupi mamiliyoni asanu ndi limodzi. Mnthawi ya Kuukira boma kumene kunkachitika m'maiko achiluya, masamba amchezo anathandizira kufalitsa nkhani zokhudza kupita patsogolo pa kakhaliidwe ka anthu ndi ndale. Ngati uthenga uli mphamvu, ndekuti luso lofalitsira uthenga lampatsa munthu mphamvu. Malire a mayiko adakalipo, koma pakali pano sakudetsa nkhwawa kwenikweni.

Potengera zimenezi, kusindikizidwa kwa buku la Eamonn Butler kukanakhala kosafunikira. Maziko a dziko la ufulu likuwonjezera ku gulu la zolembe zatsopano pa ufulu. Ukatswiri wa Butler wagona mukuthekera kwake kotambasula mfundo zovuta ndinso za chikoka mu chingerezi chosavuta kumvetsetsa. Iyeyu ankagonjetsa mosavuta mfundo za otsutsana naye popereka zitsanzo zenizeni zopezeka mdziko zomwe zinkafotokozera maganizo ake ndi kuthandizira mfundo zake.

Bukuli ndichiyambi chabwino koposa kwa omwe akufuna kumvetsetsa mfundo zenizeni za dziko la ufulu. Bukuli lidzakhalsanso lofunikira kwa olimbikitsa ufulu m'mayiko mmene mfundo zimenezi sizidziwika, ngakhalsenso amene amateteza ufulu m'madera mmene ufulu weniweni umaphwanyidwa.

ALI SALMAN

Founder and Executive Director,

Policy Research Institute of Market Economy (PRIME),

Islamabad, Pakistan

September 2013

Maziko a dziko la ufulu

Maganizo omwe afotokozedwa m’bukuli, monga zonse zosindikizidwa ku IEA, ndia mlembi osati abungweli, omwe amaliyang’anira, mamembala a khonsolo yamaphunziro kapena ogwira ntchito aku-luakulu. Kupatula zolembe zina, monga kusindikiza zophunzitsa, zolembalemba zonse za IEA zimaunikidwa ndi akatswiri osachepera awiri pa zamaphunziro kapena akafukufuku omwe ndi anamandwa mugawolo.

Kuthokoza

Chithokoza chapadera chipite kwa Nigel Ashford, yemwe walola mlembiyu kuti agwiritse ntchito maganizo ake ochuluka opezeka m’buku lake lotchedwa *Principles for a Free Society*. Zogwiritsa ntchito zina zachokera m’ mabuku a H. B. Action, lotchedwa *The Morals of Markets*, J. S. Mill, mubuku lake lotchedwa *On Liberty*, Madsen Pirie, mubuku lotchedwa *Freedom 101*, Richard Wellings, mubuku lotchedwa *A Beginner’s Guide to Liberty*, Enerst Benn, mu buku lotchedwa *Why Freedom Works* komanso mubuku lotchedwa *The Morality of Capitalism* lolembedwa ndi Tom Palmer.

Maziko a dziko la ufulu

Chidule

- Ufulu umadzetsa chitukuko. Umapangitsa anthu kuonetsa luso, kupanga chinthu komanso mwatsopano, kupanga chuma chimene poyamba panalibepo. Mayiko omwe ali ndi ufulu anachita bwino. Omwe alibe ufulu adakasaukabe mu umphawi.
- Anthu okhala mdziko la ufulu sakhala ndi chuma popondereza anzawo, monga m'mene amachitira achuma m'mayiko omwe ufulu ndiwochepa. Sangakhale achuma posaukitsa ena. Amakhala ndi chuma powapatsa anzawo zomwe akufuna komanso kutukula miyoyo yawo.
- Omwe amapindula kwambiri ndi kusintha pa chuma m'mayiko ndi anthu osauka. Mayiko omwe muli ufulu anthu ake sasiyana kwambiri pa chuma kusiyana ndi mayiko opanda ufulu. Anthu osauka m'mayiko omwe muli ufulu amakhala ndi mwayi opeza zosangalatsa m'miyoyo yawo zomwe sankaziyembekezera m'zaka zochepe zomwe zadutsa, zosangalatsa zomwe zimangopezeka kwa anthu olamulira m'mayiko opanda ufulu.
- Malonda pakati pamayiko amapezetsa ochita malonda misika yatsopano ndi kuchotsa muumphawi wadzaoneni anthu oposa biliyoni imodzi m'zaka makumi awiri zapitazi. Ndithudi, ufulu ndi chida chimodzi chofunikira kwambiri komanso chopindulitsa mu mbiri yamunthu.
- Kuyesera kwa maboma kuti afananize chuma kapena zomwe anthu amapeza ndikobwezeretsa zinthu m'mbuyo. Izi zimbwezera m'mbuyo mtima olimbikira komanso oyambitsa mabizinezi komanso zimagwetsa mphwayi anthu kuti awonjezere mpamba womwe ungapangitse kuti dziko lonse lipeze zochulukana.
- Dziko la ufulu silopezekeratu. Limapezeka potengera zochita za anthu, potsata malamulo omwe amapititsa patsogolo kukhalira limodzi mwamtendere. Silimangoperekedwa ndi atsogoleri andale.
- Udindo wa boma umakhala wochepe kwambiri m'dziko la ufulu. Boma limakhalapo kuti liteteze anthu ake poonetsetsa ndi

Maziko a dziko la ufulu

kulimbikitsa chilungamo. Silimakakamiza anthu ake kukhala ndi katundu wofanana ndipo sililetsa zochitika chifukwa chakuti anthu ena sakugwirizana nazo kapena akuziona kuti ndizolakwika. Atsogoleri sangapondereze nzika pofuna kuti apindule okha, kukondera anzawo, kapena kugwiritsa ntchito mphamvu zawo pozunza adani awo.

- Boma la m'dziko la ufulu limakhala logonjera ku mphamvu ya lamulo. Malamulo ake amagwira ntchito pa aliyense mofanana. Pakuyenera kukhala ndondomeko yovomerezeka ndi lamulo pa mlandu uliwonse, kuyesedwa mlandu mosakondera, komanso osamangidwa nthawi yayitali usanazengedwe mlandu. Oganiziridwa kuti alakwa akuyenera kutengedwa ngati osalakwa mpaka atapezedwa kuti ndiwolakwa, ndiponso munthu asavutisidwe pozengedwa mlandu umodzi kambirimbiri.
- Kulolerana makhalidwe ndi maganizo a anthu ena ndizo zipindulitsa dziko. Nthawi zonse choona sichimadziwikiratu; chima-dziwika pamene maganizo osiyanasiyana aperekedwa. Sitimadalira oweruza milandu kuti atsekereze maganizo olakwika okhaokha. Iwowa atha kutsekereza mwangozi maganizo komanso njira zomwe zikanapindulira koposa dziko mtsogolo.
- Njira zamakono zofalitsa uthenga zikulepheretsa maboma ankhanza kubisa zochita zawo ku dziko lonse lapansi. Zotsatira zake, mayiko ambiri akutenga nawo mbali pa ntchito zamalonda komanso zokopa alendo, ndipo maganizo atsopano akufalikira. Anthu ambiri akuona ubwino wa ufulu pa zachuma komanso kakhaliidwe ka anthu, ndipo akumaufuna ndithu.

Maziko a dziko la ufulu

Maziko a Dziko la Ufulu

1 CHIYAMBI

Cholinga cha Bukuli

Bukuli likufotokoza mfundo zofunikira zomwe zimapanga dziko la ufulu. Chifukwa chomwe likufunikira nchakuti ufulu weniweni wamunthu, pakati pa anthu, pandale, komanso pazachuma ndiwo-sowa kwambiri – ngakhale m’mayiko omwe amadziona kuti ali pa ufulu. Pali kusiyana kwakukulu pakati pamayiko omwe ali ndi ufulu kwambiri ndi omwe ali ndi ufulu pang’ono, pomwe m’dziko lililonse munjira ina kapena inzake, khalidwe la anthu komanso chuma zimaletsedwa kapena kulamuliridwa ndi adindo kapena andale. Kuletsa ndi kulamulidwa kumeneku kwakhalapo nthawi yayitali, ndipo kumalepheretsa zambiri m’moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, mpaka zakhala gawo la chikhalidwe chathu. Anthu amangoziona ngati ndi gawo la moyo, zachibadwa komanso zosapeweka.

Zotsatira zake n’zakuti anthu ambiri padziko lapansi, ngakhale amakhulupirira kuti ali ndi ufulu, sangathe nkuganizira komwe kuti ufulu weniweni umatanthauza chani – ndiochepa okha amene amamvetsa mmene dziko la ufulu lingakhalire komanso mmene lingayendere.

Ngakhale zili choncho, anthu ambiri amafuna ufulu. Amafuna kuchita malonda mopanda kukatenga ziphaso zochuluka zowavomereza. Amafuna kukhala otetezeka pamene akukhala mnyumba zawo, kumalo awo ochitira ulimi komanso kumalo ogwirira ntchito, osati kukhala pachiopezo ndi andale kuti atha kuwathamangitsamo ndi kuwachita chipongwe. Amafuna kukhala ndi ufulu wosankha chomwe chili chabwino pabanja lawo osati kuchita zomwe adindo alamula. Amafuna kukhala miyoyo yawo mosafuna kupereka ziphuphu kwa apolisi komanso kusavutitsidwa ndi amaudindo.

Ichi ndi chifukwa chake kuli kofunika kwambiri kufotokozera mfundo zenizeni za ufulu wakakhalidwe ka anthu komanso pa chuma. Masomphenya enieni a chimene ufulu uli, komanso mmene umagwirira ntchito, ndiwo maziko omwe angapangitse anthu kukhala ndi dziko lenileni la ufulu.

Maziko a dziko la ufulu

Kalembedwe ka Bukuli

Mutu 2 ukufotokoza osangoti za ubwino pa chuma wopezeka m'dziko la ufulu okha koma ukufotokozanso za makhalidwe omwe amadza kaamba ka ufuluwo. Ufulu pa chuma komanso mdziko zagona pa zikhulupiriro zamphamvu – osati zikhulupiriro zimene zimabetchera madongosolo ena a makhalidwe koma zikhulupiriro zimene zimathandizira, kulimbitsa ndi kuwapititsa patsogolo. Ufulu ndiwa aliyense.

Mutu 3 ukulongosola za m'mene dziko la ufulu lingaperekere zofuna za anthu mosavuta komanso mokwanira mosadalira atsogoleri amphamvu kuti awauze anthu zochita. Kunena zooni, ukufotokoza zifukwa zomwe boma likuyenera kuchepetsera malire komanso ulamuliro ndipo ukusonyeza mmene dziko la ufulu likuyenera kukhalira komanso mmene lingagwirire ntchito.

Mutu 4 ukufotokoza za kulimbana komwe kumaonekera pakati pa ufulu ndi kufanana. Ukukamba kuti ufulu wochuluka umadzetsa kufanana kwakukulu pa chilichonse chofunikira. Koma kukakamiza kufanana pa zotsatira pakati pa anthu kumapondereza mfundo za ufulu ndi kuwononga zinthu kwa nthawi yayitali.

Mutu 5 ukufotokoza za dongosolo pa nkhani zachuma mdziko la ufulu, kufotokoza mmene nkhani za misika zimapangitsa anthu kutukuka ngati boma silikulamulira. Mutuwu ukulongosola za malamulo omwe timawatsata kuti ndondomekoyi iyende bwino, kufunikira kwenikweni kwa ufulu pa malonda popititsa patsogolo mgwirizano pakati pa anthu.

Mutu 6 ukuunika mfundo zokhudza katundu ndi chilungamo. Mutuwu ukulongosola m'mene malamulo a dziko la ufulu akuyenera kufikira kwa aliyense, kugwira ntchito pa anthu omwe ali m'maudindo komanso kwa anthu wamba mosasiyana, ngati kukakamizana ndi kuchitirana nkhanza kuyenera kuchepetsedwa. Ndipo ukulongosolanso mmene dziko la ufulu lingalemekezere ufulu weniweni wa anthu.

Maziko a dziko la ufulu

Mutu 7 ukufotokoza mwatsatanetsatane m'mene dziko la ufulu limayendera osafunanso kulamuliridwa ndi adindo. Ukukamba za malamulo okhudza makhalidwe ovomerezeka omwe amakhazikitsa ndondomeko yoyendetsera bwino dziko koma opanda kupondereza ufulu. Ukutsindika za kufunikira kololerana ndipo ukufotokoza mavuto opanga dziko potengera chikhalidwe chosadzikonda.

Mutu 8 ukukamba za momwe tingakhazikitsire dziko la ufulu lomwe panalibe. Ukusoyeza kufunikira kowonjezera zokometsera m'moyo wa tsiku ndi tsiku, ndi kuipa kokakamiza ziganizo kuchokera kwa adindo. Ukusonyezanso ngakhale m'mene zofunikira pa umoyo wamunthu zingaperekedwere popanda boma. Mutuwu watsindikanso za kufunikira kwa ufulu pochita malonda ndi mtendere.

Maziko a dziko la ufulu

2 UBWINO WA UFULU PA CHUMA NDI CHIKHALIDWE

Dziko la ufulu

Tanthauzo la ufulu

Ufulu (kapena kumasuka – Mu chingerezi mawuwa amagwiritsidwa ntchito mosinthanasinthana) umatanthauza zambiri osati kusangokhala mndende kapena muukapolo kokha. Umatanthauza kukhala omasuka kuchita chinthu, kulankhula ndi kuganiza zomwe wasankha, popanda kuopsezewa ndi ena kuphatikizapo adindo. Ukukhudza moyo wamunthu pawekha, wa m’banja, kapena wapagulu ngakhale maganizo ako okhudza ndale komanso pochita zachuma ndi ena.

Dziko la ufulu limayenenera kulimbikitsa malingaliro oterowa. Potengera mbiri ngakhalenso pano, ufulu waonetsa kuthekera kodzetsa chuma ndi kuchifalitsa kwa nzika. Ufulu wasonyeza kuti ndi chida chopindulitsa komanso chopangitsa mtundu wa athu kuchitapo kanthu. Ufulu wapititsa patsogolo miyoyo ya anthu– makamaka osaukitsitsa – padziko lonse lapansi.

Ufulu umatanthauza kuti palibe chotchinga chomwe chaikidwa mu njira yako, ndipo palibe chokuletsa kuchita chimene wasankha. Umatanthauza kusakakamizidwa, kusalamuliridwa, kusawopsezewa, kusachititsidwa mantha, kusaumirizidwa, kusasokonezedwa, kapena kusanamizidwa ndi ena. Ukutanthauza kukhala m’ moyo wako osachitidwa chipongwe, osanamizidwa, osaberedwa kapena osapwetekedwa. Izi zili chonchi chifukwa mfundo ya ufulu imagwira ntchito mofanana kwa aliyense m’ dziko la ufulu. Palibe aliyense waife yemwe ali wololedwa kulowerera, kupsinja kapena kupweteka ena, zomwe zingachotse ufulu womwe nawonso alinawo.

Choncho ufulu umakhalapo pokhapokha ngati anthu ena sakupwetekedwa. Ufulu wako woponya chibakera umathera pomwe mphuno yanga yayambira. Munthu suukugwiritsa bwino ntchito ufulu wako ngati ukuopseza, kukakamiza, kuba, kupanga chipongwe, kapena kupha ena ndiye kuti sukutsata zomwe ufulu umafuna. Mosemphana,

Maziko a dziko la ufulu

ukuphwanya ufulu wawo wosachitidwa nkhanza. Iyi imatchedwa mfundo ‘yosapwetekana’: uli omasuka kuchita zomwe ukufuna pokhapokha ngati sizikuwapweteka ena.

Chimodzimodzi, sukuphwanya ufulu wa aliynse pokana ukali wawo. Ufulu ndi mfundo yosapwetekana zimakulolani kuletsa ena kuti asakupwetekeni komanso amene mumawakonda. Ndinu ololedwa kulowererapo pofuna kuletsa kuti ena asapwetekedwe, kuphatikizapo alendo – ngakhale ntchito yoteteza nzika zinayi nthawi zambiri imasiyidwa m’manja mwa apolisi komanso owona za malamulo.

Komabe, mfundo yosapwetekana imagwira ntchito pomwe kupweteka kwachitikira anthu ena. Mfundoyi imakulola kupanga zomwe ukufuna ndi thupi lako komanso katundu wako, koma usaphwanye ufulu wa ena pochita izi. Mwachitsanzo, utha kupereka chuma chako chonse, kulolera kuvulala popanga chinthu choopsa, kapena kudzipweteka thupi lako, bola zonsezi zisapweteke munthu wina. Ndipo ngakhale anthu ena angayesere kukuletsa kudzipwetekaku, sangakugwire kuti usachite, ngati iweyo wasankha wekha.

Ufulu ndi udindo wa boma

Zitha kumveka mwankhanza kunena kuti tilibe ufulu wolowerera pa zochita za ena, ngakhale zili zowakomera iwo. Koma palibe mmodzi waife yemwe angadziwe chowakomera ena. Anthu pawokha ndiwo angakhale oweruza abwino pa zochita zawo. Amamvetsetsa bwino zikhulupiriro, nyengo zawo, zosowa zawo, zofuna zawo, mantha awo, chiyembekezo chawo, zomwe akufuna atazifikira koposa wina aliynse. Amadziwa bwino zolinga zawo ndi zochita zawo.

Anthu apadera akhoza kukondera poweruza ena. Ngati tingalole anthu kulowererapo pa ufulu wa ena, atha kutero mnjira (modziwa kapena mosadziwa) zokomera iwo okha osati munthu winayo. Ichi ndichifukwa chake mphamvu zoletsa ena zimaperekedwa m’manja mwa apolisi ndi akhothi, omwe – mu dziko la ufulu weniweni – amatha kukhala osakondera.

Maziko a dziko la ufulu

Tonsefe mmene tilili, zokhumba zathu aliyense zitha kukwaniritsidwa pokhala mdziko mmene tili pa ufulu. Udindo wa boma m'dziko limeneli ndi kuteteza ufulu wathu kuti ena asatiphwanyire – ndi kuwufikitsa komwe sunafike kwenikweni komanso kuupititsa patsogolo kumene sunamalizike. Pamene anthu abwera pamodzi nkupanga boma kapena ulamuliro uliwonse pa iwo eni, amafuna: kuteteza ndi kupititsa patsogolo ufulu wawo osati kuwuikira malire.

Nthawi zambiri, maboma ambiri samakhazikitsidwa motere. Amakidwa pa anthu ndi magulu omwe akonzeka kugwiritsa ntchito mphamvu pokwaniritsa zofuna zawo, osati kufikitsa ufuluwu kwa aliyense. Kuwononga kotereku kumachitika mololezedwa ndi anthu ambiri, omwensho mapeto ake amapindula popondereza anthu omwe ali ochepa. Koma ufulu siutengera kuchuluka kwa anthu: kuti ukhale ndi tanthauzo, ukuyenera kugwira ntchito mofanana kwa anthu onse.

Ngakhale maboma omwe amaika pamtima zofuna za anthu nthawi zambiri amachepetsa ufulu chifukwa chakuti samvetsetsa kapena kulemekeza mfundo yosapwetekana, kapena saona choipa chomwe chimadza kaamba ka kulowerera kwawo. Nthambi zaboma zoletsa zaupandu, mwachitsanzo, zitha kuletsa maganizo ena ndi mawu ena kapena zithunzi zina zokamba kapena kuulutsa, zomwe akuona kuti zitha kulakwira anthu. Pakutero, amapweteka alembi aluso, oimba, ansangulutso, atolankhani ndi ena pakuchepetsa ufulu wawo wa kaganizidwe ndi kulankhula, kuwononga tsogolo lawo ndi kuwamana phindu la thukuta lawo, upangiri komanso nzeru zawo. Ndipo pamene mfundo yaboma yopereka ziletso yavomerezedwa, kumakhala kophweka kwa womwe ali olamulira kuiwonjezera – kuletsa chilichonse chodzudzula boma lawo kapena kuletsa ganizo lililonse lomwe likuwapatsa chiopsezo.

Komanso, ulamuliro weniweni umaika misonkho pofuna kufananitsa zomwe anthu amapeza, osayang'anirako m'mene izi zingachotsere ufulu wa anthu opereka msonkho kusangalalira katundu wawo monga mmene kuba kwenikweni kumakhalira. Monga umbava, chio-psezo chakutenga zaeni motero, kumalepheretsa anthu kuti

Maziko a dziko la ufulu

asamasunge ndalama komanso kupangira chinthu chodzawathandiza mtsogolo– zomwe mapeto ake zingawononge chitetezo komanso chitukuko cha dziko lonse.

Maboma oterewa atha kunena kuti akupanga izi mokomera anthu, koma ndi ndani yemwe akuyenera kudziwa chokomera anthu? Anthu osiyanasiyana amakhalanso ndi zokhumba zosiyana komanso zopikisana. Kufananitsa zokhumba zopikisana choncho nkosatheka. Koma munthu payekha ali pabwino kudziwa, komanso kuchita, zokhumba zake kusiyana ndi adindo omwe amakhala kutali nagwiritsa mphamvu zawo kuwachitira anthuwo.

Kuumirizana ndi koipa. Ngakhale kuumiriza kwina – monga kuletsa munthu woopseza – kukhoza kukhala choipa chovomerezeka, tiyenera kuyesetsa kuchepetsa kukakamizana. Ambiri omenyera ufulu amati anthu onse ali ndi ‘ufulu wachibadwidwe’ – monga ufulu wokhala ndi moyo ndi ufulu okhala ndi katundu wamunthu payekha –omwe amapereka malire mphamvu zaboma paife. Sitingalole nzika zina kutibera kapena kutiikira malire ife, ndiye tingalole bwanji boma kutero?

Mu mbiri zambiri za anthu, zikusonyeza kuti anthu sanakhalepo a ufulu. Maboma sanakhazikitsidwepo ndi anthu mwakufuna kwawo koma kukakamizidwa ndiwomwe akufuna kugwiritsa ntchito mphamvu. Koma palibe munthu yemwe akutsogoleredwa mokakamiza adindo ndi munthu wokwanira mokwanira. Anthu ndiwokwanira pachikhalidwe ngati akupanga zisankho mwa iwo okha. Amakhala wosakwanira ngati ena akuwapangira zisankho. Choncho pamenepo ali ngati chinthu chosafunikira, osati anthu enieni.

Nkhani ya ufulu pamakhalidwe

Ufulu umalola anthu kukhala anthu enieni pogwiritsa ntchito luso ndi kuthekera kwawo mmene akuonera – osangoti mokomera iwo okha koma mokomeranso mabanja awo ndi ena omwe alinawo pafupi. Dziko la ufulu si gulu la anthu lokhala paokha komanso lodzikonda; koma ndi kulumikizana kwa anthu onse akudera momwe

Maziko a dziko la ufulu

akukhala. Kuthekera kwake kothandiza mtundu wonse wa anthu ndiye chithimethime cha khalidwe la dziko la ufulu.

Maziko a uzimu ndi a khalidwe la mtendere

Monga Katswiri pa zachuma Amartya Sen ananenera, ufulu ndi ganizo la dziko lonse. ¹Maziko a ufulu ali pafupifupi mu zipembedzo zonse, kuchokera ku chisilamu mpaka chipembedzo chachibuda, kuchokera ku mayiko aku Asia mpaka Kunzambwe. Mfumu Yayikulu yaku India Ashoka ankalingikitsa ufulu ndi kulolerana pandale zaka zikwi ziwiri zapitazo. Mfumu yayikulu Akbar yaku Mughul yomwe inalamulira mzaka zam'ma 1600 inaunikirapo za kulolerana pamene khoti loweruza zachipembedzo linali kuzunza akhristu omwe ankatsutsana nawo pachipembezo ku Ulaya. Chipembedzo cha Chisilamu, kuchokera kumayambiriro, chakhala chili ndi ufulu pa nkhani zachuma ndi kuchita malonda ngakhale zimenezi zinali zisanavomerezeke kumayiko akunzambwe. Mafumu aku Turkey anali ololera kwambiri kusiyana ndi mafumu aku Ulaya.

Mmawu ena tikhoza kunena kuti, Ufulu, umagwirizana ndi zikhalidwe komanso zipembedzo zikuluzikulu za padziko lapansi. Sikuti langokhala ganizo lochokera ku mayiko a azungu, kapena longofuna zinthu, kapena lotsutsana ndi dziko lodalira zikhulupiriro zawo zamphamvu. Kunena zoon, dziko la ufulu limadalira anthu kuvomereza mwakufuna kwawo malamulo ndi makhalidwe amene mdera lawo omwe akuletsa kupwetekana, kuberana, kuzunzana kapena kugwiritsa ntchito ulamuliro molakwika - malamulo opangitsa anthu kumakhala mwabata posatengera kusiyana kwawo ndi kumachitira zinthu pamodzi. Mkati mwa dongosolo lalikulu limeneli, ufulu umalola anthu kusankha zikhulupiriro zawo, kupitiriza kutsatira chikhalidwe ndi chipembedzo chawo. Sakukakamizidwa kutsatira zikhulupiriro, zikhalidwe kapena zochita za ena mwa atsogoleri adziko.

¹ Amartya Sen, 'Universal truths: human rights and the Westernizing illusion', Harvard International Review, 20(3), 1998, pp. 40-43.

Chikhalidwe cha kukhulupirira ndi mgwirizano

Dziko la ufulu silidalira mphamvu kapena ulamuliro, koma limadalira chikhulupiriro ndi mgwirizano. Chuma m'dziko la ufulu chimabwera ngati pali kusinthana mosakakamizika, kudzera mu kupanga katundu ofunikira ndi kuchita naye malonda ndi ena. Chuma sichibwera chifukwa cha mchitidwe wosolola ndi kulanda wochokera kwa atsogoleri, kugwiritsa ntchito mphamvu zawo pokhwathula misonkho ya anthu, kudzipatsa mphamvu mu zambiri ndi mwayi iwo eni, abale awo komanso anzawo. Umu ndim'mene chuma chambiri chapangidwira mu mbiri ya anthu – pochita zinthu modzikonda nagwiritsa ntchito mphamvu mokakamiza. Mmaloko mwake dziko la ufulu limadalira zolinga zabwino za kugwirizana ndi kusinthana kosakakamiza.

Kugwira ntchito, mgwirizano ndi kusinthana mosakakamiza kumadalira chikhulupiriro. Palibe munthu yemwe angachite malonda ndi anthu omwe akuwaganizira kuti ndiwomira – pokhapokha ngati awumirizidwa kapena palibiretu njira ina (mwachitsanzo pamene zinthu zopangidwa zili mmanja mwa boma kapena ogwirizana nalo). Mu dziko la ufulu, anthu amasankha ndipo amaloledwa kutengera malonda awo kulikonse – choncho opanga katundu akuyenera kusonyeza kwa ogula – omwe alipo komanso omwe angagule katundu wawo mtsogolo – kuti ndiwokhulupirika. Akuyenera kukwaniritsa malonjezano awo, apo ayi aziwonongera mbiri yawo zomwe zidzapangitsa kuti asamachite bwino pa malonda. Ndipo kwa anthu ambiri, kuwononga mbiri yabwino komanso njira yawo yopezera ndalama ndi chinthu chodetsa nkhwambiri.

Dziko la ufulu sililamuliridwa ndi atsogoleri pogwiritsa ntchito mphamvu. Limagwira ntchito mwachizolowezi ndi moonekeratu podzera muzochita za anthu mwakufuna kwawo – motsogozedwa ndi khalidwe lodalirana komanso kukhulupirika. Malamulo ndi ndondomeko zovomerezeka zimene zimalimbikitsa mgwirizano wosakakamizikawu zimangokhazikika zokha m'dziko la ufulu kotero anthu sachitanso kufunsa za izo. Sizifunikanso atsogoleri kuwauza

Maziko a dziko la ufulu

anthu kuti akhale okhulupirika komanso ochita bwino zinthu, kapena kulimbikira pa ntchito ndi kugwirizana ndi anthu ena. Anthu amachita izi mwachizolowezi tsiku ndi tsiku.

Kufunika kwa chikhulupiriro ndi mgwirizano m'dziko la ufulu kumapangitsa ubale pakati pa anthu ndi magulu kukhala ofunikira kwambiri kusiyana ndi m'madera omwe akugwiritsa ntchito mphamvu polamulira. Mgwirizano pa zikhulupiriro zauzimu, banja, ubwezi, mdera, mtundu, kuyandikana ndi magulu a anthu a zokhumba zofanana umakhala ofunikira. Maboma ambiri m'mayiko opanda ufulu amaona migwirizano yotero ngati chiopsezo pa ulamuliro wawo, ndipo amayesetsa kuyifooketsa, kuyilekanitsa ndi kuyithetsa. Nthawi zambiri angokwanitsa kuwapangitsa maguluwa kukhala am'chibisira. Gulu longodzipereka limakhala lofunikira kwambiri kwa anthu pakuti limakhala lamphamvu kwambiri kusiyana ndi ulemu woperekedwa kwa adindo aboma.

Zofuna zamunthu ndi malamulo

Dziko la ufulu silifuna ulamuliro ochokera kwa adindo. Limagwira ntchito kudzera mwa anthu wamba kusintha zikonzero ndi zochita zawo kukhala zikonzero ndi zochita za ena. Zomwe zimawapangitsa anthuwo kutero ndi malamulo ndi zikhulupiriro zomwe amazitsatira – monga kukhulupirika ndi kupewa ziwawa – zomwe zimalepheretsa mkangano pakati pa anthu osiyana okhalanso ndi zofuna zosiyana.

Malamulo okhazikikawa komanso zikhulupiriro zofananazi kumaposa kungolola anthu kukhala chabe ndi mtendere. Zimalola anthu kugwirizana pofuna kupititsa patsogolo zokhumba zawo. Mwachitsanzo, dziko la ufulu limalola anthu ake kuchita malonda wina ndi nzake mosaumirizidwa, nkukambirana mopindulira onse. Sizikutengera atsogoleri kusankha chomwe chingapindulire anthu, kapena kuganiza m'mene zokhumba zosiyana zingabwerere pamodzi mokomera onse, kapena kuganiza choyenera kupanga pokwaniritsa zokhumba zawo, kapena kukakamiza anthu ena kutsata chikonzero chawo. M'dziko la ufulu, anthu eni amasankha zokhumba zawo, ndipo amasankha njira yabwino yofikira zokhumba zawo pogwirizana ndi anthu ena. Amaloledwa kulowa mu mgwirizano uliwonse

pokhapokha ngati wina sapwetekeka popanga izi.

Anthu ena odzudzula sangaone m'mene dziko lingayendere ndi kutukuka ngati silisankha zolinga zofanana ndikulamula nzika zake kukwaniritsa zimenezi. Amaopa kuti dziko la ufulu likhoza kukhala chimpwirikiti cha zokhumba za anthu paokha zomwenso zili zokhazikika komanso zosapindulitsa – zomwe zikuyenera kuponderezedwa kuti zofuna za anthu onse zionekere.

Uku ndi kulakwitsa. Dziko la ufulu limavomereza kuti anthu amadzikonda. Komanso limavomereza kuti kudzikondaku ndi chilimbikitso champhamvu ndipo sikungaponderezedwe mosavuta. Anthu amaona ngati zokhumba za gulu – monga m'mene adindo ndi andale amanthauzira – kuti ndi zosafunikira kwenikweni kusiyana ndi zofuna zawo. Tikuyenera kukumbukira kuti kudzikonda ndikwabwino komanso kofunikira: ngati munthu salabadira zokhumba zake m'moyo (monga chakudya, madzi, pokhala ndi zovala), sangakhallitse, posatengera kuti gulu lawo ndi lachifundo chochuluka bwanji.

Dziko la ufulu limalondolera zokhumba za munthu payekha kunjira yopindulitsa. Silimangoondereza mu chiyembekezo chabe chokhala ndi dziko lina labwino. Malamulo amangoikidwa pofuna kuti anthu asakakamize zofuna zawo pa ena. Anthu ali ndi ufulu kupititsa patso-golo zokhumba zawo, paokha kapena mogwirizana ndi ena, pokhapokha ngati akulemekeza ufulu wa enawo kuti akhoza kuchitanso chimodzimodzi. Sangawakakamize ena kuvomereza ndi kutsata zolinga za ena.

Nkhawa ya odzudzula kuti dziko la ufulu lingadzitse mpungwe-pungwe wosatha pa zokhumba za anthu ikugonjetsedwa ndi chifukwa chodziwikiratu chakuti mayiko a ufulu ndiwomwe amatukuka – ndipo pafupifupi nthawi zonse amatukuka kwambiri kuposa omwe alibe ufulu. Pogwiritsa ntchito malamulo osavuta omwe amathandiza anthu kulemekeza ufulu wa ena, amapangitsa kudzikonda kwawo kukathera ku migwirizano yofunikira ndi kuchitira zinthu limodzi.

Mantha akuti anthu m'dziko la ufulu akhoza kumangoganiza zongokwaniritsa zolinga zawo zokha ndiolakwikanso. Anthu analengedwa

Maziko a dziko la ufulu

kuti azikhala pamodzi ndi anzawo. Pachibadwidwe chawo amalumikizana ndi banja, anzawo komanso anthu okhala nawo moyandikana, omwe amawaganizira pa zochita zawo. Amafunitsitsa ulemu komanso mafuno abwino kuchokera kwa anzawo komanso mbiri yokhala munthu wabwino. Amalolera kuti zofuna zawo zisapite patsogolo pofuna kuti ubale ndi ena upitirire. Kaamba koganizira ena, iwo amapindula pakuti anzawowo amakhalanso okonzeka kuwathandiza zikawathina.

Izi zimachitika kwambiri m'mayiko a ufulu. Kuthandiza ena, ngakhale alendo osawadziwa, magulu othandiza omwe siaboma ndikochuluka m'mayiko a ufulu kuposa omwe alibe ufulu weniweni – osati chifukwa anthuwo ndiachuma kwambiri, koma chifukwa chakuti mayiko a ufulu amatsindika pa kuchita zinthu mongodzipereka, osati kuka-kamizidwa kutero ndi dziko.

Mgwirizano kudzera mu chimvano cha malamulo.

Pofuna kugwirizana bwino ndi ena, tikuyenera kupanga zochita zathu kukhala zodalirika komanso zotsatira zake zodziwika. Mgwirizano siungatheke ngati anthu akusinthasinthu maganizo awo, kuchita zinthu mwakufuna kwawo, kapena kuphwanya malonjezo awo. Dziko la ufulu limalola anthu kuchita monga akufunira m'moyo wawo, pokhapokha ngati ena sakupwetekeka. Komanso limalimbikitsa khalidwe lokhazikika lomwe ndilofunikira mu mgwirizano wa anthu.

Mwachitsanzo, dziko la ufulu lili ndi malamulo okhudza umwini, kuyang'anira, ndi kusinthana kwa chuma. Izi zimalola anthu kukhala ndi katundu ndikuika ndalama zawo mu katundu yemwe angadzagwiritse ntchito mtsogolo – monga nyumba, mafakitale, ndi zipangizo zomwe zingathandize kutukula miyoyo yawo komanso kuphweketsa njira yopangira zinthu mosavuta komanso motsika mtengo – mosaopa kuberedwa kapena kuponderezedwa ndi anthu ena kapena adindo. Malamulo amenewa (a ufulu pa katundu) sanakonzedwe ndi boma, koma akhala akupita patsogolo mukupita kwa zaka. Malire awo ayesedwa kudzera mu milandu yosawerengeka imene yakambidwa m'makhothi ochuluka, kupanga malamulo omwe akupangitsa anthu kukhala otetezeka pa zochita zawo ndi ena – ndinso kupangitsa

mgwirizano kukhala wosavuta komanso opindulitsa.

Mayiko ambiri a ufulu afikanso povomereza malamulo ena kukhala ofunikira kuti pakhale mgwirizano wa mtendere pakati pa anthu. Malamulo amakhalidwe amaika malire omwe amapangitsa kulumikizana kwa anthu pochita zinthu kukhala kosavuta kwa aliyense. Ndipo pali mlingo wamakhalidwe ovomerezeka pakati pa anthu – mchitidwe, ulemu, ndi ndondomeko zochitira malonda abwino – omwe umakula popita nthawi m'mene anthu akuchitira zinthu limodzi. Mchitidwe opindulitsawu, womwe umapezeka kwambiri m'mayiko a ufulu, ndipo maboma opanda ufulu sangaukwaniitse.

Nzika za m'dziko la ufulu zilinso ndi ufulu wapachiweniweni. Ufuluwu utha kukhala wosiyana pena, koma zina mwa zovomerezeka ndi ufulu osakamizidwa kugwira ntchito kapena ukapolo, ufulu ku nkhanza kapena chilango chosayenera wina akalakwa. Izi zikuphatikizapo ufulu wa chikumbumtima ndi chikhulupiriro – ufulu wokhala ndi maganizo ako pa chipembedzo kapena ndale, ufulu ochita zomwe chipembedzo chako chikufuna, ndi kutenga mbali pandale opanda kuopsezidwa kapena kuchititsidwa mantha. Zikuphatikizanso ufulu oyankhula – ufulu wodzifotokoza wekha komanso ufulu wanyumba zoulusira mawu (wailesi, wailesi ya kanena, nyuzipepala, ndi masamba a intanenti) kuulusa nkhani kapena kupereka ndemanga mmene afunira. Zikuphatikizanso ufulu okumana pamodzi komanso kupanga ubale ndi yemwe ukufuna. Ndiponso zikuphatikiza chinsinsi – osazemberedwa kapena kuyang'aniridwa ndi ena, makamaka adindo. Mwachidule, dziko la ufulu limayembekezera nzika kulolera maganizo aena, zikhulupiriro, dongosolo la moyo wa ena, ndi zochita ndiponso kusalowerera, potsatira lamulo lakusapwetekana.

Chilungamo ndi mphamvu ya lamulo

Dziko la ufulu limakhalanso ndi malamulo achilungamo. Izi ndi zilango kaamba kopweteka wina, osangoti thupi chabe komanso chinyengo ndi zina. Mwina tinganene kuti, mdziko la ufulu, chofunikira kwambiri ndi mphamvu ya lamulo. Vuto lalikulu la magulu andale si kasankhidwe ka atsogoleri ake – izi nzosavuta – koma kuchepetsa

Maziko a dziko la ufulu

mphamvu zawo. M'dziko la ufulu, udindo ndi mphamvu ya adindo m'boma zimapatsidwa malire. Izi zimaonetsetsa kuti mphamvu zomwe apatsidwa kuti ateteze nzika ku ukali ndi kupereka chilango kwa olakwa sizikugwiritsidwa ntchito molakwika kapena mwakufuna kwa iwo amene azipeza.

Mayiko a ufulu anapanga njira zosiyanasiyana – monga malamulo oyendetsera zisankho, malamulo a dziko komanso kulekanitsa mphamvu – ndi cholinga chofuna kuika malire a mphamvu za adindo. Koma njira yabwino yotetezera nzika ku nkhanza kuchokera kwa owalamulira ndiyokuti malamulo azigwira ntchito pa aliyense mofanana. Iyi ndiyomwe imadziwika kuti mphamvu ya lamulo. Pa mfundoyi, boma silingakondere kapena kupereka mwayi ku mitundu ya anthu ena, mwachitsanzo, kapena kulola gulu lina la anthu kuti lisamapereke msonkho. Ndipo malamulowa ayenera kugwira ntchito mofanana pa boma ngakhale pa anthu onse.

Izinso zimakhudza mmene malamulowo akugwirira ntchito. Kuti mphamvu za akhothi zigwire ntchito mosakondera komanso mosa-khala mwakaphulira, malamulo a chilungamo ayenera kugwira ntchito pa aliyense m'dziko mofanana. Nzika ziyenera kuthandizidwa mofanana komanso dongosolo lonse la chilungamo litsatidwe. Izi zikuphatizika osamangidwa mwachisawawa, osamangidwa opanda kuzengedwa mlandu, kuzengedwa mlandu moyenera ndi kupereka mpata ngati pali mboni, chigamulo kupangidwa ndi oweruza ovome-rezeka ndi anthu osati adindo osankhidwa, komanso osazengedwa kwambiri mlandu umodzi.

Zotsatira za kuika malire konseku pa andale, adindo, ndi oweruza milandu kuletsa kugwiritsa ntchito mphamvu molakwika, kuchotsa mchitidwe opereka mwayi wapadera kwa ena ndi kuchepetsa zoipa za kukakamizana. Choyenera kudziwa nchakuti, boma mu dziko la ufulu lili ndi udindo woteteza ndi kupititsa patsogolo ufulu wa anthu, osati kuuchepetsa.

Nkhani ya ufulu pa chuma

Kukwera mtengo kwa zinthu kwakukulu

Kufikira m'zaka zam'ma 1750, umoyo wamunthu unali usanasinthe kwenikweni. Pafupifupi aliyense ankagwira ntchito pa nthaka, kuchita ulimi wa zakudya umene unali wokhetsa thukuta komanso wosadzi-wikiratu. Njira zaulimi munthawiyi zinali zofanana ndi zomwe zinkagwiritsidwa ntchito munthawi ya ulamuliro wa Farao. Anthu ambiri analibe ndalama yogulira zowasangalatsa ngati zovala zina zapadera. Ochepa ankakwanitsa kugula nyama. Ochepa omwe anali olemera kwambiri anali okhawa omwe anabadwira mabanja achuma kale. Ndipo nthawi zambiri, chumachi chinkachokera mu mphamvu yokhazikitsa misonkho pa alimi mopindulira iwe mwini – kapena pokhala wantchito kapena mnzake wa munthu yemwe anali nazo mphamvuzo.

Kwa anthu ambiri, uku kunali kukhala mozunzika kwambiri. Mu chaka cha 1800, katswiri wina pa kayendetsedwe ka chuma wotchedwa Deirdre McCloskey anawerengetsera, mlingo wamalipiro amunthu padziko lapansi omwe unali pakati pa \$1 ndi \$5 pa tsiku – yomwe ndiyosakwana kugulira kapu ya khofi m'mizinda ikuluikulu padziko lapansi lero. ²Pano, mlingo wamalipiro amunthu ukufikira \$50 pa tsiku. Uku ndi kukwera kwambiri pachitukuko.

Koma uwu ndi mlingo wapakatikati chabe, zimene zikubisa kutukuka kumene mayiko ena – ngakhale siwonse – akwanitsa. Mlingo wa malipiro mu dziko la Tajikistan, limodzi mwa mayiko omwe kulibe ufulu, siudutsa kwambiri \$7 pa tsiku. Koma mlingo wa malipiro mdziko la United States, limodzi mwa mayiko a ufulu, pano apotsa \$100 pa tsiku. Izi zadza kaamba ka ufulu. Anthu am'dziko la Amerika lero ndiachuma koposa khumi ndi zinayi kusiyana ndi anthu m'dziko la Tajikistan, ndipo ndiachuma pakati pa makumi awiri ndi zana kuposa m'mene analili makolo awo mu zaka za mma 1800. Mayiko

² Deirdre N. McCloskey, 'Liberty and dignity explain the modern world', in Tom G. Palmer (ed.), *The Morality of Capitalism*, Students for Liberty and Atlas Foundation, Arlington, VA, 2011.

Maziko a dziko la ufulu

a Switzerland, Australia, ndi United Kingdom omwe ali pa mndandanda wa maiko omwe ali ndi ufulu kwambiri potengera lipoti la bungwe lapadziko lonse loona za ufulu pa chuma –mlingo wa chuma pa munthu umaposa \$90 pa tsiku. Ufulu ndi chitukuko zimayendera limodzi³.

Sizachilendo, kuti anthu akuthawa m'mayiko osauka komanso opanda ufulu kupita m'mayiko ochita bwino koma a ufulu. Chaka chilichonse, mayiko makumi awiri omwe alibe ufulu weniweni amakhala ndi anthu pafupifupi 1.12 pa anthu chikwi aliwonse otuluka m'dziko kusiyana ndi olova. Mosemphana, mayiko makumi awiri a ufulu amakhala ndi chiwerengero cha anthu pafupifupi 3.81 pa anthu chikwi aliwonse olova m'mayiko awo kusiyana ndi otuluka.⁴Maiko amene ali ndi ufulu kwambiri pa zachumawo mwa mayiko makumi awiriwa amakhala ndi anthu ochulukira kwambiri obwera m'dziko lawo. Mwachidule, mayiko omwe ali pansu pa mndandanda wa mayiko a ufulu akutaya chiwerengero cha anthu, pomwe mayiko omwe ali pamwamba akuwonjezera chiwerengero.

Mwa njira ina, anthu akusankha ufulu wawo ndi mapazi awo. Ndipo akuchita izi ngakhale mayiko opanda ufulu akuletsa kutuluka kwa anthu komanso mayiko a ufuluwa akuyesetsa kuletsa anthu kulowa mdziko lawo.

Ufulu ndi kupereka mwachifundo

Maiko a ufulu amachita bwino osati pa kuzunza osauka omwe ali nawo. Monga anaonera katswiri wa kaganizidwe kozama pa makhalidwe a anthu wa mdziko la Russia, Leonid Nikonov, gawo lapakatikati lachuma cha dziko lonse omwe umapita kwa anthu osaukitsitsa khumi pa zana lililonse m'mayiko a ufulu komanso opanda ufulu ndiwofanana (2.58 pa zana komanso 2.47 pa zana motsatana). Komabe nkwabwino kwambiri kukhala osauka m'dziko lolemera

³ Fraser Institute, Economic Freedom of the World 2012 Annual Report, FraserInstitute, Vancouver, BC, 2012.

⁴Gabriel Openshaw, 'Free markets and social welfare', Mises Daily, 4 October 2005, http://www.mises.org/daily/1915#_edn2.

Maziko a dziko la ufulu

(komwe osauka amalandira mlingo wa \$23 pa tsiku) kusiyana ndi kukhala osauka m'dziko losauka (komwe osauka amalandira mlingo wa \$2.50 pa tsiku)⁵

Chuma m'mayiko a ufulu komanso olemera chimakhala chofikirika ndi anthu. Nzika zawo zosaukitsitsa sizili zolephereratu kukhala ndi chuma – kusiyana ndi mayiko omwe ufulu ndiwochepa komwe zimatengera banja lomwe wachokera, gulu la anthu omwe uli, mtundu kapena chipembedzo, kapena chipani cha ndale. M'mayiko a ufulu mumakhala kuyenderana kwambiri pakati pa anthu. Munthu wolemera kwambiri padziko lonse, yemwe anayambitsa kampani ya Microsoft, Bill Gates, anayambira kampani yake mu garaja.

Ndipo pano, Gates akufuna kudzapereka chuma chake chonse ku ntchito yachifundo. Izi nzosadabwitsa: ntchito zachifundo kwa magulu omwe siaboma ndi zambiri m'mayiko olemera. Kafukufuku wa bungwe la Barclays Wealth linapeza kuti anthu awiri pa anthu asanu aliwonse olemera kwambiri m'dziko la Amerika amati kupereka zachifundo ndi chimodzi mwa zitatu za zinthu zawo zofunikira pogwiritsa ntchito chuma chawo⁶.

Malingana ndi bungwe laku UK la Charities Aid Foundation, mayiko asanu omwe anthu ake ndiwothekera kupereka chuma chawo ku ntchito yachifundo ndi Australia, Ierland, Canada, New Zealand, ndi United States – onsewa ali pamwamba mu mndandanda wa mayiko a ufulu. ⁷Ndipo mayikowa ali ndi chuma chambiri chogawa kusiyana ndi nzika za m'mayiko osauka, opanda ufulu.

Ufulu umathetsa tsankho

M'mayiko opanda ufulu mchitidwe wa tsankho ndiwaukulu. Kukhoza kukhala kovuta kupeza ntchito yabwino, kapena kupeza chithandizo

⁵ Leonid Nikonov, 'The moral logic of equality and inequality in market society', in Tom G. Palmer (ed.), *The Morality of Capitalism*, Students for Liberty and Atlas Foundation, Arlington, VA, 2011.

⁶ Barclays Wealth, *Global Giving: The Culture of Philanthropy*, London, 2010.

⁷ Charities Aid Foundation, *World Giving Index 2012*, Charities Aid Foundation, West Malling, 2012.

Maziko a dziko la ufulu

chabwino, ngati suukuchokera ku gulu, chipembedzo, chibadwa kapena banja loyenera. Koma maboma omwe amapereka ufulu pamalonda amachotsa tsankholi. Opanga zinthu m'mayiko a ufulu sangakwanitse tsankho posankha ochita naye malonda kapena omulemba ntchito⁸.

Mwachitsanzo, Olemba ntchito akhoza kudana ndi anthu obwera, makamaka ngati akuchokera ku mtundu wina wa anthu, chikhalidwe kapena chipembedzo china. Koma anthu obwera akhoza— ndipo amatero nthawi zambiri – kuvomereza malipiro ochepa pa ntchito yomweyo. Apa, olemba ntchito omwe amasankha kulemba nzika za dziko zokhazokha amadziika okha pa chiphinjo. Ndalama zolipira ogwira ntchito kwa iwo zimakhala zochuluka kusiyana ndi omwe amalemba ntchito nzika za mayiko ena. Phindu lawo lidzakhala lochepa, apo ayi ayenera kukweza mtengo wa katundu wawo ndipo malonda awo adzalowa pansu. Izi sizabwino pa malonda. Koterokwabwino pa nkhani za chuma kuti olemba ntchito akhale ndi tsankho.

Funso: Kodi mayiko a ufulu siwokonda zinthu chabe?

Ayi. Ufulu pa zachuma umawapatsa anthu chisankho komanso mwayi wambiri. Umawapatsa zofunikira zenizeni pa moyo wawo – chakudya, pokhala ndi zovala – zabwino. Ndipo umawapatsa anthu mwayi omwe sankauyembekezera ufulu pa malonda komanso misika usanakule. M'malo mozunza anthu kuwagwiritsa ntchito zowawa ndi zosayenera moyo wawo onse, umawalola anthu kusangalala ndi zinthu zomwe amazitenga zapamwamba monga kuyendayenda, nyimbo, luso, chikhalidwe ndi zochitika zosiyanasiyana m'dera. Umawapatsa kuthekera kokwanitsa kukhala ndi zipatala komanso sukulu zabwino.

Chuma ndi chida chabe chomwe chimatipatsa kuthekera kofikira zomwe timazikhulupirira – osangoti katundu wabwino yekha, komanso zomwe timazona zofunikira pa chikhalidwe

⁸ For a gowod outline of this point, see Milton Friedman and Rose Friedman, *Capitalism and Freedom*, University of Chicago Press, Chicago, IL, 1962.

komanso pagulu. Ichi nchifukwa chake mayiko olemera, a ufulu kwambiri ali ndi mabwalo ambiri azamasewero, nyumba zikuluzikulu zopangiramo zionetsero, nsangulutso, sukulu zaukachenje, malo osungiramo mabuku komanso malo osungiramo zinthu zamakedzana.

Ngakhale kwa ogwira ntchito mdziko, mayiko a ufulu pantchito za malonda anadana ndi tsankho. Mwachitsanzo, patha kukhala kusa-gwirizana kuti akazi azipita kukagwira ntchito potengera chikhali-dwe, kupangitsa kukhala kovuta kuti mkazi apeze ntchito. Koma olemba ntchito atsankho ndi akazi atha kukhala ndi aluso ochepa oti awalembe ntchito kusiyana ndi anzawo omwe alibe tsankholi. Chitsanzo china chabwino ndi kugawanikana komwe kulipo ku India. Kupita patsogolo kwa tekinoloje mumafakitale m'madera ngati Hyderabad kwachulutsa mwayi wa anthu ogwira ntchito omwe ndi-wosalidwa mdzikolo. Olemba ntchito mu bizinesi ya mpikisanoyi amafuna anthu oganiza mwaluso. Sangachite tsankho potengera ndi gulu lomwe munthu akuchokera kapena mtundu wake. Zomwe malamulo othetsa tsankho akanika kuchita mu zaka makumi ambiri zapitazi, kudzikonda kwa anthu ochita malonda mwa ufulu zikukwaniritsidwa m'zaka zochepa.

Luso lopanga zinthu la anthu a ufulu

Chifukwa china chomwe mayiko a ufulu atukukira nchakuti amagwiritsa ntchito luso lonse lomwe lilipo. Nzika za mayiko a ufulu ndizomasuka kugwiritsa ntchito maganizo awo ndi kuthekera kwawo kugwira ntchito ndi tsankho lochepa lomwe lingawalepheretse. Ngati angapange, kuwonjezera ukadaulo ndi kupereka katundu yemwe angatukule miyoyo ya anthu ena, anthuwo awathokoza powagula katundu wawo. Choncho mayiko a ufulu amapanga zinthu komanso mwaukadaulo, ndipo pakutero amatukuka mwachangu.

Ufulu pa chuma umalondolera zofuna za anthu kuti zipindulire anthu ambiri. Umapeza ndalama popanga zomwe anthu ena akufuna ndipo ali wokonzeka kukulipira. Ndipo umafuna kuti abwererense kudzagula zambiri ndi kukawauza anzawo za ubwino wa katundu wako.

Maziko a dziko la ufulu

Opanga katundu amaika chidwi chawo pa ogula osati iwo eni. Ochita malonda odziwika ambiri m'mayiko a ufulu amati anakwanitsa kuchita bwino pa bizinezi zawo poika chidwi chawo pa zofuna ndi zoyenera za makasitomala awo osati pofuna kupeza phindu lambiri paiwo.

Chilungamo ichi chili kutalitali ndi chithunzithunzi cholakwika cha 'mkhalidwe wa kuchita chilichonse kuti zikuyendere ngakhale utapweteka anzako' m'mayiko a ufulu pa malonda. Dziko la ufulu weniweni pa malonda ndi dongosolo lalikulu la mgwirizano, posadalira kukakamizana koma kuchita malonda mwaufulu ndi kusinthana pakati pa anthu a ufulu.

Kupanga mpamba

Maiko a ufulu pamalonda amalemera pokhazikitsa mpamba wopindulitsa, ngakhaleenso kulimbikitsa luso lopanga zinthu ndi kusamalira makasitomala. Nzophweka kugwira nsomba ndi ukonde kusiyana ndi dzanja, koma izi zikutanthauza kugwira nsomba zochepe kwa kanthawi pomwe uli mkati mopanga ukonde. Posalabadira phindu lopezeka msanga, umatha kukonza mpamba, ndikupanga ntchito yokonza zinthu mtsogolo idzakhale yosavuta.

Awa nde maziko opereka mphamvu kwa anthu kuti aziyang'anira ntchito zamalonda. Anthu amakonza mpamba, monga kukhala ndi nyumba, mafakitale, ndi makina, omwe amathandizira moyo wawo kukhala wosavuta ndi ntchito yawo kukhala yopindulitsa (nthawi zambiri zimapindulitsa mochuluka: taganizirani kusiyana kolima munda pogwiritsa ntchito mathirekitale kusiyana ndi makasu). Ndipo mapangidwe ake ndiwochulutsa zinthu: kuwonjezera kapena kupititsa patsogolo kwa zida za tekinoloje zogwiritsa ntchito kumawonjezera phindu ndi kuchepetsa kwambiri ntchito.

Dziko la ufulu litha kuchulutsa mpamba wopindulitsawu ndi kupitiriza kuwonjezera phindu lake ndi kuchita bwino kwake pokhapokha ngati likupereka kuthekera kwa nzika zake kukhala ndi nyumba, mafakitale, makina ndi katundu wina wodzetsa chuma popanda

Maziko a dziko la ufulu

kuopa kuti angalandidwe kapena kuberedwa. Limateteza anthu ake kuti asalandidwe katundu ndipo lili ndi malamulo okhudza umwini wa katundu omwe amapangitsa umbava kukhala ochepa.

Kuteteza umwini wakatundu kotereku, kudzera m'malamulo ndi chikhalidwe, ndi chinthu chofunikira kwambiri m'dziko la ufulu komanso la ufulu pamalonda. Nchachidziwikire kuti alimi ochepa ndiwo angalole kutaya mphamvu zawo kukafesa mbewu, kubzala, kulima ndi kusamalira mbewu zawo ngati atadziwa kuti zokolola zawo zidzabedwa ndi mbava. Momwemonso, ndi anthu ochepa omwe angalole kugwira ntchito mopyola muyeso ngati malipiro awo ambiri angatengedwe kudzera mu msonkho. Mabanja sangasunge ndalama zawo ngati pangakhale chinyengo chilichonse kudzera mukutsika mphamvu kwa ndalama kwachinyengo. Anthu ochita malonda sangalole kuika ndalama zawo m'mabizinezi ngati katundu wawo angadzatengedwe nkukhala waboma popanda chipepeso. Mwayi womwe ungapangitse anthu achuma ochepa kupindula kwambiri m'misika kukhoza kupangitsa anthu ochepa kwambiri kuyambitsa mabizinezi atsopano.

Ngati anthu akuponderezedwa koposa ndi mbava kapena boma, zimapangitsa anthu kuti asalimbikire pa ntchito, asasunge chuma komanso asatukuke. Ibn Khaldun, katswiri wachisiramu pa zamaphunziro komanso zamalamulo mzaka za mma 1400, anamvetsetsa bwino mfundoyi. Analemba kuti:

Zikuyenera kudziwika kuti upandu pa katundu wa anthu umachotsa chilimbikitso chogula komanso kukhala ndi katundu. Anthu amakhala ndi kaganizidwe koti cholinga komanso mathero okhala ndi katundu ndiakuti adzalandidwe. Pamene khumbo lofuna ndi kukhala ndi katundu latha, anthu safunanso kukhala naye. Mlingo umene ufulu okhala ndi chuma waphwanyidwira umaperekeranso mlingo wa kuthekera kwa anthu kuti asakhalenso ndi katundu⁹.

⁹ Ibn Khaldun, Muqaddimah: An Introduction to History, 1377.

Maziko a dziko la ufulu

Katundu ndi chitukuko

Kukhala wotetezeka paumwini wa katundu wako kumakupatsa mphamvu pa tsogolo lako ndi la banja lako. Mwachitsanzo, ngati wakwanitsa kukhala ndi nyumba yako – zimene anthu m’mayiko ambiri sangakwanitse – moyo wako ndekuti uli ndi pokhala potetezeka. Komanso umakhala ndi katundu yemwe ungagwiritse ntchito kubwereka ndalama zoyambira bizinezi ndi kupanga mpamba wako zopezera chuma kusiyana ndi kungokhala kudalira chifundo cha anthu achuma mpaka kale. Zimakupatsa chodalira pa chuma zokupangitsa kuyesera zinthu zina zatsopano – monga kusiya ntchito ndi kukayang’ana ina, kapena kuika ndalama zoyambira bizinezi ina.

Umwini wotetezeka pa katundu umalimbikitsa ukadaulo ndi malonda, zomwe zimawonjezera phindu la munthu ndipo choncho kuwonjezera chuma cha anthu. Miyoyo yathu ikanakhala yosaukitsitsa tikanati timadzipangira chilichonse patokha – kulima chakudya chathu, kusaka madzi athu, kusaka mafuta athu, kupanga zovala zathu, kumanga nyumba zathu kapena kudziteteza tokha ku chiopsezo. Ochepa mwaife ndiomwe ali ndi luso lopanga zonsezi, ndipo tingafune zipangizo zokwanira kuti tizipange mosavuta komanso mokwanira. Koma ngati umwini pakatundu ulemekezedwa, sitingapange zonsezi paife tokha. Anthu atha kupanga zida zomwe angafune kuti agwirire ntchito moyenerera, ndi kugulitsa katundu kwa enafe. Mlimi atha kugula makasu ndi mathirekitale, m’misiri atha kugula makwerero ndi fosholo, opanga zobvala atha kukagula ulusi ndi makina osokera. Ndipo izi zitha kuwapangitsa kuzama pa luso la ntchito yawo, kukwanitsa kuyang’anira kapangidwe ka katundu wawo, mosiyana ndi momwe ena ongoyamba kumene angachitire. Kudzera mu kugawana kwa ntchito kotere tikhoza kukhala ndi katundu wapamwamba, otsika mtengo komanso miyoyo ya zinthu zambiri.

Komabe, zonsezi n’zotheka ngati anthu ali otetezeka mokwanira kukhala ndi mpamba odalirika ndi kuchita malonda, kukhulupirira kuti saberedwa kapena kunamizidwa. Njira ina ndiyovutirapo. Monga Ibn Khaldun akupitirizira kunena kuti: ‘pamene anthu

Maziko a dziko la ufulu

sakupanga malonda kuti apeze zosowejera mmoyo wawo, ndipo pamene asiya kuchita zinthu zowapindulitsa, mabizinezi achitukuko amatha, ndipo chilichonse chimawonongeka. Anthu amapita kuli-konse kuti akapeze zowathandiza mmoyo, malo otalikana ndi dziko lakwawo'. Izi nzomwe zikuchitika masiku ano pamene tikuona kusamuka kwa anthu kuchoka m'mayiko opanda ufulu kupita m'mayiko a ufulu.

Kupanga chuma mosapweteka ena.

Anthu ena amakhulupirira kuti katundu wamunthu amabwera pokhapokha wina apwetekedwe. Izi sichoncho. Dziko la ufulu pachuma limapanga chuma komanso kuwonjezera ubwino wa chuma chomwe chilipo kale.

Ubwino simaonekedwe a zinthu. Ndim'mene anthu amaganizira za zinthu. Ogulitsa amapereka katundu chifukwa amamuona osafunikira kusiyana ndi ndalama za makasitomala. Makasitomala amapereka ndalama chifukwa amaona katundu kukhala ofunika kusiyana ndi ndalama zomwe amagulirazo. Ngakhale ana asukulu amasinthana zoseweretsa, aliyense kuyamikira ubwino omwe akuupeza posinthana chinthu chomwe atopa nacho ndi chomwe akufuna. Msintho wawo wadzetsa ubwino. Palibe yemwe wapwetekedwa pamalonda oterewa: ndithudi, palibe akanalola kuti asinthane akanakhala kuti wina atenga chosakhala bwino.

Chimodzimodzi, ngati wina angalime ndi kubzala mbewu pomwe panalibe, ndipo anthu ali wokonzeka kugula zokololazo, akupanga ubwino watsopano pa chinthu chomwe chinali chosafunikira poyamba. Chuma chapangidwa, koma palibe yemwe waberedwa.

Komanso, ngati wazamalonda angamange fakitale yokonza nsapato, zovala kapena china chatsopano chomwe anthu angafune kugula – ndipo akupanga ndalama pochita izi – ndani waberedwa? Atha kupanga chuma, koma sanabere aliyense. Kumbali ina, apanga ndi kufalitsa ubwino wa chinthu chomwe kunalibe¹⁰.

¹⁰ point is well made by UK businessman Sir Ernest Benn in *Why Freedom Works*, Sir Ernest Benn Ltd, London, 1964..

Maziko a dziko la ufulu

Dziko la ufulu silopereka mphamvu zoyendetsera ntchito za malonda kwa anzawo a atsogoleri

Anthu ena amati mu ulamuliro wopereka mphamvu zoyendetsera ntchito za malonda kwa anthu oima paokha, zokhumba za anthu achuma zimapondereza osauka, ndipo andale amabera anthu popereka mwayi otheratu wa bizinezi, mwayi wapadera, kupereka ndi kutsitsira mitengo ya katundu kwa anzawo omwe ali ndi mabizinezi.

Koma m'dziko la ufulu weniweni, mpikisano umapangitsa kuponderezana kapena mchitidwe wopereka mphamvu zoyendetsera ntchito za malonda kwa anzawo a atsogoleri kukhala zosatheka. Mabizinezi kuti akhalepo amadalira makasitomala awo. Ngati sanga-pereke katundu wabwino makasitomala asiya kuwagula nkupita kwa ena. Ndipo nthawi zonse pamakhala ogulisa ena odikirira chifukwa m'mayiko a ufulu boma silikhala ndi mphamvu yopereka mwayi otheratu, kuteteza makampani ena kapena kuletsa anthu kuyamba mabizinezi atsopano. Dziko la ufulu weniweni pachuma limalola mpikisano, zomwe zimapereka mphamvu kwa ogula kuposa ogulitsa: makampani atha kugwa ngati sakupanga katundu wogwirizana ndi ndalama za ogula. Makampani ena akhoza kukula kwambiri – mwachitsanzo, mbali yopanga galimoto, yomwe imafuna ndalama zambiri pofuna kuiyamba. Koma amakhalabe pa mpikisano kuchokera kwa ena omwenso ali ndi kuthekera kopanga bizinezi yomweyo. Mavuto amabwera pamene adindo akuletsa mpikisano komanso kugwetsa mphwayi kapena kuletsa amabizinezi atsopano kuyambitsidwa.

Kunena zoono, nthawi zambiri mpikisano weniweni wopanda zopinga zilizonse umavuta kukhazikika. Ngakhale m'mayiko a ufulu masiku ano, andale amaika malamulo omwe – nthawi zambiri mosazindikira – amachepetsa mpikisano ndipo choncho amafoola mphamvu zomwe ogula alinazo pa ogulitsa. Ndipo ogulitsa ndi-womwe nthawi zambiri amapanga upo kuti izi zichitike. Mwachitsanzo, makampani okhazikika atha kukakamiza andale kukhazikitsa malamulo okhudza ubwino wakatundu komanso mlingo woyenerera

Maziko a dziko la ufulu

kufikiridwa popanga katundu, kufotokoza zomwe zikuyenera kupangidwa komanso njira yomwe zikuyenera kupangidwira. Akhoza kufotokoza kuti malamulowa ndiwofunikira kuti ateteze anthu ku katundu osakhala bwino. Koma zotsatira zenizeni ndi kuteteza mabizinezi awo kwa ogulitsa atsopano kapena aang'onoang'ono omwe angapange katundu wapamwamba mwa njira yaluso zomwe sizikupezeka pa mndandanda wa malamulo. Kapena mwinanso, andale atha kulowelerapo pogwiritsa ntchito ndalama zaboma kuti atukule ma kampani omwe akulowa pansi chifukwa chosowa ndalama kapena ali pa chiopsezo ndi makampani akunja, ponena kuti mpofunika kuteteza ntchito za nzika za dzikolo. Atha kuletsa kulowetsa katundu wakunja mdziko kuti ateteze makampani am'dzikolo. Izi zitha kuthandiza omwe akugwira ntchito mkampaniwo kwakanthawi kochepe – koma ndizolowa mthumba anthu komanso odula msonkho, omwe amakhala ndi chisankho chochepe, kugula katundu mokwera mtengo kusiyana ndi m'mene akanagulira pa katundu yemwe siwabwino.

Dziko likatalikirana ndi ufulu ndipo m'malo mwake kupereka mphamvu pachuma kwa adindo, limachulutsa kuthekera kwa andale ndi ogulitsa katundu kupondereza anthu pofuna kudzipindulira okha. Zizindikiro za mchitidwe wopereka mphamvu zoyendetsera ntchito za malonda kwa anzawo a atsogoleri zimapezeka paliponse, koma zimakula kwambiri m'mayiko a ufulu ochepa pachuma. Nthawi zambiri zimangotengedwa mwachizolowezi kuti omwe ali ndi udindo amazigwiritsa ntchito kudzilemeretsa iwo eni ndi mabanja awo ndi anzawo. Ndipo amaganiza ngati aoneka ofooka ngati sachita izi.

Koma m'mayiko a ufulu weniweni adindo saloledwa kugwiritsa ntchito mphamvu zawo zopatsidwa ndi malamulo kapena ndalama za misonkho kupereka mwayi wachuma kwa anzawo. Pali malamulo okhwima molingana ndi kugwiritsa ntchito mphamvu komanso m'mene ndalama zaboma ziyenera kugwirira ntchito. Ogulitsa katundu sangachite chinyengo ndi adindo kuti agule katundu motsika ndi kutetezedwa, chifukwa mphamvu zokondera moterozo palibe.

Maziko a dziko la ufulu

Kusowa kwa ufulu kumapereka mphamvu kwa makampani komanso andale kuti apondereze ena, osati mpikisano pa umwini wa ntchito zachuma.

Chipambano cha ufulu

Ngakhale kuti ufulu pachuma ndi malonda sizipezeka kotheratu, zakwanitsa kutukula anthu pafupifupi mabilyoni awiri ku umphawi wadzaoneni mu zaka makumi atatu zapitazo. Izi ndizomwe mayiko amphamvu komanso osapereka mphamvu kwa anthu monga Russia, China ndi mayiko ena akumwera chakum'mawa pa dziko lapansi akanika kukwaniritsa, ngakhale akhala akuyesera zaka zokwana theka la zana. Koma pamene zikhomo ndi ziletso pamalonda zakhala zikuchotsedwa, mayiko ambiri akhala akulowa nawo mu ndondomeko ya kachitidwe ka malonda padziko lonse lapansi ndipo chuma chafalikira. Chafalikira makamaka kwa anthu osaukitsitsa m'mayiko osaukitsitsa omwe avomereza ufulu watsopano wochita malonda ndi mayiko ena. Kodi pangakhaleenso mfundo ina yabwino ndi yopindulitsa padziko lapansi yoposa ya ufulu?

3 NSANAMIRA ZA DZIKO LA UFULU

Dziko lopanda boma

Ufulu ndi chikhalidwe

Mu dziko la ufulu, gawo lalikulu la miyoyo ya anthu limakhalidwa mopanda kuganizirako za boma. Iyi siili ngati nthabwala yaku India chabe yakuti: ‘Chuma chimakwera usiku – pamene boma likugona’. Koma izi zikutanthauza kuti boma silitengapo gawo konse mu zochitika zambiri zomwe zili zofunikira kwenikweni kwa anthu.

Anthu m’dziko la ufulu samakhala odzisankha kumachita zawozawo. M’ malo mwake, ndi anthu ochitira zinthu limodzi. Amafuna kukhala ndi anzawo, kulumikizana ndi kuchitira limodzi zinthu ndi ena munjira zambiri. Atha kukhala mamembala olimbikira mmagulu a zipembedzo. M’ makalabu ndi m’ magulu amakhala ndi anzawo omwe ali ndi zokonda zofanana ndi zawo, kaya ndi kuimba, kuwerenga, kuphika, kuwedza nsomba, kusewera ndi kuonera mpira kapena kutolera zinthu. Amacheza komanso kupanga magulu ndi ena ofanana nawo, kaya ndi achinyamata, achikulire, anzawo a kusukulu, makolo atso-pano kapena omwe ali ndi ulumali ofanana ndi wawo. Atha kukhala ndi malo ophikira nsuzi kapena kumayendetsa malo ogona anthu osowa ndi opanda kwawo. Ili limatchedwa gulu lapachiweniweni.

Pambali pa ufulu wochita zinthu komanso mayendedwe omwe anthu a m’ mayiko a ufulu amasangalala nazo, nzika zawo zimagawana ndi kulemekeza zikhulupiriro zapamwamba, chikhalidwe ndi miyambo. Anthu a ufulu, makamaka achinyamata, atha kutsutsana ndi njira zachikale – ndipo umu ndi m’ mene njira zabwino zopangira zinthu zimapezekera ndipo chitukuko chimaonekera. Koma ufulu si mdani wa chikhalidwe. Ngakhale nzika zochokera mayiko ena zomwe sizili mbali ya chikhalidwe cha m’ dzikoli ziyenera kulemekeza chikhali-dwecho ngati zikufuna kulandiridwa. Ngati akufuna kulembedwa ntchito ayenera kuphunzira chilankhulo. Ngakhale pamayambiriro sangamvetse miyambo ndi mfundo zoyenera kutsatira pochita zinthu m’ dziko la enilo, akuyenera kuchita machawi kuti azimvetse poopa

Maziko a dziko la ufulu

kupalamula, komanso ngati akufuna kutukuka. Sikuti azisalidwa kwenikweni: pakuti m'dziko la ufulu, aliyense amakhala ofanana ndi nzake. Koma palibe nzika – ngakhale aliyense - yemwe angakhale ndi anthu omwe sakugwirizana nawo, kapena omwe salemekeza chikhalidwe chawo kapena omwe sangathe kumvana nawo chiyankhulo.

Anthu amafuna anzawo, ndipo amawafuna ngati njira imodzi yopezera mwayi komanso kupititsa patsogolo zofuna zawo. Choncho ukakhala wakunja kwa gululo zinthu sizimakuyendera. Anthu m'dziko la ufulu sangakhale ndi zikhulupiriro zofanana, koma ngati anthu ndibwino kulolerana. Ufulu wa kaganizidwe, kuyankhula ndi kuchita zinthu omwe anthu amakhala nawo m'dziko la ufulu umalemekeza chikhalidwe, makhalidwe ovomerezeka ndi miyambo yomwe ilipo.

Ndani amafuna boma?

Kulumikizana kwa zokhumba za mbali zonse, mgwirizano, ndi udindo, chikhulupiriro ndi kudalirana kumapititsa patsogolo miyoyo yathu. Koma kuti izi zitheke sizisowa boma. Timagwirizana wina ndi m'nzake, ndi kutukuka kuzera umembala wathu m'magulu osiyana-siyana, popanda adindo aliwonse kulowererapo.

Ngakhale mu gawo la malamulo, lomwe wina atha kuliganizira kuti ndi mbali yaboma, timapanga ziganizo zonse mwaife tokha. Migwirizano mu dziko la ufulu siimapangidwa ndi kukhazikitsidwa ndi boma koma imapangidwa ndi mbali zomwe zakhudzidwa, zomwe zimaika mfundo zoti zivomerezedwe ndi kutsatidwa mosakakamizika. Ambiri omwe amalowa mu mgwirizanowu nthawi zambiri amagwirizana kuti kusamvana kwawo kulikonse kuyenera kuweruzidwa ndi oweruza oima paokha osati makhothi oyendetsedwa ndi boma, omwe amakhala ochedwetsa, amtengo okwera komanso opanda chilungamo kusiyana ndi omwe siaboma.

Izi zimathandiza kupanga maubale a magulu ndi migwirizano ngati anthuwo ali ofananirapo mu zambiri. Ngati anthu ambiri akuchokera ku mtundu umodzi wa anthu kapena chipembedzo chimodzi,

Maziko a dziko la ufulu

kumakhala kosavuta kulowa mu mgwirizano molimba mtima. Izi sizinathandizidwe ndi atsamunda kapena mikumano yomwe inkachitika nkondo zitatha omwe anaikanso malire ndi kulunzanitsa anthu amitundu yosiyasiyana pamodzi. Mayiko ambiri omwe posachedwapa akhudzidwa ndi nkondo, monga Syria, Libya, Lebanon kapena Iraq, kunalibe zaka zana zapitazo; anapangidwa ndi andale osati kufuna kwa anthu. Atsamunda aku Britain anakwitsanso pochita chimodzimidzi ku mayiko aku Afrika ndi ku dera la India, poika pamodzi anthu amitundu yosiyasiyana pansu pa ulamuliro umodzi.

Nzosadabwitsa kuti tili ndi mayiko ambiri osakhazikika, momwe maboma sangakwanitse nkomwe kuteteza miyoyo ndi katundu wa nzika zawo. Amenewo ndiye maziko pomwe tikuyenera kukhazikitsa dziko la ufulu komanso kupereka ufulu pa nkhani zachuma. Ndikovuta kupanganso chikhalidwe chogwirizana pamene chawonongeka komanso ngati kulemekezana ndi kukhulupirirana palibe zomwe zili nsanamira za mgwirizano wathu. Chabwino chomwe tingayembekezere nchakuti magulu osiyasiyanawa agwirizane pamfundo zomwe zingawalole kukhalira limodzi, ngakhale sakugwirizana bwino. Koma kukhalira limodzi ndi mgwirizano pakati pa anthu osiyana udzakhala wosavuta ngati mfundo za dziko la ufulu zingakhazikitsidwe, ndi chiyembekezo chakuti aliyense apindula mofanana.

N'chifukwa ninji boma liyenera kupatsidwa malire

Kodi boma liyenera kumachita chani?

Anthu ochepa masiku ano amakhulupirira kuti boma liyenera kukhala ndi mphamvu pa gawo lililonse la miyoyo yathu. Tonse timakhulupirira kuti udindo wa boma uyenera kukhala ndi malire munjira inayake. Anthu ambiri amavomereza kuti timafuna boma kuti lipange chiganizo kapena lichite chinthu choyenera kupanga ngati gulu, koma silikuyenera kulowerera pa zinthu zomwe tingazipange bwino patokha. Ndipo anthu ambiri oganiza bwino amati payenera kukhala malire poteteza atsogoleri athu kugwiritsa ntchito mphamvu zawo molakwika.

Maziko a dziko la ufulu

Nkhani kwenikweni sikukula kwa boma, koma chomwe chilipo kuti aganizire ndi kupanga, ndi kaganizidwe komanso kapangidwe kazinthuzi. Poti dziko la ufulu ndi chuma chake zimakhazikitsidwa pa chikhulupiriro, nzika za dziko zimayembekezera boma kuwateteza ku chinyengo ndi umbava. Koma sitingafune kuti boma lizimanga munthu ukayidi wa moyo wake wonse kaamba kozemba kulipira mtengo wokwerera basi, kapena kuika makamela a ukazitape m'nyumba ya aliyense kuti aziona ngati akutenga mwachinyengo nyimbo kuchokera pa masamba a pa intaneti ogawana zinthu. Zochita za boma zikuyenera kugwirizana ndi vuto.

Chifukwa china chomwe mphamvu zaboma zikuyenera kukhala ndi malire ndichakuti maganizo opangidwa ndi munthu – monga kugula ndi kugulitsa katundu – amapangidwa mosakakamiza. Koma ganizo lopangidwa ndi boma – monga kuletsa kugulitsa ndi kugula katundu wina – limadalira kugwiritsa ntchito mphamvu kuti litheke. Kugwiritsa ntchito mphamvu nkolakwika, ngakhale nthawi zina kuli kofunikira. Pamene tikupanga chiganizo potengera ndale tikuyenera kuonetsetsa ubwino womwe chingakwaniritse mosiyana ndi choipa chomwe chinapangidwa. Tisathamangire kukwaniritsa zabwino tisanaganizire zoipa zake.

Moyo wa gulu la anthu komanso wa pachuma umafuna ufulu kuti ziyende bwino. Zimapita patsogolo mu ndondomeko yapang'onopang'ono yoyesera ndi kulakwitsa zinthu zazing'ono. Anthu ambiri aluso lopanga zinthu amayesera maganizo ambiri osiyanasiyana–mwachitsanzo, katundu watsopano, kapena njira yatsopano yophunzitsira. Maganizo omwe sanachite bwino amasiyidwa msanga, koma omwe amapititsa patsogolo moyo amatengedwa ndi kufalitsidwa ndi anthu ena. Koma ngati boma likukhala ndi mphamvu zambiri pachuma kapena umoyo wa anthu limalepheretsa anthu kuyesera kaganizidwe katsopano: ndondomeko yokhazikika komanso ya pang'onopang'ono yoyesera ndi kulakwitsa imachedwetsedwa.

Kuwonjezera apo, pamene boma lalowererapo ndekuti nkhanayo ndiyayikulu. Limapanga ziganizo m'malo mwa anthu onse pankhani monga za katundu yemwe akuyenera kupangidwa kapena posankha

njira zoyenera kuphunzitsira. Mapeto ake, zimachedwetsa upangiri pa zinthu komanso chitukuko. Ndipo pamene boma lalakwitsa – zomwe zimachitika ndithu kumakhala kulakwitsa kwakukulu komanso kowononga.

Tikhalirani ndi boma?

Pali zifukwa zabwino zokhalira ndi boma kuti lizipanga zinthu zina. Tikhoza kufuna ulamuliro kuti upange ndi kukwaniritsa malamulo ena ofunikira okhudza m'mene tingachitire zina – kusankha mbali yamsewu yoyendetsa galimoto, mwachitsanzo, kapena kuonetsetsa kuti tikulemekeza zomwe tagwirizana.

Kuwonjezera apo, patha kukhala mapolojekiti ena omwe aliyense atha kufuna atapanga nawo, omwe ndiwosatheka kupangidwa (kapena kupangidwa mwadongosolo) ndi munthu aliyense. Izi nzomwe zimatengedwa kukhala katundu wa aliyense. Zitsanzo zikhoza kukhala ntchito za chitetezo ndi za apolisi: pamene aliyense amapindula ndi chitetezo chabwino, nkofunikira bwanji kuti aliyense adzipereke kugwira ntchito imeneyi? Chitsanzo china ndikuipitsa kwa mpweya m'mizinda yambiri ya m'mayiko ongotukuka kumene. Kugwiritsa ntchito mafuta osatulutsa utsi pophikira, kuika zosinthira utsi oipa kuchokera ku injini ya galimoto, ndi kuika zosefa zoipa pa chumuni cha mafakitale zingachepetse vutoli ndikupanga moyo kukhala wabwino kwa tonsefe. Koma anthu sangalole kudzipereka kuti achite izi podziwa kuti ena akhoza kupindula pa kudzipereka kwawo, ndikumagwiritsa ntchito mpweya wabwino chifukwa cha iwo. Koterotitha kukhazikisa malamulo ngati dziko pa izi kudzera mwa andale kuti aliyense athandizirepo kuchepetsa mpweya oipawu kudera kwawo, kapena aliyense apereke msonkho kulipirira apolisi ndi achitetezo. Tikatero tikwaniritsa zinthu zomwe zimapindulira anthu onse, zomwe sizingapezeke pamsika.

Anthu ena olimbikitsa za ufulu – titha kuwatchula *libertarians* – amati sitikufunikira boma kotheratu. Amati mayiko a ufulu amachita bwino popeza njira zogwirizanirana komanso zoperekera thandizo kwa aliyense, mwachitsanzo pothandiza mwachifundo, kapena

Maziko a dziko la ufulu

kupeza njira zabwino zina zoletsa ena kukolola pomwe sadalime popereka phindu kwa okhawo amene alipira. Iwo samakhutiranso kuti boma ndilofunika polimbikitsa migwirizano komanso kuteteza miyoyo ya nzika ku zoopsa komanso katundu wathu kuti asabedwe, poganiza kuti anthu paokha kapena magulu akhoza kudzipangira zon-sezi okha.

Ena omwe amalimbikitsa dziko la ufulu – amatchedwa *classical liberals*– amati mphamvu pang’ono zopangira ziganizo za ndale komanso zoyendetsera dziko zikufunika kuti zititeteze, kuonetsetsa kuti migwirizano ikutsatidwa ndi kupereka katundu wofunikira kwa anthu – ngakhale kuti likuyenera kumangochita ntchito zomwezi. Gulu la *libertarians*, limaopa kuti boma likangopatsidwa mphamvu pang’ono limawonjezera kwambiri: pafupifupi maboma onse padziko lapansi lero adadzipatsa maudindo paokha – osati zomwe anthu amafuna– zomwe zimaposa ntchito zenizeni zomwe tatchulazi.

Maganizo pa ufulu wamunthu komanso wazachuma

Kuganizira za malire a udindo za boma sichinthu chophweka. Anthu amatsutsana osangoti kuti ziganizo zizipangidwa ndi anthu paokha kapena pamodzi, komanso ngati nkofunika kuti zifikire ziganizo zathu patokha komanso pachuma.

Titha kupeza maganizo anayi osiyana.

- Gulu loyamba tikhoza kulitchula *individualistic*. Limati anthu paokha ayenera kukhala omasuka paokha kupanga ziganizo zokhudza moyo komanso chuma chawo.
- Motsutsana ndi awa ena ndi *authoritarians*, amalimbikitsa kuyang’anira pamodzi makhalidwe a munthu komanso chuma.
- Gulu lachitatu ndilomwe limalimbikitsa ufulu wamunthu pa ziganizo zokhudza chuma koma kulamulira limodzi zisankho za anthu. Awa atha kutchedwa osunga chikhalidwe (ngakhale mawuwa amatanthauza zosiyana m’zikhaliidwe zosiyana). Kusakaniza kwa ufulu wamunthu pachuma koma

kumuyang'anira pa zochita zake pa gulu zimapezeka kwam-biri m'mayiko ambiri a Kummawa.

- Gulu lomaliza ndilomwe limafuna ulamuliro pa zachuma koma anthu akhale ndi ufulu oyendetsa miyoyo yawo.

Funso: nzoona kuti boma lizipereka zinthu monga chitetezo?

Ayi. Pali zina zomwe zikuyenera kuganizidwa limodzi, monga ngati kuli koyenera kupita ku nkondo, koma pali zochepa zomwe sizingaperekedwe pawekha. Mayiko ambiri amapereka ntchito zina zachitetezo kwa makampani omwe siaboma, omwe amakonza magalimoto, sitima zapa madzi, ndege zankhondo ndi zida, kumanga ndi kukonza malo okhala asirikali, ndi kupereka chakudya komanso zina zofunikira.

Sikale kwambiri lomwe tinkaganiza kuti ndi boma lokha lomwe lingathe kutumiza makalata, ntchito zamalamya, kuyendetsa ntchito za pa njanji, kupereka madzi, gasi ndi magetsi, kumanga misewu, zipatala, ndi ndende, ngakhale kupanga zitsulo ndi kupanga magalimoto. Pano makampani omwe siaboma amapanga zonsezi. Ndipo chifukwa amakhala pa mpikisano, amayenera kupanga zabwino kwambiri.

Ndikovuta kwambiri kupeza dzina lenileni la gulu lotsirizali. Ku Amereka, amatchedwa *liberals*, koma uku nkugwiritsa ntchito mawuwa molakwika. M'mayiko ena, *liberals* amatanthauza *classical liberal*— ganizo lakuti ndondomeko zina za malamulo aboma zikufunikabe, koma zisankho zambiri pachuma ndi pamoyo wamunthu zikuyenera kukhala m'manja mwa anthu eni. Zotsatira zake, mawuwa anabedwa ndi andale komanso ophunzira aku Amereka omwe amakhulupirira za ufulu wamunthu koma omwe amafuna boma kukhala ndi mphamvu zambiri pazachuma.

Kufotokozero kwa mawu onsewa ndikosakwanira kufotokoza kuti chisakanizo cha maganizo okhudza nkhani za umoyo wa anthu ndi chuma ndi chani. Pali maganizo ochuluka ngakhale mugulu lililonse. (*Individualists*, mwachitsanzo, kufikiranso *libertarians*, omwe

Maziko a dziko la ufulu

amakamba za ufulu onse, kufikira kwa *classical liberals* omwe amakamba za udindo wochepa waboma. *Authoritarians* amachoka ku *totalitarians*, kulimbikitsa kukhala ndi mphamvu zonse, kufikira kwa *statists* omwe amalimbikitsa mphamvu zochepa ku makampani omwe siaboma popanga ziganizo.)

Mwazonsezi, nkofunika kudziwa kuti maganizo andale ndiovuta kuwalongosola mu chisakanizo chophweka chomwe chingalumikize pamodzi osiyana maganizo a dziko. Nzofunika kwambiri kuganizira molingana ndi kuchuluka kwa ufulu womwe anthu amaganiza kuti ukhalepo pa magawo awiri osiyana a moyo, wachuma komanso wamunthu payekha.

Nchifukwa chiyani munthu ayenera kukhala ndi chisankho?

Pali zifukwa zambiri zomwe munthu angafunire ufulu wa iye yekha komanso pachuma. Choyambirira, munthu ndiamene amadziwa bwino zosowa zake kusiyana ndi boma lomwe lili patali. Amakhala ndi chiyembekezo chake, mantha, maloto, zokhumba, zosowa, zofuna ndi zomwe akuyenera kukwaniritsa. Amazindikira bwino nyengo zawo ndi za anzawo, mabanja ndi magulu a anthu omwe amacheza nawo ndi kufuna kuthandiza. Akuziwa bwino za mwayi omwe alinawo komanso mavuto omwe angadze chifukwa cha zochita zosiyanasiyana. Kotero akhoza kupanga bwino ziganizo zokhudza miyoyo yawo ndi tsogolo lawo.

Palinso mfundo ya makhalidwe kuti kwa anthu omwe akupangiridwa zisankho sianthu kwenikweni koma akapolo chabe. Choncho ngati sakukhala ndi udindo pa zomwe zikuchitika, sangaphunzire pa zomwe achita bwino komanso kulakwitsa. Akhoza kuzunzika ndi mfundo zoipa zopangidwa ndi adindo, koma sangachitenso kanthu kenikeni kuti zisadzachitikenso, ndipo saona chifukwa chochitira zimenezo. Koma anthu omwe amapindula ndi zomwe achita bwino, kuvutika ndi zomwe alakwitsa, amalimbikitsika kubwereza zomwe zatheka ndi kupewa zomwe sizinatheke.

Kusiyana pa zochita za anthu kumalimbikitsa chitukuko

Palinso ubwino wokhala pakati pa anthu osiyanasiyana. Anthu amene

Maziko a dziko la ufulu

ali ndi ufulu wopanga ziganizo zawo amachita zinthu mnjira zambiri zosiyanasiyana. Amatha kusankha, kuchita zomwe akuziona panthawiyo. Atha kuyeserera makhalidwe osiyanasiyana – ‘kuyeserera pakuchita, monga katswiri wakaganizidwe kozama wa ku Mangalande John Stuart Mill analembera mu nkhani yake ya mchaka cha 1859 yotchedwa *‘On liberty’*.¹¹Ena mwayiwo amatha kuchita bwino, ena ayi. Koma tonsefe titha kuphunzira kuchokera kwaiwo, ndikupititsa patsogolo miyoyo yathu, kulimbikira zomwe zikuthekazo ndi kusalimbikira zomwe sizikutheka.

M’mayiko a ulamuliro wamphamvu kwambiri, mosiyanitsa, pali njira imodzi yokha yopangira zinthu yomwe imatsatidwa chifukwa ziganizo zimamangidwa pamodzi. Cholakwika chilichonse chimakhala vuto la aliyense. Ngati njira yomwe yasankhidwa yachita bwino, sitiloledwa kuyesera njira ina yomwe ingathenso kuchita bwino kwa-mbiri. Kotero kupanga ziganizo kumakhala kochedwerapo komanso kodalira adindo. Kutukuka m’dziko lotero kumakhala kochedwa komanso kopweteka.

Mu dziko la ufulu pa zachuma, opanga katundu amakhala akudziwitsidwa zoyenera kuchita ndi makasitomala. Nthawi iliyonse ya tsiku lililonse, anthu amakhala akusankha katundu yemwe akumufuna kusiyana ndi wina. Amakhala akusiyanitsa mtengo, kudalirika, kukula, maonekedwe, mtundu ndi ubwino uliwonse wa katundu yemwe akugula. Anthu opanga zinthu amauzidwa mwachangu kusiyantsa kumeneku, ndipo amaona chimene chikuyenda malonda komanso chomwe sichikuyenda malonda. Pozindikira kuti opikisana nawo akuchitanso chimodzimidzi, ogulitsa amafulumira kupanga zambiri zomwe anthu akufuna kusiyana ndi zomwe sakuzifuna. Ndipo amayesera kupanga katundu watsopano ndi osiyanasiyana yemwe akuona kuti makasitomala angamukonde kwambiri.

Mosiyanitsa ndi m’dziko lomwe adindo ali ndi mphamvu zosankha katundu woyenera kupangidwa. Mosatengeranso kuti ali ndi

¹¹ John Stuart Mill, ‘On liberty’, 1859, in John Stuart Mill, *On Liberty and Other Essays*, Oxford University Press, Oxford, 2008.

Maziko a dziko la ufulu

mphamvu pa chilichonse kapena magawo angapo, monga zikhalira: kupanga zisankho za chomwe chiyenera kupangidwa ndi kapangidwe kake kumakhalabe kochedwa komanso kovuta. Makasitomala amatha kuonetsera zokonda zawopakpita zaka zingapo, kudzera mu chisankho. Koma samasankha katundu aliyense yemwe akupangidwa kapena ubwino wake: ngati angachite chisankho chenicheni ndekuti asankha gawo lonse la mfundo zomwe zingakhale ndi chilichonse monga chitetezo, maphunziro, ndi zipatala kufikira ku ulimi wa mthirira, ulimi ndi mayendedwe a kumudzi. Adindo sadalira kuu-zidwa mosalekeza kumene makasitomala amachita kwa ogulitsa katundu pa pamalonda. Anthu amakhala ndi mphamvu zochepa zoumiriza atsogoleri kupanga zinthu zatsopano ndipo makasitomala sapeza zenizeni zomwe akufuna.

Kuipa kwa kulowerera

Pali mayiko ochepa lero omwe boma limayendetsa – kapena kuyesera kuyendetsa – mapangidwe a zinthu dziko lonse. Zomwe zachulukira nzakuti boma limayang’anira mbali zingapo – makamaka zomwe zimaoneka zofunikira, monga zipatala, sukulu, ulimi komanso zachitetezo – kapena amafuna kulimbikitsa kapangidwe ka zinthu pothandiza gawo lina, kuika malire amtengo ndi malamulo oyendetsa mabizinezi.

Ngakhale boma lingayendetse mbali zochepa chabe, mavuto a kupanga ziganizo mochedwa komanso movuta amakhalapobe, makamaka pamene mbalizi zofunikira kwambiri. Mwachitsanzo boma litha kuyendetsa mbali yopanga chakudya: koma ngati silingakwanitse kufikira mlingo wa chakudya chimene anthu akuchifuna, chotsatira chake ndi njala yayikulu.

Chimodzimodzi, kuyesera kwa boma kupanga zinthu mongoganizira kumadzetsanso kusagwirizana kwa zinthu zomwe zikuperekedwa ndi zomwe zikufunidwa. Mwachitsanzo, andale atha kuyesera kuti mitengo wa katundu wina kapena ntchito zina ukhale otsika – monga chakudya, ntchito za chipatala, kapena chiwongola dzanja – poika malire amtengo wa izi. Zikatero ogulitsa amapeza phindu lochepa pogulitsa zinthuzi. Mtengo omwe amagulitsira sumagwirizana ndi

ntchito yomwe agwira popanga katunduyu. Koteru amapanga katundu wochepa kapena kungosiyiratu mbali imeneyi.

Mapeto ake ndi kuperewera kwa zinthu. Pa mitengo yotsika yokhazikitsidwa ndi lamulo, opanga katundu amapanga wochepa koma ogula amafuna kugula wambiri. Chakudya chitha kukhala chotsika mtengo, koma pa chisakupezeka; chiwongola dzanja chitha kukhala chotsika koma ngongolezo palibe; zipatala zitha kukhala zaulere koma uyenera kuima pa mnzere nthawi yayitali kuti uthandizidwe.

Pali mavuto enanso ofananirapo pamene boma likufuna kupanga katundu poperekako gawo lina lothandizira popanga katundu. Bungwe la mgwirizano wa mayiko aku ulaya (European Union), mwachitsanzo, lakhala likuperekako gawo lina ndi kuteteza gawo lake la ulimi, pofuna kuonetsetsa kuti chakudya chikupezeka kwambiri komanso mosalekeza, koma kwenikweni limafuna kuteteza alimi aku Ulaya womwe anali wochepekedwa ku mpikisano ndi mayiko ena (pofuna kuti gulu lofunikirali likhale mbali yawo pandale). Kuperekako gawo lina popanga katundu kumathandizira kuti zinthu zochuluka zipangidwe – yemwe amathanso kungounjikidwa osagulidwa.

Koma pali zotsatira zina, zosaonekera kwambiri kusiyana ndi izi. Omwe amapindula kwambiri ndi mchitidwe wothandizirako gawo lina mu ulimi ku Ulaya ndi omwe ali ndi malo ambiri osati alimi osauka. Ndipo katangale wakula, pomwe alimi akhala akufuna thandizo la zakudya zomwe samapanga. Pali nkhani zambirimbi zofananirapo ndi izi padziko lonse lapansi, ngakhalenso mu mbiri: Adam Smith, katswiri pa kayendetsedwe kachuma wa mdziko la Scotland anadandaula m’buku lake la mchaka cha 1776 lotchedwa ‘*The Wealth of Nations*’, anadandaula zamabwato ansomba za *hering* momwe ankakozedwera kuti achulukitse thandizo lolandira kusiyana ndi nsomba zomwe angagwire¹².

Kuthandizirapo kulikonse pa kapangidwe ka zinthu kumachulukitsa zipangizo ku gawo limenelo kusiyana ndi ena kumene nthawi,

¹² Adam Smith, *The Wealth of Nations*, 1776, Bowok IV, ch. V.

Maziko a dziko la ufulu

mphamvu ndi mpamba zikanagwiritsidwa bwino ntchito. Mwachitsanzo, maboma ambiri akuthandizirapo popanga mphamvu za dzuwa komanso mphempho zokwera mtengo, kugwiritsa ntchito ndalama za anthu komanso zamabizinesi zomwe zikanagwiritsidwa ntchito moyenerera. Uku ndikulowetsa pansi ntchito zachuma zomwe zimabwezera chitukuko cha anthu m’mbuyo.

Maganizo opangidwa ndi anthu ochepa

Chifukwa china chosankhira kuti ziganizo zizipangidwa ndi anthu kusiyana ndi adindo nchakuti zisankho zimapangidwa ndi anthu ochulukira kusiyana ndi anthu ochepa omwe ali ndi udindo. Nzosakayikitsa kuti adindo omwe amapanga zisankho m’ malo mwa aliyense amayenera kupatsidwa mphamvu kuti maganizowo agwire ntchito. Koma adindowo nawo ndi anthu; ndipo nkovuta kwa iwo kuti akane mayesero pogwiritsa ntchito mphamvuzo popititsa patso-golo zofuna zawo ndi za banja lawo, anzawo kapena oyandikana nawo, mtundu wawo kapena chipani chomwe akuchokera. Migwirizano yogwira ntchito za boma komanso mphamvu zoyendetsera bizinesi ndi ntchito zachuma zimaperekedwa kwa anzawo. Ndalama zambiri zimagwiritsidwa ntchito kutukula maboma omwe atsogoleriwo akuchokera. Ntchito m’boma, kupolisi, ndiku makhoti zimapita kwa omwe amawakonda, osati omwe zikuwayenera.

Koma pamene mphamvu yopanga ziganizo yachepetsedwa kwa andale ndikupatsidwa kwa anthu wamba, nkhani ya katangale wotere imachepa. Boma likhoza kuika chidwi pa udindo wake weniweni woonetsetsa kuti palibe kuponderezana – osati kupindula ndi mchitidwewu.

Nthawi zina kudyerana masuku pamutu kumakhala kovuta kukuona. Tate wa kayendetsedwe kachuma kamakono wotchedwa Adam Smith adalemba kuti ‘Palibe luso lina lomwe boma lina limaphunzira pa linzake mwachangu, kuposa kusolola ndalama za anthu’¹³. Mwachitsanzo, pobwereka ndalama, boma limagwiritsa ntchito ndalama pa zitukuko zomwe zingawapangitse kupambana masankho

¹³ Ibid., Bowok V, ch. II, Part II, Appendix to Articles I & II.

komanso kulemeretsa owatsatira, mbali inayi akuika chipsinjo cha ngongoleyi pa ena. Ngongoleyi ikhozanso kukhudza m’badwo wina wotsatirawo. Ngati ngongoleyi yafika pokulitsa, atha kungopanga ndalama zambirimбири ndikubweza ngongoleyo ndi ndalama yotsika mphamvu. Koma kuba kumeneku, kaya moonekera kapena mobisa, kumagwetsa mphwayi anthu kupanga chuma. Amakhala osalimbikitsika kuyamba mabizinezi atsopano ndi kukhala ndi mpamba wopindulitsa, ndipo dziko lonse limazunzika.

Boma la dziko la ufulu lenileni silingangoledwa kubwereka ngongole pokhapokha zitavutitsitsa, ndipo ngakhale zitakhala choncho likhala ndi malire. Ndipo silingakhale ndi ulamuliro onse pa ndalama ndikupanga zambirimбири pamene likufuna ndalamazo. Ndipo misonkho m’dziko la ufulu ikanakhala yochepe yotoleredwa kwa anthu ambiri – osati yongounjikidwa pa adani pa andale kapena anthu ochepe okha monga ‘olemera’. Misonkho ikanakhala yophweka, yopanda kampeni kumphasa, yosavuta kupereka komanso yodziwikiratu. Sii-kanangoperekedwa kwa mabungwe a boma kapena omwe siaboma omwe cholinga chawo ndikungochulutsa ndalama zomwe akutolera kwa anthu olupira misonkho.

Mfundo ya atsogoleri opanga ziganizo mmalo mwa anthu

Kaganizidwe ka olamulira ambiri n’kakuti ayenera kupanga ziganizo zonse chifukwa anthuwo, ngati ana, sangathe kudzipangira okha ziganizo. Uku nkudzitsutsa okha: izi zimanyozetsa ‘anthu’ omwe ndi gwero la mphamvu zawo. Ndipo ndi mbwerera kuganiza kuti anthu omwe ali ndi nzeru zosankha boma labwino, akhale opanda nzeru zoyendetsera miyoyo yawo.

Pali nthawi zina zomwe dera lonse lingapindule ngati anthu akanao- netsako khalidwe labwino. Koma zambiri mwa izi ndi nkhani zachikhali- dwe zomwe lamulo silingagwirepo ntchito. Ndipo ngakhale tingawalimbikitse anthu kuchita zinthu zimene zingathandize ena pamakhalidwe, boma la ufulu silingazipange izi. Limangopatsidwa mphamvu loletsa choipa kuchitikira ena, osati kukakamiza anthu kuti athandize ena. Pali mfundo ya ‘katundu wagulu’ yomwe imapanga

Maziko a dziko la ufulu

anthu kuchitapo kanthu pa zinthu zothandiza aliyense monga chitetezo, koma izi sizichitika kawirikawiri.

Nzoona kuti anthu kawirikawiri amadabwa ndi kusowa kwa chidwi pankhani zina monga m'mene zinthu zoyendetsedwa ndi boma zikugwirira ntchito. Koma izi zimakhala choncho chifukwa amadziwa kuti kudandaula ndikungotaya nthawi pakuti palibe chomwe chingasithe. Ngati chinachake chinasintha chifukwa cha kulowererapo kwa anthu, bwenzi anthu ambiri akutero.

Funso: Kodi nzoonadi tonse tili ndi udindo kuboma?

Ayi. M'dziko la ufulu, boma lili ndi udindo paife. M'malo ambiri, maboma anakhazikitsidwa, ndipo amakhalapobe chifukwa chokakamira. Ili siboma lovomerezeka. Boma la dziko la ufulu ndilomwe laikidwa ndi anthu ngati bungwe kuti lipange ziganizo kapena kupanga zinthu zochepa zomwe ziyenera kuganiziridwa kapena kupangidwa ndi gulu pamodzi (monga chitetezo) kapena mosakondera (monga chilungamo). Limakhalapo kuti litumikire nzika – osati mosemphana.

Njira zoikira malire pa boma

Demokalase

Mu nthawi zochepa m'mene maganizo agulu sangazembedwe, dziko la ufulu limafunsa maganizo a anthu onse, pakuti zotsatira zake zikukhudza anthu onse. Mwanjira ina, pali demokalase.

Sizingakhale kuti gulu lonse la anthu lipanga nawo ganizolo – izi zitha kukhala zovuta komanso zotenga nthawi yayitali. Nthawi zambiri, anthu amasankha anthu oti akawaimilire popanga ziganizo m'malo mwawo. Anthu owaimirirawa si nthumwi chabe, zongoyembekezereka kunena maganizo a owasankhawo; nawo amabweretsanso kaganizidwe kawo pochita izi.

Demokalase siyofanana ndi kaganizidwe kongowona m'mene anthu ambiri afunira. Anthu ochuluka akhoza kufuna kuti anthu achipebedzo china kapena mtundu wina wa anthu omwe ndi ochepa

Maziko a dziko la ufulu

aphedwe, koma boma la dziko la ufulu silingapange izi. Limakhalapo kuti liteteze ena kuti asapwetekedwe, osati kukolezera zimenezi. Ntchedzero yakalekale imafotokoza demokalase ngati nkhandwe ziwiri ndi nkhosa kusinkhasinkha chakudya choti chidyedwe madzulo. Koma m'dziko la ufulu pali malire a mphamvu za anthu ochuluka oteteza anthu omwe ndiwochepa.

Vuto lalikulu simmene timasankhira boma, koma m'mene tingayikire malire pa mphamvu zake. Nawonso ndi anthu: mphamvu zomwe timawapatsa zitha kuwanyenga. Ngati ufulu ukuyenera kutetezedwa, pakuyenera kukhala njira yochotsera atsogoleri paudio. Zisankho mudziko la ufulu sikungosankha atsogoleri basi komanso ndi njiranso yowachotsera.

Anthu ena olimbikitsa ulamuliro wamphamvu amati zisankho zima-ngobweretsa mpungwepungwe pamene maboma osiyana, mwina a mfundo zotsutsana kwambiri, amavoteredwa ena kukhala m'boma ena kuchotsedwa. Koma chifukwa mphamvu zaboma zimakhala ndi malire mu dziko la ufulu, mlingo wa mpungwepungwe uliwonse umachepetsedwa. Ngati boma lili lovomerezeka, kuthekera kwam-pungwepungwe kumakhala kochepe kusiyana ndipamene sizili chonchi. Pogwiritsa ntchito mphamvu za nthambi, maboma osavomerezeka atha kulamulirabe nthawi yayitali; koma njira zokhazo komanso zoyenerera zosinthira ndi kudzera mu zisankho zamtendere zochitika pakapita nthawi kapena kuukira kokhetsa nako mwazi. Anthu m'dziko la ufulu amakonda zisankho zomwe zimachepetsa kukakamiza ndi chiwawa, ndipo kusintha ndi chitukuko zimachitika mwachangu.

Pali zina zomwe zimafunika kufikiridwa ngati zisankho ziyenera kukhala zovomerezeka. Pakuyenera kukhala, mwachitsanzo, chisankho chenicheni cha zipani. Ngati pali munthu mmodzi yekha kuti asankhidwe, ndiye kuti sichisankho cha ufulu: m'dziko la ufulu pamayenera kukhala maganizo osiyanasiyana. Izi zimatanthauza kuti anthu oimirira zisankho osiyanasiyana ayenera kulongosola ndi kusindikiza mfundo zawo, ndiponso kukhala omasuka kutsutsa

Maziko a dziko la ufulu

anzawo ndi zipani zina. Ndipo anthu ayenera kukhala omasuka kusankha mtsogoleri wakumtima kwawo mosaopa kuti achitiridwa nkhanza – choncho masankho ayenera kukhala achinsinsi. Mayiko ena amaika malire pa ndalama zogwiritsira ntchito pomemeza anthu kuti asapereke mwayi waukulu kwa anthu kapena zipani zachuma kwambiri. Ambiri amaika malire a zaka zomwe mtsogoleri akuyenera kulamulira zisanafike zisankho zina, osati kulisiya boma lolamula kuganiza za ichi.

Kupanga ziganizo kwa gulu

Maboma am'mayiko opanda ufulu analowa m'boma mokakamiza. Ena amakhalabe m'boma mokakamiza, ngakhale ambiri amapeza njira yoti aonekere ngati ndi ovomerezeka – mwachitsanzo, podzi-khazikitsa ngati oyang'anira chipembedzo kapena chikhaliidwe. Mosiyana ndi dziko la ufulu, boma limakhalapo pa zolinga zochepa komanso movomerezeka ndi anthu.

Ngakhale zili choncho, maboma amasemphana zolinga zawo zoteteza anthu kuti asapwetekedwe ndi kuchitikira limodzi zomwe sizingapangidwe ndi anthu paokha. Mwachitsanzo, nthawi zambiri amatenga gawo lalikulu popereka katundu waboma. Ngakhale ganizo losankha katundu yemwe akuyenera kuperekedwa lingapangidwe ndi anthu, atha kuperekedwa, yense kapena ochepa, ndimakampani omwe siaboma. Mwachitsanzo, mabungwe achifundo, akhoza kusamalira osauka ndi odwala. Ndipo pankhani yoteteza kuti ena asapwetekedwe – monga ku zotsatira za kuipitsa chilengedwe – mlingo wa vutoli utha kuvuta kuyeza kwake ndipo kulowererapo kwa boma kutha kukhala kovuta.

Ngati ziganizo zina zikuyenera kupangidwa ndi gulu, ndi malamulo anji atsatidwe popanga ziganizozo? Zabwino ndi kukhala ndi chigwirizano: aliyense atenge nawo mbali popanga chiganizocho, ndipo pasachitike kalikonse pokhapokha aliyense avomereze. Poti anthu sangalole kuvotera ganizo lomwe akuliona kuti liwapsinja, kotero kuthekera koti ganizo lopangidwa ndi gulu litha kuwapsinja nkochepa.

Koma chigwirizano ndichovuta kuchikwaniritsa. Poyamba, zitha kutenga nthawi yayitali kuti aliyense akhale ndi nthawi yowerenga ndikuvota pa ganizo lililonse. Nchifukwa chake amasankha aphungu m'malo mwake. Ndipo kufika pangwirizano wa chilichonse kutha kukhala kovuta, chifukwa munthu aliyense ayenera kuvomereza chikonzero chonse. Kotero, maganizo agulu – opangidwa ndi zisankho zagulu, riferendamu kapena mavoti mu Nyumba ya Malamulo – amapangidwa ndi anthu ochuluka. Atha kukhala anthu oposa makumi asanu pa zana lililonse (50+1%) kapena anthu awiri pa atatu aliwonse. Izi zimachepetsa mavuto omwe amabwera popanga zisankho mbali inayi kuonetsetsa kuti ambiri mwa anthu mdziko atenga nawo mbali kusiyana ndi atsogoleri ochepa.¹⁴

Zokhumba zamunthu wovota payekha

Pali nkhani ina ya mfumu yaku Roma, yomwe inafunsidwa kusankha yemwe waimba bwino pa mpikisano, atamvetsera mmodzi anapereka mphoto kwa wina, ponena kuti winayo atha kuimba bwino kuposa oyambayo. Ndipo lero, anthu ali ndi mchitidwe woganiza kuti pamene sali okhutsidwa ndi zomwe dziko la ufulu pa anthu ndi pachuma likupanga, ndi ntchito yaboma kukonza zinthu. Mwachitsanzo, ngati opanga zinthu akanika kupereka zinthu za gulu monga chitetezo ndi umoyo wa anthu kapena chitetezo, boma liyenera kupereka mmalo mwake. Kapena ngati fakitale ikuipitsa mpweya, boma likuyenera kuchitapo kanthu poletsa zimenezi. Koma izi siziyenera kutero.

Misika itha kukanika kutipatsa zomwe tikufuna nthawi zina. Koma pamene tikukamba zakulephera kwa misika, tizikumbukira kuti pali kulephera kwa boma pompo. Ngakhale m'mayiko a ufulu, boma sizida zongoganiza za anthu, molondola ndi mosakondera. Zokhumba za anthu paokha zimakhalapo m'boma, kuchokera kumtunda mpaka kumunsi.

Anthu amaganiza kuti zisankho ndi njira yoonetsera 'zokhumba za

¹⁴ For a more detailed summary of this and the following points, see Eamonn Butler, Public Choice – a Primer, Institute of Economic Affairs, London, 2012.

Maziko a dziko la ufulu

gulu' ndi kuzikwaniritsa. Koma m'dziko la ufulu muli zokhumba zosiyanasiyana – ndipo zokhumba zimenezi zimatsutsana. Anthu omwe amafuna misonkho yotsika amatsutsana ndiwomwe amafuna boma kugwiritsa ntchito ndalama zambiri. Omwe angapindule ndi msewu watsopano amatsutsana ndiwomwe nyumba zawo zitagumulidwe pomanga msewuwu. Zisankho sizimakhazikitsa zokhumba za gulu. Zimangolinganiza zokhumba za anthu zosiyanasiyana. Ziganizo za gulu zimapangidwa pa tsinde la kutsutsanaku.

Zokhumba za andale paokha

Monga m'mene munthu ovota amafuna kukwaniritsa zokhumba zawo, chimodzimodzinso andale. Anthu ambiri amaona udindo wawo ngati njira yolemerera kapena yothana ndi adani awo. Atha kutengedwa ngati ofooka ngati sangagwiritse ntchito ofesi yawo motere. Ngakhale m'mayiko a ufulu, katangale likhoza kukhalanso vuto.

Ngakhale pamene andale akufunitsitsa kutumikira anthu, choyambirira akuyenera kupeza mpando. Akuyenera kukhala ndi mavoti okwanira kuti asankhidwe. Izi sizikutanthauza kuti akuyenera kuonetsera maganizo a gulu lambiri. Atha kupeza mavoti ambiri pokopa anthu ochepa omwe alibe owaimirira.

Magulu a anthu ochepa omwe amakhala ndi zokhumba zamphamvu amachita bwino pandale chifukwa amakhala ndi chinachake chomwe akufuna pokhazikitsa mfundo zowakomera – monga kuthandizirapo pa ntchito za mafakitale awo omwe. Pakukhala ochepa komanso olimbikira, kumakhala kosavuta kuyendetsa zinthu, ndi kuchita zinthu limodzi pokopa ndi kunyengerera anthu. Koma magulu aku-luakulu, monga ogula ndi olipira msonkho, omwe samakhala ndi mfundo yeniyeni, ndiwovuta kuti amemezane. Ndipo samalimbikitsidwa kwenikweni, chifukwa zotsatira za mfundo monga kuthandizirapo kwa boma pa mafakitale zimagawidwa mochepa kwa onse.

Mgwirizano ndi kuthandizana pa ndale

Mphamvu za maganizo a anthu ochepa zimakula pamene magulu a zokhumba zofanana apanga migwirizano ndi ena kuti aphantikizane

pa chisankho. Mgwirizano wa magulu angapo, onse ofuna kuika wo-waimirira m’modzi, umapereka mwayi kwa woimirayo kusiyana ndi wina aliyense payekha.

Chizolowezi chomwecho cha zokhumba zapadera chimachitikanso ku Nyumba ya Malamulo. Aphungu omwe akufunitsitsa zitukuko zina muboma lawo atha kupereka mavoti awo kwa aphungu ena omwe akufunanso zitukuko zina m’dera lawo. Koma zotsatira za ndondo-meko zimenezi ‘uvotere zofuna zanga nane ndivotera zako’ – yotche-dwa kuthandizana pa ndale – nchakuti mfundo zambiri zotero zimavomerezedwa ndipo boma limakula kwambiri koposa m’mene wina aliyense akufunira.

Pamene malamulowa ayamba kugwira ntchito, zokhumba zawo zimaonekera. Adindo omwe apatsidwa ntchito yoyang’anira amakhalanso ndi zokhumba zawo. Kupeza kwawo ndi malipiro awo amatengera kukhala ndi ogwira ntchito ambiri, ndipo – modziwa kapena mosadziwa – amapanga mndandanda wa kagwiridwe ka ntchito kukhala kosamvetsetseka kuti akwaniritse kukhala ndi ogwira ntchito ambiri, ndondomeko yomwe imadziwika kuti kumanga ufumu. Kuwonjezera apo, amanyengereredwa kwambiri ndi magulu a anthu ochepa kusiyana ndi anthu onse, kotero amagonjera kwambiri magulu a zokhumba zawowa, ndiponso mwina amatha kulandira ziphuphu kuchokera kwaiwo.

Kuika malamulo

Powomba nkota, posankha boma, kupanga malamulo ndi kuwagwiritsa ntchito, magulu a anthu ochepa okhala ndi zokhumba zoikidwa pamodzi amawerengeredwa kwambiri kusiyana ndi gulu lomwe limakhala ndi maganizo osiyanasiyana. Ziganizo zopangidwa pazifukwa zandale sizigwirizana ndi maganizo a gulu la anthu. Ndipo gawo la boma lili ndi kuthekera kokula kuposa m’mene anthu akufunira, kuposa m’mene zingamvekere bwino, ndinso kuposa m’mene zingafunikire kuti dziko la ufulu likhazikike – kufikira pamene ufulu waphwanyidwa.

Maziko a dziko la ufulu

Mayiko a ufulu ambiri amakhazikitsa malamulo osiyanasiyana kufuna kuchepetsa mavutowa. Gawo lofunikira kwambiri pa zimenezi ndi masankho. Koma alibe mphamvu yokwanira yoletsa andale ndi adindo. Amakhalapo patalipatali, ndipo kawirikawiri zipani zazikulu ndizo zimatenga gawo lalikulu, zomwe zimapangitsa kusintha kukhala kochedwa. Zoletsa zamphamvu nzofunika.

Mgwirizano wa malamulo oyendetsera dziko

Njira yabwino yoikira malire pa mphamvu yaboma ndiyokhazikitsa malamulo ovomerezeka ndi aliyense, kapena ndi anthu ochuluka, omwe amalongosola m'mene zisankho ziyenera kuchitikira komanso kapangidwe ka ziganizo za ndale. Ngati aliyense angagwirizane nawo malamulowo, kumakhala kovuta kuti boma liike malamulo olikomera – mwachitsanzo, poletsa oimirira otsutsa kapena kuika misonkho yokhwima pa omwe avotera otsutsa.

Dongosolo landale kuikiridwa malire posiyanitsa mphamvu za nthambi zaboma. M'malo moti munthu mmodzi kapena nthambi imodzi ikhale ndi mphamvu zonse zopangira malamulo, ganizo ndilomwaza mphamvu imeneyo ku nthambi zosiyanasiyana, zomwe pazokha zikhoza kuimitsa, kusintha kapena kuletsa zomwe nthambi zina zingapange. Pachifukwa ichi, nthawi zina imachedwa njira yakauniuni.

Ngati nthambi imodzi yaboma, gulu la akuluakulu a mbali olamulira kapena Nyumba ya Malamulo, ili ndi mphamvu zonse, zipani zikuluzikulu kapena magulu ena a zokhumba zawo akhoza kuyesetsa kuti apeze mwayi umenewu kuti uwapindulire. Koma ngati malamulo agawa mphamvu pakati nthambi ziwiri zaboma, kumakhala kovuta kuti magulu ena a zokhumba zawo apeze ulamuliro umenewu. Ngati nthambizo zasankhidwa mosiyana, kutha kukhala kovutirapo kwambiri kuti ena a zofuna zawo akhale ndi mphamvu mbali zonse. Ngati imodzi mwa nthambiyo itha kuletsa kapena kusintha mfundo zopangidwa ndi ena, zimapangitsa mchitidwe wothandizana pandale, komanso kupondereza magulu anthu ochepa, kukhala kovuta.

Ngati chiletso mu ndondomeko ya kauniuni wa nthambi zaboma, ma-

Maziko a dziko la ufulu

lamulo ambiri oyendetsera boma m'mayiko a ufulu amasankha pulezidenti ngati oimirira anthu onse, yemwe (amayembekezeredwa) akuyenera kukhala pamwamba pa zipani ndi kutsutsa malamulo omwe akupsinja magulu a anthu ochepa.

Chiletso china choletsa kupondereza ndikukhala ndi nthambi ya khoti yoima payokha. Ichi nchofunikira kwambiri mudziko la ufulu. Oweruza milandu asakhale ndi mbali a andale, ndipo ayenera kukana malamulo osavomerezeka komanso oponderezera magulu a anthu ochepa – ndipo ayenera kugwira ntchito yawo mosaopa mkwiyo wa andale.

Malamulo oyendetsera dziko nthawi zina amaika malire pa zochita za boma monga kulinganiza dongoloso lachuma – poonetsetsa kuti ndondomeko yake ikhale yokhazikika kwa kanthawi (monga zaka zitatu kapena zisanu), komanso kuika malire angongole za pachaka ndi kuchuluka kwa ngongole zonse zaboma. Ena amaika malire a mlingo wa ndalama zonse boma lingagwiritse ntchito, kuti aonetsetse kuti boma silikugwiritsa ntchito mphamvu molakwika. Kuwonjezera apo, pamatha kukhala malire anthawi yokhalira pampando pofuna kuti andale asakhale m'maudindo zaka zambiri, ndi *sunset clauses* poletsa nthambi zina zaboma kupitirira malire a mphamvu zawo.

Unyinji woyenera

Njira ina yotetezera anthu ochepa ndi kudzera muvoti ya unyinji woyenera. Ufulu ukanatha kukhala wosatetezeka ngati, mwachitsanzo, olamula akanakhala ndi kuthekera kosintha malamulo ndi mavoti a aphungu ochepa mu Nyumba ya Malamulo. Choncho mayiko a ufulu amaika ziletso zovuta – monga mavoti awiri pa anthu atatu aliwonse munthambi zonse komanso mlingo wochuluka pamasankho ofuna kumva maganizo a anthu kapena] mu zigawo kapena dziko lonse.

Mu nkhani zomwe nkosavuta kupondereza kwambiri magulu a anthu ochepa molakwika, ziganizo zikuyenera kupangidwa ndi unyinji wa anthu ambiri. Mwachitsanzo, ndikosavuta kukhazikitsa misonkho

Maziko a dziko la ufulu

imene ingapweteke kagulu kena ka anthu. Ena olimbikitsa dziko la ufulu amafuna kuti malamulo a msonkho – osati mlingo wa msonkho koma yemwe akupereka msonkho komanso msonkho wanji – uyenera kusankhidwa mogwirizana ndi gulu lonse kuti magulu a anthu ochepawa atetezedwe, ngakhale unyinjira uli wochulukitsa.

Anthu omangika

Pa msika uliwonse, ogulitsa amakhala omasuka kupitisa malonda awo kwina ngati pali chinyengo kapena ngati anthu sakupereka ndalama zoyenerera ndi katundu. Koma ngati boma lanu likuchita chinyengo kapena kukuponderezani, palibe kulikonse kothawira. Utha kungoganiza zotuluka mdzikolo– koma potengera chiyankhulo ndi zovuta zina, iyi siyimakhala njira yabwino. Uku ndiko kukakamizika – zomwe zimapangitsa kukhala kofunika kuti udindo wa boma, ndi mbali zake zonse, ziyalidwe bwino komanso kupatsidwa malire mosayerekeza ndi omwe akuyenera kutero pofuna kusunga komanso kupititsa patsogolo ufulu wa anthu.

4 KUFANANA NDI KUSIYANA

Kufafana m'dziko la ufulu

Anthu ambiri amaganiza kuti anthu m'mayiko a ufulu ayenera kukhala osiyana kwambiri. Pakuti, amalola anthu kufunafuna ndi kukhala ndi chuma chambiri. Izi (zomwe zimapitisa patsogolo ganizoli) zikuyenera kudzetsa kusiyana kwambiri pachuma.

Koma ganizoli ndilolakwika. Monga taonera, kusiyana kwa chuma pakati pa mayiko a ufulu ndi opanda ufulu pafupifupi ndikofanana. Ngati pali kusiyana, mayiko a ufulu amakhala ofananirapo.

Kuwonjezera apo, mayiko opanda ufulu ali ndi kusiyana kwina kosakhala kwachuma komwe sikupezeka m'mayiko a ufulu. Nzika za m'mayiko a ufulu zitha kufuna kuwonjezera chuma chawo kapena ndalama zomwe amapeza posintha ntchito, kapena kuchita ntchito zowapindulira. Izi nzosatheka m'mayiko opanda ufulu. Ntchito zam'boma zimapezeka kwa okhawa okonda chipani cholamula, kapena kwa abwenzi ndi ogwirizana ndi olamula. Lamulo, kapena kukondera, kutha kuletsa akazi, mtundu wina wa anthu ochepa kapena magulu ena kugwira ntchito zina. Anthu amtundu wina kapena gulu lina akhoza kungopatsidwa ntchito zonyozeka zokha. Nzika zamayiko ena zitha kuletsedwa kukhazikitsa bizinezi, ngakhale kutsegulitsa buku laku banki.

Ngakhale kwa womwe angapeze ntchito, kusiyanaku kumakhala-pobe. Mwachitsanzo, ku Soviet Moscow, nthambi ya sitolo ya GUM ku Red Square ankangolola alendo achuma komanso akuluakulu a zipani zandale okhaokha. Akuluakulu a zipani zandale okha ankakonda kuyendera magalimoto apamwamba a mtundu wa *Zil limousine* – magalimoto ankaima kupereka mpata kuti adutse - kapena kukasangalala mwezi wathunthu kumalo achilengedwe. Malo abwino komanso opumulira kumapeto kwa sabata ankaperekedwa ndi audindo, omwe amakondera anzawo powapatsa nyumba zabwino.

Nzonsezi ndi kusiyana kosathawika: omwe amapwetekeka ndi oti mwina mwayi ovota kapena kukopa anthu kuti asinthe malamulo

Maziko a dziko la ufulu

alibe. Mosiyana ndi izi, anthu onse a m'dziko la ufulu ali ndi mwayi ofuna ntchito yabwino kapena kuyamba bizinezi ndi kupeza chuma. Onse akhoza osakwanitsa, koma palibe yemwe amawaletsa.

Mitundu ya kufanana

Kufanana mu dziko la ufulu sinkhani yopereka chuma mofanana kapena kakhalidwe ka moyo kofanana. Ndi kuonetsetsa kuti aliyense akuthandizidwa mofanana.

Izi zimaonekera zokha munjira zinayi.¹⁵Nzika za dziko la ufulu zili ndi kufanana pamakhalidwe: onse ali ndi mwayi ofanana opanga chisankho paokha ndi kuthandizidwa moyenera komanso kulemekezedwa ndi ena. Palinso kufanana pa lamulo: lamulo limateteza ndi kuwatumikira mofanana mosayang'anira mtundu, chipembedzo, kuti ndiwamwamuna kapena wamkazi, chuma kapena banja lomwe akuchokera. Amafafana pa ndale: onse atha kuvotera komanso kuimira pa mpando wandale. Ndipo ali ndi kusasiyana popeza mwayi: palibe zoletsa zoikapo dala popeza mwayi wa ntchito kapena sukulu kapena chilichonse chowatukula pa moyo wawo.

Kufanana pa makhalidwe

Mu dziko la ufulu, anthu amaganiziridwa ndi kulemekezedwa mofanana. Onse ali ndi ufulu wofanana wopanga zisankho zokhudza miyoyo yawo, pokhapokha ngati sakupweteka ena pakutero.

Ganizoli limachokera pa chikhulupiriro chawo chozama chokhudza mmene analengedwera ngati anthu. Chilengedwe chomwe tonsefe timagawana. Tonse timafuna kupanga zisankho, mosatengera mtundu wathu, chipembedzo kapena kuti ndife mwamuna kapena mkazi; ndipo tonse timafuna ena alemekeze ufulu wathu pochita izi. Lamulo mu dziko la ufulu ndiloti 'chita monga m'mene ungafunire ena akuchitire'.

¹⁵ A gowod outline of these points can be found in Nigel Ashford's Principles for a Free Society, Jarl Hjalmarson Foundation, Stockholm, 2003.

Maziko a dziko la ufulu

Izi sizikunena kuti anthu ndiwofanana mmakhalidwe pa zopanga zawo. Omwe amapweteka kapena kubera ena samachita bwino. Anthu ena amaphwanya mwadala malamulo akakhalidwe ka anthu kapena okhudza kugonana. Koma miyoyo yawo imakhalabe yofunika. Kuphwanya kwawo kwa lamulo kapena kulakwitsa kwawo ndikongofunika chilango kapena chidzudzulo choyenerera ndi kulakwa kwawo. Koma izi sizikuwapangitsa kuti azunzidwe mopzyola muyeso kapena kuchititsidwa manyazi.

Kufanana pa lamulo

Lamulo mu dziko la ufulu limateteza ndi kulanga mosakondera. Olakwa samalangidwa mosiyana ndi apolisi, akhoti kapena andende potengera makhalidwe ake ena omwe akusiyana ndi mlandu wake monga chuma, ubale, gulu lochokera, potengera kuti ndi wamwamuna kapena wamkazi, chipembedzo, kapena mtundu. Nzika sizingangomangidwa kapena kuzunzidwa mopanda chifukwa kaamba kakuti adindo amadana nawo. Aliyense ali ndi mwayi wofanana wopeza chilungamo ngati waberedwa kapena wapwetekedwa ndi ena, posatengera kuti iye ndi ndani komanso kuti alakwawo ndi odziwika bwanji.

Mu zosema zopezeka m'nyumba za makhoti odziwika bwino adziko lapansi, chilungamo chimaonetsedwa ngati kunyamula sikelo kudzanja limodzi komanso lupanga mbali inayi. Koma chinthu chofunikira kwambiri nchakuti, chosemacho ndichophimbidwa kumaso. M'dziko la ufulu, chilungamo sichiona chilichonse kupatula mfundo zofunika pa mlandu uliwonse.

Kufanana pa ndale

Kufanana kwina komwe kumachokera ku chilengedwe cha munthu ngati anthu ndi kufanana pa ndale. Zofuna za aliyense ndi maganizo ake zimakhala zofunika kuziganizira. Kotero aliyense mu dziko la ufulu ali ndi ufulu ovota pa zisankho kapena riferendamu, ndipo palibe amene amaponya mavoti ochuluka kuposa imodzi. Izi zimathandizira kuti zofuna za aliyense zitsatidwe ndi oimirakomanso ndi omwe asankhidwa.

Maziko a dziko la ufulu

Pali zoletsa zochepa. Sitimawalola ana kuvota, pokhulupirira kuti sanakhwime nzeru kuti angaganize zanzeru m'mene iwo ndi ena akuyenera kulamuliridwa. Chimodzimodzi, anthu omwe ali ndi vuto la misala athanso kuikidwa mugulu losayenera kuvota: koma vuto ili liyenera kuunikidwa mwapadera kupewa olamula kuwachotsa otsutsana nawo pazifukwa zoterezi.

Pali maganizo osiyana pa nkhani yoti mbava zomwe zamangidwa ziziloledwa kuvota. M'mayiko ena, anthu omwe ali m'ndende sakhala ndi ufulu wovota, poyang'anira kuti munthu yemwe anaswa malamulo sakuyenera kutenga nawo mbali mu ntchito yowapanga. M'mayiko ena, okhawo omwe analakwa milandu ikuluikulu saloledwa. Koma m'mayiko ena, mbava zimakhala ndi ufulu wonse wovota potengera chilengedwe chomwe timagawana nawo cha umunthu.

Mfundo ya kufanana pandale imatanthauza kuti akazi ayenera kuvota mmene achitira amuna – ngakhale m'mayiko ena a ufulu, ufuluwu wavomerezedwa muzaka zosapsyola zana zapitazo. Dziko la New Zealand lidali dziko loyamba, kupereka ufulu ovota kwa amayi m'chaka cha 1893. Dziko la Australia linachitanso chimodzimodzi m'chaka cha 1902, ngakhale zolepheretsa zinkapitirira kukhalapo kwa gulu la amayi omwe anali eni nthaka m'dzikolo mpaka mchaka cha 1962. Mayiko ambiri aku Ulaya anayamba kulola amayi kuvota itangotha nkhondo yoyamba yapadziko lonse lapansi, ngakhale ku France anachedwerapo kufikira m'chaka cha 1944 ndipo ku Switzerland chinali chaka cha 1971.

Choletsa chilichonse pa ufulu ovota chiyenera kuchepetsedwa kwambiri. Nkosavuta kwa olamulira m'mayiko opanda ufulu kukaniza adani awo kuvota powaponya mundende kapena kuwanena kuti ndiamisala, kapena kupereka zifukwa zosiyanasiyana zoletsa. Uku ndiko kugwiritsa ntchito ulamuliro molakwika.

Ngati zili zotheka, voti ya aliyense iyenera kukhala ndi mphamvu yofanana. Mwachitsanzo, payenera kukhala mlingo wofanana wa osankha mu dera lililonse lochitira chisankho mmene oimirira

amasankhidwa. Maboma aakulu atha kutanthauza kuti ovota aliyense ali ndi mphamvu yochepa pa zotsatira. Zifukwa zokhalira ndi maboma osiyana makulidwe ndi mmene deralo lilili potengera zachilengedwe zopezekamo. Malire a madera azisankho ayenera kusankhidwa ndi anthu oima pawokha poopa kuti angaikidwe mokondera zipani zolamula.

Motsagana ndi ufulu ovota, aliyense ali ndi ufulu opikisana nawo ndi kukhala pa udindo uliwonse. Palibe mipando mu Nyumba ya Malamulo yomwe inapangidwira omwe ndi amuna kapena akazi, mtundu kapena achipembedzo chapadera. Dongosolo loyendetsera zisankho liyenera kuteteza kufanana kumeneko, mwachitsanzo, poonetsetsa kuti aliyense ali ndi ufulu oimirira pa mpando osaopa kuopsezewa – makamaka ndi andale a mbali yolamula. Zomwe zikutanthauza kuti ayenera kuledwa kukopa anthu ndi kuyankhula, kusindikiza ndi kuulutsa maganizo awo ndi kudzudzula opikisana nawo komanso malamulo. Masankho ayenera kukhala mpikisano wa mfundo, ndipo sipangakhale masankho a ufulu ngati maganizo ndi ufulu wolankhula zikuponderezedwa. M'mayiko ena opanda ufulu, ndi mlandu wawukulu kudzudzula boma; pomwe m'mayiko a ufulu kudzudzula koterokoyenerera m'moyo watsiku ndi tsiku wandale.

Kufanana pa mwayi

Kufanana pa mwayi kukutanthauza kuti munthu asaletsedwe mwadala kukwaniritsa zokhumba zake, m'maphunziro, pantchito, kapena mbali iliyonse yamoyo wake. Mwachitsanzo, mtundu wawo usawalepheretse kupeza malo pa sukulu kapena mu timu yamasewero. Chipani chawo kapena kukhala wamwamuna kapena wamkazi kusawalepheretse kupeza mwayi wantchito. Ngakhale kusauka kwawo kapena kochokera kwawo kusawalepheretse kukwatira munthu osiyana nawo.

Izi sizikutanthauza kuti sukulu kapena olemba ntchito atenge kapena alembe aliyense mosayang'anira zowayenereza zawo. Sukulu itha kulola okhawa omwe akhonza mayeso, ndipo olemba ntchito amafuna umboni komanso ukadaulo. Mzimayi womasuka sangangokwatiwa

Maziko a dziko la ufulu

ndi mwamuna chifukwa mwamunayo wamukonda ayi. Kufanana pa mwayi kukutanthauza kuti palibe choletsa chilichonse chaikidwa pamunthu, komanso kuti sali okakamizidwa kuchita chomwe saku-funa. Mwachitsanzo, maukwati osankhiridwa ndi ena alipo m'zikhaliidwe zambiri ndipo ndiololedwa m'dziko la ufulu ngati eni akewo avomereza. Koma munthu sangakakamizidwe kukwatira asakufuna, ngakhale makolo awo atafunitsitsa. M'dziko la ufulu, munthu yemwe ndiwoyenera kukwatira amatengedwa kukhala oyenera kudzi-sankhira yekha. Monga mgwirizano uliwonse, ukwati sumatheka ngati m'modzi mwa anthuwo waumirizidwa kulowa m'banja.

Ngakhale anthu sakuyenera kukhala ndi zowapinga popanga zisankho zawo, pali zina zachibadwa zomwe zimawasiyanitsa anthuwa. Munthu yemwe anabadwa osamva sangakwanitse kukhala olemba nyimbo kapena otsogolera anzake kuimba (ngakhale Beethoven anakwanitsa patapita nthawi). Munthu opanda miyendo sangafune kumakwera mapiri. Ndipo ana amakhala ndi poyambira posiyana motengera ndi banja lomwe akuchokera: makolo ena atha kukwanitsa kumugulira mwana wawo mabuku ndikumuthandiza ntchito yaku sukulu pamene ena atha kunyalanyaza.

Anthu ena am'mayiko aku Ulaya amati, ngakhale ana ali ndi chiyambi chosiyana m'moyo, sukulu ziyenera kuonetsetsa kuti anawa akafikire mlingo wofanana munthawi yomwe atadzakule ndi kuyamba ntchito. Motero sukulu zimayesetsa kupereka maphunziro okwanira, ndi 'ku-wabweza' ana nzeru kusiyana ndikukangowafikitsa kumathero awo. Koma zoonadi zake, sitingakwanitse kufananitsa zomwe zinasiyana pachibadwa – ndipo njira yokhayo yofananitsa kusiyanaku ingakhale maloto chabe imene ingafune boma kuti litenge anawa akangobadwa kumene ndikuwalera mofanana.

Funso: anthu osauka alibe ufulu ogula galimoto zapamwamba za mtundu wa limousines, ndichonchodi?

Eya, ndichonchodi. M'dziko la ufulu, aliyense ali ndi ufulu wogula katundu wapamwamba, ngakhale ndiwochepa okha omwe angakwanitse. Ndinkhani ya ndalama, osati ufulu; anthu

osauka alibe ndalama yogulira galimoto zapamwamba, koma palibe munthu aliyense kapena waudindo angawaletse. Aliyense atha kufuna atakhala ndi katundu wapamwamba, pogwira ntchito molimbika kuti apeze ndalama, posunga ndalama kapena kubwereka.

Kumbukirani kuti mabanja osauka am'mayiko achuma kwa-mbiri ndi a ufulu pano, ali ndi mwayi osangalala ndi kutentha mnyumba zawo, magetsi ndi madzi abwino zomwe zinali zinthu zapamwamba zaka zochepa zapitazo. Mosiyanita, m'mayiko opanda ufulu, anthu sangafune kukhala ndi zinthu monga nyumba yayikulu kapena minda yachonde pokhapokha adindo awapatse izi.

Tsankho labwino

Mayiko ena ayesera kufananitsa kusiyana kwachibadwidwe, ndikuthetsa kukondera, pokhala ndi mapologalamu a tsankho labwino. Izi zitha kungokhudza mchitidwe wofikira magulu a anthu ochepa omwe samaganizira kuti atha kukhala ndi mwayi wa zinthu zina – Mwachitsanzo, ana anzeru koma osauka, omwe sangalingalire zofunsira malo ku sukulu zaukachenjede zapamwamba – ndi kuwalimbikitsa kuti ayesere. Kuwafikira ndi kuwalimbikitsa uku sikoletsedwa, chifukwa kumangowonjezera mwayi omwe ulipo kwa magulu amenewa.

Koma tsankho labwino litha kukhalanso munjira yopereka mwayi kwa magulu a anthu ochepa – monga kuika ndondomeko zokakamiza sukulu ndi olemba ntchito kuti atenge gulu la anthu ochepawa. Izi zitha kuthandiza kufikira mlingo winawake: ndithudi, tsankho labwinoli mu dziko la United States mu zaka zam'ma 1960 kupitirira mtsogolo linathandiza anthu okuda kuonetsa kuthekera kwawo mu sukulu komanso pa ntchito zomwe zinachotsa chitonzo chomwe azungu amakhala nacho pa iwo. Koma tsankho labwinoli siligwirizana ndi dziko la ufulu. Ngakhale lingathandize kuchotsa chitonzo ndi kupititsa patsogolo ufulu, limakondera gulu lina la anthu ena m'malo mowathandiza mofanana.

Maziko a dziko la ufulu

Anthu ena amagwirizana ndi kukondera ndi kuthandizira magulu ena pofuna kukonza tsankho loipa lomwe linalipo kalelo. Koma chapita, chapita, tsankho lokondera anthu ena lero silingachotse kulakwiridwa kwa anthu ena am’gulu la anthu ochepa omwe anapwetekedwa m’mbuyomo. Ndipo mfundoyi itha kuoneka yolakwika kwa anthu ochuluka, omwe akuyenera kufikira mlingo wawukulu kuti apeze mwayi ofanana wa sukulu kapena ntchito. Anthu am’gulu lochepa akhoza kuyamba kutengedwa ngati gulu latsopano lokonderedwa, ndipo pakhoza kukhala mkwiyo wobwezerana ngakhale ziwawa zimene zosagwirizana ndi mfundoyi komanso anthu ochepa omwe akupindula nayo.

Tsankho loipa

Kunena chilungamo, tsankho silikhalapo nthawi zonse kuti lithandize magulu a anthu ochepa. Nthawi zambiri, tsankho limakhala anthu ochuluka kudzipatsa okha ufulu, mwayi ndi zokhumba zomwe sizingapezeke kwa magulu a anthu ochepa. Zitsanzo zodziwika bwino ndi ku dziko la Malaysia ndi South Africa, koma dziko lapansi lili ndi nkhani zambiri zokhudza lamulo kupondereza magulu a anthu ochepa chifukwa cha mtundu, chipembedzo, chiyankhulo, chibadwidwe pankhani ya kugonana kapena maganizo awo pandale.

Mobwereza, tsankho lotero sililoledwa m’dziko la ufulu: m’dziko la ufulu, anthu onse amafanana pa lamulo ndipo palibe gulu lomwe lingadzimatse mwayi wapadera. Nthawi zambiri tsankholi lafika pokhala mchitidwe wozunza magulu a anthu ochepa. Akalandidwa ufulu omwe anthu ambiri akusangalala nawo, magulu a anthu ochepa alibe mwayi odzitukula okha. Atha kufika pomaoneka ngati anthu otsalira kapena osakwanira kukhala anthu. Ndipo pamene umunthu wawo wachotsedwa, palibe malire achitonzo ndi kuzunzidwa komwe angakumane nako.

Kufanana pa zotsatira

Anthu ambiri akamakamba za kufanana, samatanthauza ufulu othandizidwa mofanana pansu pa mfundo za kufanana pa makhalidwe, kufanana pa lamulo, kufanana pa ndale kapena kufanana pa mwayi.

Amatanthauza kufanana pa kupeza kwa zinthu monga chuma, ndalama komanso mlingo wa kakhalidwe ka moyo. Ndipo ambiri amalimbikitsa kugawanso kuchokera kwa olemera kupita kwa osauka pofuna kufananitsa zotsatirazi.

Chiwerengero cha kusiyana pachuma

Anthu omwe amalimbikitsa kufanana pa zotsatira nthawi zambiri amagwiritsa ntchito chiwerengero chotchchedwa '*Gini coefficient*' chomwe chinatchulidwa potengera dzina la katswiri wa zowerengera komanso za umoyo wa anthu waku Italy, *Corrado Gini*. Ndi njira yoyezera mlingo wakusiyana pa chuma. Ngati pali 0 zikutanthauza pali kufanana ndipo ngati pali 1 zikutanthauza pali kusiyana (ngati pamene munthu m'modzi ali ndi chuma chonse).

Mabungwe akuluakulu osiyanasiyana monga *World Bank* ndi *US Central Intelligence Agency* amayesera kuyeza mlingowu m'mayiko osiyanasiyana ndikuwaika pa mndandanda molingana ndi kusiyana kwawo. Mndandandawu umapenekera kuti mayiko ambiri otsogola ali ndi mlingo wochokera pa 0.25 kufikira 0.5 – kutanthauza kufanana kwakukulu. Kusiyana kwakukulu kumaonekera m'mayiko aku Africa, motsogozedwa ndi dziko la South Africa lomwe mlingo wake unafika pa 0.7

Tikhoza kukhalabe okayikira kawerengedwe kotere, komanso ganizo lakuti chuma cha m'mayiko omwe ali ndi mlingo wokwera chiyenera kufananizidwa mokakamiza. Choyamba, mayiko ochepa ali ndi mndandanda wokwanira wokhudza chuma, zomwe zikupangitsa njira ya *Gini coefficient* kukhala yosadalirika (chomwe chitha kukhala chifukwa chimene mabungwe osiyanasiyana amapeza zotsatira zosiyana). Chachiwiri, kusiyana kwakukulu pa chuma kutha kuonetsa kusiyana kwa magulu a anthu komwe kuli kwabwino. Kutha kusonyeza kutukuka pa nkhani za luso lamakono, kupita patsogolo kwa m'mizinda komwe sikunafikire madera akutali. Sizingakhale zanzeru kuletsa kutukuka kumeneku pochepetsa chuma cha katswiri wa za makompyuta m'mizinda pofuna kupatsa alimi a mbewu zapakhomo. Koma mmalo mwake chumachi chikhale

Maziko a dziko la ufulu

chofikirika kuti osauka agawane nawo kuchita bwino pochotsa zotchinga (monga ziletso pa mayendedwe) zimene zimawalepheretsa kuchita izi.

Vuto lina la njira ya chiwerengerochi ndilakuti limafananitsa chuma chosaukira chabe, osawerengera misonkho yomwe anthu akupereka ndi phindu lochoka ku boma (umoyo wa anthu, penshoni, chithandizo cha chipatala chaulere ndi zina zosamalira umoyo) lomwe amalandira. Kungotenga njira ya chiwerengero yosiyana yaku United Kingdom yokha, chuma chosaunikira chabe cha anthu khumi pa anthu zana aliwonse achuma chimachulukira makumi atatu kuposa anthu khumi pa anthu zana lililonse osauka, zomwe zikuonetsa kusiyana kwakukulu. Koma anthuwa akalipira misonkho yawo ndikulandira phindu lawo losiyanasiyana kuchokera ku boma mlingowo umatsikako kufikira kasanu ndi kamodzi. Anthu amagwiritsabe ntchito chiwerengero choyambirirachi kuti akwaniritse mfundo yogawanso chuma, koma uku ndi kugwiritsa ntchito njira chiwerengeroyi mwachinyengo.

Kufanana pa ndalama zolandiridwa kapena chuma?

Ganizo lakuti anthu apindule mofanana potenga nawo mbali muzochitika zam'dera limatchedwa *egalitarianism*. Koma kutha kukhala kovuta kufikira tanthauzo lake lenileni la mawuwa, mwina chifukwa cha kudzitsutsa kwake komwe.

Anthu okamba za kusakonderaku atha kukhala osamvetsetseka pa mfundo yeniyeni ngati akufuna kufanana pa ndalama zolandiridwa – kapena pa chuma. Ngati akutanthauza kuti ndalama zikhale zofanana, ayenera kuvomereza kuti kusiyana kwakukulu pachuma kungoyenera kuonekerabe. Munthu wina atha kusungira ndalama zake ndikuika mu chinthu chodzamuthandiza mtsogolo ndi kupeza mpamba komanso chuma, pamene wina ndalama yomweyo atha kuipangira juga kapena kungoiwonongera pazomwe zingamukondweretse nthawi yomweyo. Mosadutsa nthawi yayitali, chuma chawo chikhala chosiyana kwambiri.

Komanso, ngati ntchito zonse zingalipire mofanana, anthu ambiri atha kufuna ntchito zooneka zosavuta komanso zabwino ndipo patha kusowa anthu ogwira ntchito zovuta komanso zosasangalatsa. Avutikirenji munthu kulimbikira ntchito pamene malipiro ake ndiwofanana ndiyemwe akugwira ntchito mwaulesi?

Palinso zina zambiri zokhudza ntchito kuposa kulandira zinthu. Pali zomwe akatswiri pa kayendetsedwe ka chuma amati *ndalama za m'maganizo* – kukhala ndi ogwira nawo ntchito amene mumagwirizana, mwachitsanzo, kugwira ntchito mbali yabwino yadziko kapena yosavuta kufika ndi yokhala ndi zoyenereza zambiri mumzindamo. Izi ndizabwino kwa womwe akusangalala nazo, koma sizinthu zoti zingafananizidwe kwa aliyense.

Ngati, mbali inayi, anthu ofuna kusakondera akutanthauza kuti chuma chifananizidwe, patha kukhalabe kusiyana kwakulu pa ndalama, kutengera kuthekera ndi luso la ogwira ntchito komanso m'mene olemba ntchito akuwafunira. Ngati anthu ena anasunga ndi kuwonjezera pa chuma chawo, pamene ena anagwiritsa ntchito ndi kuchepetsa, chuma chawo mosakhalitsa chiyamba kusiyana. Ndiye titani? Wilfred Pickles, muulutsi wa pologalamu yotchuka ya *'Have a Go'*, pa wailesi ku UK mzaka za mma 1950, ankayamba pofunsa opikisana za iwo komanso zokhumba zawo. Wina anati: 'chokhumba changa ndikutenga ndalama zonse padziko lapansi ndikuzigawa mofanana kwa wina aliyense'. Anthu anakondwera kwambiri ndi mawu achifundowa. Mwatsoka, munthuyu anawononga zonse powonjezera kuti: 'ndipo ndikadzamaliza gawo langa tidzagawananso. Mu dziko loti likusinthasintha nkovuta kuti chuma chonse chifanane.

Zotsatira zofanana, kaya ndi ndalama kapena chuma, sizachilengedwe komanso sizokhazikika. Kufananitsa chimodzi mwayicho, ndikuziika kukhalabe zofanana, kukhoza kufuna kuphwanya kwakukulu ufulu komanso kuwononga katundu. Zikhoza kukhudza kulanda chuma moopseza kwa ena n'kuchipereka kwa ena – ndipo izi zizayenera kuchitikachitika kuti zinthu ziyandikire pofanana.

Maziko a dziko la ufulu

Chuma china ndi chosatheka kuchilekanitsa ndi kuchigawanso: fakitole yayikulu yopanga zinthu ikhoza kugawidwa mmagawo ake komanso potengera magawo a makina, koma sangapangenso kanthu. Siingathekenso kuigulitsa kuti ndalamayo igawidwe – mudziko lokhala ndi chuma chofanana, palibe munthu mmodzi angakhale ndi kuthekera koigula.

Mfundo zogawanso zotero zikhoza kukhala zokakamiza komanso zosakwanira. Zitha kumana anthu kupeza phindu la thukuta lawo ndi kuchotsa chilakolako cholimbikira ntchito ndi kusunga ndalama. Akhoza kuwononga chuma mmalo mochigawanso. Ndipo zitha kufuna ulamuliro wa mphamvu kwambiri kuti zikwaniritsidwe – zomwe zosagwirizana ndi dziko la ufulu.

Njira zogawiranso

Vuto lina ndilosankha kuti ndi ndani yemwe akuyenera kukhala nawo mu dongosolo logawanso. Nthawi zambiri, anthu ofuna kusakondera m'mayiko achuma amaika pempho lawo kwa nzika zawo, kapena mayiko ofananirapo zochitika. Chifukwa kugawa ndalama kapena chuma mofanana dziko lonse lapansi kutha kutanthauza (ngakhale zitakhala zotheka) kusaukitsa kakhaliidwe ka anthu m'mayiko achuma. Ndi mfundo yoti siingavomeredwe mwamtendere.

Mosiyanita *Egalitarians* m'mayiko osauka, amakhala ndi masomphe-nya adziko lonse lapansi lofanana: kugawana chuma cha m'mayiko onse olemera, amati kukhoza kusintha kwambiri miyoyo ya anthu awo osauka. Koma ili ndi loto losatheka chifukwa mayiko achuma sangagwirizane nazo.

Komanso kugawana uku sikungapereke chuma chokhazikika kwa anthu osauka. Chuma sichipezeka polanda chamnzako. Palibe mlingo okhazikika wa chuma omwe ungapangitse munthu kulemera posaukitsa wina. Chuma chimapangidwa kudzera mu ukadaulo opanga zinthu, malonda, ndi kukhala ndi mpamba. Powononga mpamba wa omwe alinawo sizingathandize omwe alibe. Mfundo yabwino ndiyokonza zomwe zimabwezeretsa m'mbuyo, monga nkondo ndi umbava, zomwe sizilimbikitsa anthu m'mayiko osauka kukhala ndi mpamba wawo.

Mafunso okhudza chomwe chikuyenera kugawidwa, kupita kwa ndani komanso kuchokera kwa ndani, akuonetseratu kuti sipangakhale mgwirizano weniweni wa m'mene mfundoyi ingakhali. Ndipo kuti kugawanaku kugwire, payenera kukhala ndondomeko yabwino, yomwe aliyense ayenera kutsatira. Popanda mgwirizano, njira yokhayo yomwe ingatheke ndi kugwiritsa ntchito mphamvu.

Kukakamizika kuvomereza kufanana pa chuma kutha kupha mfundo yakuti aliyense azilimbikira kufuna chinthu chabwino. Popeza katundu aliyense ungamupeze mu ukadaulo wako, malonda kapena kulimbikira kugwira ntchito atha kudzalandidwa, ndani angalimbikire kuti apeze chinthu? Ndipo pali kuluza kwambiri kwa anthu apa. Malonda ndi luso: anthu kuyesera kupanga katundu wabwino ndi tchito zabwino pofuna kukhala ndi katundu watsopano, dongosolo lochitira ndi luso lamakono zomwe zimapititsa patsogolo miyoyo ya wina aliyense. Polowetsa panso ntchito za malonda ndi luso lopanga zinthu lotero, mfundo zolimbikitsa kuti anthu ndi ofanana ndipo ayenera kukhala ndi mwayi wofanana zimapha kuthekera pa zinthu za m'miyoyo ya anthu pa dziko lonse lapansi.

Kufanana ndi chilungamo

Matanthauzo awiri a chilungamo

Anthu ochuluka omwe amagwirizana ndi mfundo yogawananso chuma kapena ndalama amati ndi 'kusowa kwa chilungamo' kuti anthu ena ndiwolemera kuposa ena – ndipo ochepa atha kukhala olemera kwambiri kuposa osaukitsitsa. Kusowa 'chilungamo pakati pa anthu' kumeneku kumawonjezerekanso ndi nkhani yakuti chuma cha anthu sichimasonyeza kwenikweni kufunikira kwa munthu m'dera.

Ganizo limeneli limapondereza liwu la chilungamo, – lomwe tonse timavomereza kuti ndi chinthu chabwino komanso chofunikira ndi choyenera munthu aliyense wa ife – ndi kuchipatsa tanthauzo losiyani-ranatu, la kufanana ndi kusakondera.

Maziko a dziko la ufulu

Tanthauzo lenileni la chilungamo limakhudza khalidwe lomwe timaliyembekezera kuchoka kwa wina ndi mnzake. Ngati wina waphwanya mgwirizano kapena waba, timati sanachite chilungamo, chifukwa khalidwe limeneli ndilosaloledwa potengera pa mfundo yosapwetekana komanso pa malamulo athu ndi makhalidwe ovomerezeka. Mwanjira ina, tanthauzo la chilungamoli, lotchedwa chilungamo pa migwirizano, limakhudza mmene anthu ayenera kukhalira. Limagwira ntchito pomwe anthu achita mwadala. Ngati wina watenga chimfine kapena walumala, ndi tsoka, koma osati kusowa kwa chilungamo, chifukwa palibe yemwe wachita mopanda chilungamo.

Kagwiritsidwe ntchito ka liwu la ‘chilungamo’, nthawi zina kotchedwa chilungamo cha kagawidwe, sikokhudza m’chitidwe pakati pa anthu, koma kagawidwe ka zinthu pakati pawo. Ngakhale m’mayiko a ufulu, kagawidwe kachuma kapena ndalama zolandiridwa komwe kamakhalapo ndi zotsatira chabe za kudzipereka pa ntchito zachuma m’mene aliyense amatsata malamulo komanso makhalidwe ovomezezeka. Sitinganene kuti ndi ‘kusowa kwa chilungamo’ chifukwa palibe aliyense wachita mopanda chilungamo. Palibe anafuna zotsatirazi; ndi mmene zikuyenera kuchitikira mmoyo¹⁶.

Kufunikira ku dera

Kugwiritsa ntchito kwa mawu oti ‘chilungamo pakati pa anthu’ kumalakwitsa posonyeza dera ngati munthu yemwe amasankha ndondomeko ya m’mene chuma ndi ndalama zikuyenera kuyendera. Koma dera lilibe chifuniro pa ilo lokha: ndi anthu okha omwe angapange zisankho ndi kuchitapo kanthu. Ndipo anthu amatsutsa mwamphamvu pa mfundo za chuma komanso dera. Chifukwa chimodzi chomwe anthu ambiri amakondera ganizo la ‘chilungamo pakati pa anthu’ ndichakuti silimveka bwino nkomwe zokhudza zotsatira zenizeni, ndipo limaonekera kwambiri pa kusagwirizanaku.

Tikati titambasule m’mene kugawana phindu ‘mwachilungamo pakati pa anthu’ kumakhalira, kuthekera kolephera kufika pa

¹⁶ This and the following points are well made in F. A. Hayek, *The Mirage of Social Justice*, University of Chicago Press, Chicago, IL, 1978.

mgwirizano weniweni kumaonekeratu. Anthu ambiri amagwirizana kuti kufanana pa ndalama sicholinga chenicheni, chifukwa anthu azi-pindula mofanana posatengera ulesi kapena kusokoneza kwawo. Kunena mosapsatira, palibe amakolola asanalime. Choncho anthu ambiri amati, m'malo mofananiza, phindu liyenera kuperekedwa kwa munthu potengera 'kufunikira kudera'.

Koma akuyenera kusankha kufunika kwa munthu m'dera ndindani? Dera simunthu, ndipo ndilosafunikira palokha. Anthu sangapereke kufunikira pa chinthu chomwe chilibe zofunikira pachokha. Ndi anthu okha ali ndi zofunikira, ndipo zofunikirazi zimasiyana kwambiri komanso kawirikawiri zimatsutsana. Gulu lina la anthu litha kuona kufunikira kwa osewera nkhonya, pamene ena atha kuyamikira oimba zeze; nzosatheka kunena yemwe akupereka 'kufunikira kwambiri' m'dera chifukwa kusangalala kwa anthu osiyana sikungafananizidwe. Kodi tingasankhe bwanji (kufunikira kwa kudera) kwa namwino, wokupha nyama, wokumba miyala ya malasha, oweruza milandu, ogwira ntchito zomira panyanja, otolera msonkho, katswiri yemwe wapeza mankhwala opulumutsa moyo kapena katswiri wa masamu?

Kugawa potengera oyenera

Ganizo lina la anthu okhulupirira kuti anthu ndi ofanana choncho ayenera kukhala ndi mwayinso wofanana ndilakuti phindu lidziperekedwa kwa yemwe 'akuyenera'. Komabe, palibe njira yosakondera yosankhira 'oyenera' weniweni pakati pa anthu osiyana ndi m'mene akuyenera kupatsidwira. Anthu osiyana atha kukhala ndi maganizo osiyana poyang'anira ubwino wosiyanasiyana wa zomwe zikuyenera kuunikidwa.

Ngakhale izi zili chonchi pali nkhani zenizeni zofunika poganizira kuti kuyeneraku kukhale kotani. Kodi kuyenera kwa munthu yemwe wagwira ntchito zaka zambiri koma walephera kuyamikiridwa, pamene wina yemwe wabweretsa chofunika kwa mamiliyoni akanidwe chifukwa zangochitika mwa mwayi? Sitikufuna kulimbikitsa kugwira ntchito pachabe: kutukuka pachuma ndiko kukweza

Maziko a dziko la ufulu

kufunikira kwa zomwe timapanga ndi mphamvu zomwe tikuikamo. Kuthokoza anthu potengera m'mene adziperekera kutha kungolimbikitsa mchitidwe wa kudzipereka, osati kuthandiza ena. Palibe ndo-ndomeko ya chuma yomwe ingatsatire mfundo imeneyi.

Phindu lopezeka pa misika silimagwirizana ndi kuyenerera kwa opanga katundu, kapena nthawi ndi mphamvu zomwe agwiritsa pobweretsa katundu ndi zinthu zawo kumsika. Sizimatengera kaya kuti katundu wawo anatenga zaka ndi ndalama zambiri kapena anangopezeka mwamwayi. Koma phindu lopezeka pa misika limagwirizana ndi chisangalalo komanso kufunikira komwe anthuwa amapereka kwa ena. Makasitomala amagula katundu ndi zinthu kwa ogulitsa chifukwa amaona kufunikira kwa katunduyo. Muganizo ili, phindu lopezeka pa misika limatengera kufunika komwe anthu amapereka kwa anthu ena m'dera. Limaonetseranso kusowa ndi luso la ogulitsa, chiwerengero cha makasitomala omwe akufuna zinthu ndi kufunikira kapena changu chake zomwe ogula amaziona.

Kugawa potengera chosowekera

Ganizo lina la anthu okhulupirira kuti anthu ndi ofanana choncho ayenera kukhala ndi mwayinso wofanana ndilakuti zinthuzi zizigawidwa potengera chosowekera. Komano, ndindani anganene kuti 'chosowekera' ndi ichi? Palibe chodziwikiratu chomwe chingasiyanitse anthu osowa ndi osasowa. Zomwe anthu akukumana nazo ndizosiyana: ali ndi chuma ndi ndalama zosiyana, koma izi zitha kusinthasintha kwambiri. Amakhalanso malo abwino kapena osakhala bwino, ali ndi kuthekera komanso kaganizidwe kosiyana, ndipo amagwira ntchito ndi anthu osiyanasiyana mu ntchito zosiyanasiyana. Phindu losakhudza chuma limeneli monga ntchito yomwe umayikonda ndi anthu ochezeka ogwira nawo ntchito ndilovuta kuliwerengetsera.

Kuti anthu ndiwosowa kapena ayi, ndi nkhani yopanga chiganizo, ndipo anthu osiyana atha kuyiunguza mosiyana. Kugawanso zinthu potengera kusowa kukanakhala kotheka ngati andale ena akanapatsidwa mphamvu yoono kuti chosowa ndi chani ndi kuchitapo

kanthu. Koma anthu m'mayiko a ufulu sangavomere kupereka mphamvuzi kwa wandale aliyense. Zikhoza kukhala mphamvu zonse pa miyoyo yawo. Sangakhalenso anthu a ufulu. Akhala akapolo kwa andalewo.

Komanso sikuti kupezeka kwa chosowa kungabweretse udindo pa ena. Munthu yemwe ali ndi vuto la impso atha kufuna impso yatso-pano. Koma izi sizikumiriza aliyense kupereka impso yake. Abale atha kuchimva pa umunthu komanso ngati akubanja kuti apereke, anthu ena achilendo atha kupereka pomva chisoni. Koma ichi ndi chisankho chawo. Titha kulimbikitsa ndi kuyamikira m'chitidwewu, koma dziko la ufulu silingakakamize anthu kuti adzipereke kuti athandize ena.

Dziko la ufulu pachuma limagawa zinthu, mosakakamizika, koma potengera kufunika komwe ogula amakuona pa katundu ndi zinthu zosiyanasiyana zomwe zimapezeka pamsika. Ngati anthu angasankhe nsomba zokula mwazokha kusiyana ndi zowetedwa, mwachitsanzo, kapena nsapato m'malo mwa nkhwayira, zimenezo nzomwe zimapangidwa. Ndiponso limagawa zinthu kwa anthu motengera zofuna za anthu zomwe amazionetsera kudzera mu mphatso zachifundo zomwe amapatsa ena. Maganizo awawa amasiyidwa m'manja mwa anthu: ganizo lakuti boma lokha ndilomwe lingadziwe choyenera thandizo limakanidwa mu dziko la ufulu.

Kuwononga kwina kwa chikhulupiro chakuti anthu ayenera kuthandizidwa mofanana

Chotsatira chowononga cha chikhulupiro chakuti anthu ayenera kuthandizidwa mofanana chili pa 'chilungamo pakati pa anthu' ndichakuti chimabisa ganizo ndi choonadi cha chilungamo cha m'dera. Mfundo zomwe zimamanga dziko la ufulu – monga kufanana pa lamulo – zimabisidwa komanso kuchepetsedwa mphamvu ndi tanthauzo latsopanoli. Ndi ganizo la kugawanso, sipangakhale kufanana polandira thandizo: m'malo mothandiza aliyense mofanana, tiyenera kutenga mlingo wosiyana kwa aliyense yemwe akuthandiza ndi kupereka mlingo wosiyana kwa aliyense olandira.

Maziko a dziko la ufulu

Kukhumba katundu kumakhalapo mopitirira

Pamene chilungamo chenicheni chikupezeka kuti chithetse kusa-gwirizana, chilungamo cham’dera chimadzetsa kusagwirizanaku. Pamene boma langoyesera kugawa chuma potengera kuyenera, kapena kusowa, kapena kufunikira kudera, limapezeka likuvutitsidwa ndi magulu ambiri osiyanasiyana, onse kufuna kuti phindu lawo likwere. Pakuti palibe njira yeniyeni yosankhira pakati pawo, kusa-gwirizana pandaleku kumapangitsa zisankho zosaganizira bwino. Ulamuliro wankhanza umayamba kusankha zinthu, zomwe sizigwirizana ndi dziko la ufulu.

Ndipo anthu amayesera kupeza njira zozembera boma mu ndondomekoyi pofuna kudzipindulira iwo eni ndi mabanja awo. Izi nzomwe zinkachitika ku Soviet Union, komwe anthu ambiri ankachita zosavomerezeka pofuna kupititsa patsogolo miyoyo yawo. Kukakamiza kufanana pa katundu kumangosintha anthu otsatira lamulo kukhala dziko la zigawenga.

Udindo wa achuma

Kusiyana pa ndalama zolandiridwa ndi chuma kulinso ndi ubwino wake. Khumbo la anthu lofuna kupeza ndalama zambiri ndikukhala achuma ndi chilimbikitso champhamvu. Chimawapangitsa anthu kusaka ntchito zabwino, kupeza njira zatsopano, kupanga ndi kutumiza katundu wabwino yemwe amatukula miyoyo ya anthu ena. Anthu olemera ali ndi udindo wofunikira woyesera katundu watsopanoyu. Katundu wambiri watsopano amabwera pamsika ngati wosafunikira kwenikweni – popanda msika okhazikika, amapangidwa wochepa, komanso wokwera mtengo. Choncho amagulidwa ndi kuyesedwa ndi anthu achuma. Uthenga wochokera kwa anthuwa umathandiza opanga katunduyu kudziwa mlingo wa kufunikira kwa katunduyu, komwe akufunikira ndi kuona pomwe akuyenera kukonza. Izi zimawathandiza kusiya katundu owonongeka asanayambe kupanga wambiri, ndi kukonza ubwino wa katundu yemwe akupita ku misika ikuluikulu. Pakutero, kuyesera kwa anthu achuma ngati makasitomala oyamba kumathandiza aliyense.

Anthu achuma ndi ndalama zolandiridwa zambiri alinso ndi maudindo ena ofunikira m'dera. Ali ndi zowayenereza kuyesera popereka katundu ndi zinthu zatsopano, zomwe zimachulutsa chisankho ndi kuthandiza dongosolo lopititsa patsogolo zinthu. Atha kukwanitsa kupereka ndalama zawo kupangitsa zaluso, maphunziro ndi kafukufuku yemwe akuona kuti boma sikuikapo chidwi. Kaamba ka chuma chawo akhoza kudzudzula ulamuliro wankhanza pokhazikitsa maganizo atsopano pa ndale amene atsogoleri a boma angamachite nawo mantha. Zonsezi ndi zofunika kuziganizira ngati tikuyenera kusunga dziko la ufulu.

Chiwonongeko cha mpamba

Si munthu aliyense amene angakwanitse kuyang'anira zinthu zofunikira. Omwe amafuna kudzakhala ochita malonda ayenera kutero: ngati akufuna kupanga phindu pa zomwe akupanga, ayenera kudziwa m'mene akuyenera kuthana ndi zovuta ndi kubweretsa pamodzi zinthu zofunikira kuti apange katundu wabwino komanso wotsika mtengo. Koma kugawanso kwa zinthu kukhoza kulanda zinthu m'manja mwa anthu aluso, ndikuchimwaza kwa anthu ena. Zimene zikutanthauza kutaya mpamba ndi kutaya mwayi wopanganso mpamba wina. Koma mpamba ndiwomwe umapangitsa chuma kuchita bwino; ndi katundu opangidwa ochepa, ndi zambiri zogwiritsidwa ntchito, pakapita nthawi nzodziwikiratu kuti chitukuko cham'dera chikuyenera kulowa pansu.

Kusiyanso kumapititsa patsogolo ntchito zachuma. Phindu lambiri lopangidwa ndi ogulitsa limakhala ngati maginito, kukokera anthu ndi zinthu komwe kungapezeke phindu lambiri, ndikuchoka komwe kulibe phindu. Kotero anthu ndi zinthu zimapita komwe zingawonjezere ndalama zamtsogolo. Ndi ndondomeko yopitirira, yosintha-sintha komanso yokulirakulira. Kusiyana komwe anthu amakukana ndi chikoka chomwe chimasuntha anthu ndi katundu kuntchito yopindula, kubweretsa chitukuko paliponse. Ngati tingagawenso zinthu pofuna kufanana, timatchingira mphamvu ya chikoka imeneyo, ndikutaya kufunikira kwamtsogolo, zotsatira ndi kukwera komwe

Maziko a dziko la ufulu

kukanachitika. Ndi anthu ambiri osauka omwe akudalira chuma chomwe chikukwera, ndi iwo amene amavutika kwambiri. Tingachule bwanji izi kuti ndi chilungamo pakati pa anthu?

Msonkho ndi umoyo wa anthu

Kufananitsa chuma kapena ndalama kotheratu kutha kukhala kosatheka, koma maboma ambiri amayesetsa kuyandikirapo, poika misonkho yokwera pa anthu achuma. Koma misonkhoyi itha kukhala yowononga. Pochepetsa phindu pa mabisinesi ndi kulimbikira kwawo, zimabwezeretsa anthu m’mbuyo pa zochita zofunikirazi.–ndi ntchito komanso chitukuko chomwe amapanga.

Kuipa kwina nkwakuti misonkhoyi imaikidwa pa ndalama zomwe anthu asunga komanso mpamba. Misonkho pa ndalama zomwe anthu asunga zimapangitsa anthu kutsala ndi ndalama zochepa zoyambira bizinezi zomwe zimatukula dera lonse. Misonkho pa mpamba imat-anthauza kuti ndalama zochepa ndizomwe zigwire ntchito kupanga katundu wofunikira, kotero chitukuko chamtsogolo cha dera lonse chimachepa.

M’dziko la ufulu, ntchito zachuma ndi kusinthana zimachitika mosa-kakamiza. Ogulitsa amapeza ndalama popanga katundu ndi zinthu zomwe anthu ena akufuna komanso ali okonzeka kulipira. Anthu omwe amalemera samabera munthu. Siwolakwa pa mlandu uliwonse wosowa chilungamo. Sitingalole mbava ziwabere poganiza kuti izi zichepetsa kusiyana pa katundu: ndiye tilola bwanji boma kuchita zimenezi?

5 UFULU OCHITA MALONDA

Ntchito zachuma zam'misika ya ufulu

Ndondomeko zachuma mu dziko la ufulu zimalola amalonda kuchita mwaufulu. Zimatheka kudzera mu kudzipereka kwa anthu posinthana katundu ndi ntchito pakati pa anthu – nthawi zina molunjika koma nthawi zambiri kudzera mu ndalama. Anthu ali ndi ufulu osankha m'mene, komwe ndi yemwe angagwire naye ntchito, kugula zinthu, kuyamba mabizinezi, kusungira komanso kuchita malonda. Palibe yemwe amakakamizidwa kuchita malonda motere.

Malamulo opititsira patsogolo mgwirizano

Misika ya ufulu pazachuma siyikhala yopanda malamulo kwa aliyense kuchita zomwe akufuna, osayang'anira zotsatira kwa ena. Mfundo yosapwetekana imakhalapobe. Ndipo pali mndandanda wa malamulo, omwe amakhudza kupeza, umwini, ndi kusinthana kwa katundu, ufulu wa anthu pa ntchito zawo zomwe, ndi kukwaniritsa migwirizano. Malamulowa samangokhudza za makhalidwe a anthu okha, koma amakhudzanso magulu monga kuchita malonda mogwirizana, makampani ndi mabungwe azachifundo. Udindo wa boma ndiwo kulimbikitsa malamulo omwe amateteza katundu wa anthu ndi ufulu, ndi kuonetsetsa kuti m'gwirizano ikutsatidwa.

Komabe, udindowo uli ndi malire. Malamulo sali pamenepo kutso-golera ntchito zachuma, koma kuunikira. Ali ngati dengu lamoto lomwe lili ndi motowo. Ndipo ndikofunika kuti mphamvu za kaye-ndetsedwe ka misika zisaponderezedwe ndi malamulo opyola muyeso. Koma malamulo enieni a katundu, kusinthana ndi mgwirizano amalola anthu kugwirizana, koma amasankha, mopindulira onse potengera kukhulupirirana, kudalirana ndi chitetezo. Izi zimalimbikitsa mgwirizano waukulu pachuma ndi kuchulukitsa phindu lambiri lochokera pa mgwirizanowu.

Ubwino wosinthana modzipereka

Ndikosavuta kuganiza kuti ogulitsa okha ndi omwe amapindulira pa ntchito za malonda. Popeza amakhala ndi ndalama zambiri zonse

Maziko a dziko la ufulu

zikatha, pomwe ogula amatsala ndi zochepa. Izi zimapangitsa anthu kuganiza kuti ogulitsa ndiadyera ndipo amangoyang'ana za phindu lawo, osati za anthu ena.

Uku ndikulakwitsa. Kodi, pamapeto pa zonse, cholinga cha ndalama n'chiyani? Mu nthawi imene ndalama inali golide ndi siliva, inalinsu ndi ntchito zina ngati chitsulo chomwe chimatha kupangidwa kukhala zovala zamtengo wapatali kapena zokongoletsera. Koma ndalama zopangidwa kuchokera ku mapepala ndi zitsulo zina zili ndi ntchito ina yochepa. Chinthu chokhacho chofunikira chomwe ungachitire ndi ndalama ndi kusinthanitsa ndi katundu komanso ntchito zina.

M'mawu ena, ndalama ndi chida chosinthanitsira. Wogula amasinthanitsa ndi katundu kapena ntchito ina; wogulitsa kenaka amasinthanitsa ndi katundu ndi ntchito zina kwa winanso. Onsewa amawona kuti zawayendera pa malondawa. Kupanda kutero sakanavomera.

M'mene malonda amapangitsira chinthu kukhala chofunikira

Pakuti palibe munthu angasinthanitse chinthu ndi chomwe chili chosafunika, nanga onsewa angapindule bwanji? Chifukwa chake ndi chakuti kufunika, monga kukongola, kuli ndi mwini wake. Sikuli ngati ubwino wa zinthu za sayansi monga kulemera kapena kukula kwa chinthu. Ndi momwe munthu aliyense akuganizirira za chinthu chimenecho. Anthu am'dziko lamvula amaona kapu ya madzi kukhala yosafunikira kwenikweni; koma omwe ali m'chipululu atha kuiwona yofunikira kwambiri. Chovala chatsopano wachinyamata aliyense amafuna atakhala nacho, pomwe kwa makolo awo ndi zamkutu.

Izi zili chonchi chifukwa anthu amasiyana m'mene amaonera kufunikira kwa zinthu zomwe aliyense angapindule posinthana. Wogula nkhuu kwa ogulitsa pamsika amaiwona nkhuu kukhala yofunika kuposa ndalama yomwe akugulira. Koma wogulitsa amaona ndalama kukhala yofunika kusiyana ndi nkhuu. Zomwezinsu zimachitika pamene wogulitsa wagwiritsa ntchito ndalamayo kugulira zinthu zina – monga buledi. Wogulitsa uja amaona buledi kufunikira koposa ndalama zomwe wophikayo akufuna. Anthu atatu onsewa apindula,

ndichifukwa chake onsewa anavomera mwakufuna kwawo pa msinthewu.

Kunena chilungamo, kukula kwa kusiyana kwa kufunikira koikidwa pa nkuku, ndalama ndi buledi, kumakuzanso phindu lomwe aliyense amalipeza posinthanitsa. Chomwe akungoyenera kugwirizana ndi malamulo omwe angasinthanire katunduyu – malamulo a katundu, chilungamo ndi mgwirizano zomwe zimapanga ndondomeko za misika ya ufulu pazachuma. Kuwonjezera apo, onse ochita nawo malondawa amakhala ndi zokhumba zawo: aliyense amapanga msinthewo kuti apindulire, osati kumupindulira winayo.

Koma potsatira malamulowa, aliyense mosazindikira amapindulira nzake – ngati akutsogozedwa ndi ‘dzanja losaoneka’ monga Adam Smith akunenera. ¹⁷Ngakhale amalimbikitsika ndi zofuna zawo, amagwirizana mwakufuna kwawo wina ndi mnzake.

Kudzera mu ndalama, aliyense wayife atha kuchita malonda – ndi kugwirizana – osangoti ndi anthu okhawo alinawo mumsika umodzi koma ndi mamiliyoni a anthu m’mayiko omwe sitingadzapiteko, omwe chiyankhulo chawo sitingayankhule, omwe chikhalidwe ndi ndale zawo mwina sitingazivomereze. Mu zochitika zosawerengekazi, mbali zonse zimapindula. Anthu amagwirizana. Kufunika kumapangidwa. Anthu amakhala bwino. Mtundu wa anthu umapita patsogolo.

Osauka amapindula kwambiri

Ndondomeko ya kusinthana mwa ufulu ndiyachibadwa komanso yopindulitsa moti yafalikiraponse. Imapezeka ngakhale mosaloledwa, kapena kuvomerezedwa, m’mayiko omwe amakana ganizo la ufulu wa misika ngati mfundo yayikulu yoyenera kutsatidwa. Mayiko ambiri (kuphatikizirapo ambiri akum’ mawa) omwe amapereka ufulu ochepa kwa nzika zawo pa nkhani za umoyo komanso zapagulu amapereka ufulu ochulukirapo pa zachuma.

¹⁷ Adam Smith, *The Wealth of Nations*, 1776, Bowok IV, ch. II, para. IX.

Maziko a dziko la ufulu

Kunena zoonu, ntchito zachuma ndi malonda zinali zofunikira mu zaka zoyambirira mu ulamuliro wa chisiramu ndi kufalikira kwake. Kutseguka kwa njira zamalonda pa dziko lonse lapansi kunatukula chuma panthawi ya kudzukanso pochita zinthu ku Ulaya, zomwe zinatukulanso ntchito zaluso, chikhalidwe ndi maphunziro. Mayiko aku Amerika anatukuka kudzera mukulumikizana kwawo pamalonda ndi mayiko aku Ulaya, ndipo kenaka China.

Koma si achuma okha omwe amapindula kwambiri kaamba ka kutukuka kwa miyoyo ya anthu kotereku. Pamene ufulu wazachuma wafalikira, miyoyo ya anthu osauka yatukukanso kwambiri. Monga katswiri wazachuma ku Amerika Milton Friedman akunenera, madzi ofikira m'makomo chinali chinthu chapamwamba kwambiri mu nthawi ya ufumu wa Roma: koma phungu waku Roma sikuti amawafuna madziwa chifukwa anali ndi antchito omwe amamubwere-tsera.¹⁸ Anthu osauka aku Roma amakhala m'malo osasamalika; koma osauka aku Roma lero amakhala ndi mwayi wa madzi otentha ndi ozizira omwe akupezeka mosavuta.

Zotsatira za izi zikuonekeratu mukutsegula kwa ntchito zamalonda pakati pa mayiko ena posachedwapa ndi kufala kwa mfundo zochitira malonda m'mayiko monga China ndi India. Zotsatira zake, m'zaka makumi atatu chabe, pafupifupi anthu okwana biliyoni limodzi kapena kuposera apo awomboledwa mu umphawi wadzaoneni. Mamiliyoni a anthu tsopano akhoza kufuna kukhala moyo wa gulu la anthu apakatikati nakhala ndi zinthu zosafunikira kwenikweni monga foni zam'manja, wailesi za kanema, ndi magalimoto – komanso kugwira ntchito m'maofesi ndi mafakitale abwino, kaya ozizira kapena kuwasintha kukhala otentha momwe akufunira kusiyana ndi kumangotsatira nyengo za m'dziko mwawo.

Mmene ungatukukire pachuma

Ogulitsa ayenera kutumikira makasitomala

Mu dziko la ufulu, makasitomala amakhala ndi chisankho. Sali

¹⁸ Milton Friedman and Rose Friedman, *Free to Choose*, Harcourt Brace Jovanovich, New York, 1980, p. 147.

okakamizidwa kugula kwa ogulitsa apadera, monga omwe mphamvu zoyendetsera malonda zimaikidwa ku boma kapena anzawo. Makampani ogulitsa katundu atha kuchita upo kuti akweze mitengo, koma ndizovuta kuti zomwe agwirizanazo zikhazikike, chifukwa wina mwa iwo atha kuzemba ndikutsitsa mitengo yake kuti makasitomala ambiri amutsatire. Mu nthawi yomweyo, makampani ena ali ndi ufulu obwera pa msika ndi kupikisana ndi makampani omwe akupitiriza kukweza mitengo ya katundu.

Mdziko momwe mumakhaladi msika weniweni wa ufulu pazachuma, kotero, ogulitsa alibe mphamvu yopondereza makasitomala awo. Pokhapokha ngati akupanga katundu yemwe makasitomala akufuna, waubwino omwe akufuna ndi mtengo wachikoka, akhoza kuwononga bizinezi mwachangu. Anthu ndiwosamangika ndi mphamvu yamakampani akuluakulu. Mosiyana, ogulitsa amakwanitsa kukhalabe pamsika pochitapo kanthu pa zofuna zamakasitomala.

Kampani itha kukhala yayikulu, koma imakumanabe ndi mpikisano. Kampani yayikulu itha kumapanga katundu osiyanasiyana komanso kuchita malonda osiyanasiyana. Koma sikuti imangopikisana ndi makampani akuluakulu okha. Imapikisananso ndi makampani ena ang'onoang'ono ochuluka omwe amapanga magawo ena a malonda. Makampani ang'onoang'ono atha kukwanitsa kupanga katundu yemwe makampani akuluakulu amapanga mwabwino komanso motsikirako mtengo. Makampani atsopano ndi aluso atha kupanga katundu watsopano yemwe angapangitse katundu wa kampani ina kapena kampani yayikulu kukhala wosafunikira.

Ndi nkambakamwa chabe, kotero, kuti ndondomeko yoika mphamvu za malonda mmanja mwa anthu zimapangitsa kuti kampani zikule, ndipo zotsatira zake kutenga mphamvu zonse pamsika, pamene makampani akufuna kupeza phindu lochuluka koma atachepetsa zolowa. Mlingonso uli ndi mavuto ake: makampani aakulu amakhala ovuta kuwayendetsa komanso amachedwa m'zochitika. Nkoyenera kuwerenga magazine a maiko a azungu monga, za zaka makumi asanu zapitazo. Makampani ochepa nthawi imeneyo omwe

Maziko a dziko la ufulu

ankalengezetsa malonda akupezekabe. Onse anaposedwa ndi opikisana nawo omwe anayamba mochepa koma anali ndi luso lopanga zinthu komanso kapangidwe ka zinthu kotsika mtengo.

Osakakamira ulamuliro pa chuma

Choncho, makampani kapena anthu oyendetsa sayenera kukakamira ulamuliro pachuma kuchoka m’badwo wina kupita winanso. Anthu atha kukhala achuma mu dziko la ufulu, koma pokhapokha ngati akutumikira zofuna za anthu ndi kukopa makasitomala. Indedi, ‘kubwereza zinthu zokhazokhazo m’mibadwo itatu’ ndi mchitidwe wosasowa m’mayiko a ufulu kwambiri: anthu amakhazikitsa kampani ndikupangira chuma banja lawo, koma pofikira nthawi imene zidzukululu zawo zidzalowe nawo mubizineziyo, makampani ena amakhala ayamba kuwapitirira.

Ndondomeko imeneyi ndiyabwinoko kusiyana ndi m’mayiko omwe achuma amakhala ndi mphamvu pa ndale ndi chuma, ndi kuyesetsa kuti iwo ndi banja lawo akhale nacho mopitirira. Mu dziko la ufulu pachuma, aliyense yemwe ali ndi luso komanso wolimbikira atha kufuna kukhala ndi chuma – bola ngati akutumikira ena. Mwayi okhala wachuma sumangololekwa kwa anzawo, banja kapena chipani cha omwe ali m’boma, kapena kwa mtundu wina wa anthu kapena chipembedzo. Kunena zooni, ena mwa anthu achuma m’mayiko a ufulu ndi nzika zobwera, zomwe zinabwera ndi chidziwitso ndi maganizo osiyanasiyana ndikupanga katundu kapena zinthu zatsopano zomwe anthu ali osangalatsidwa kugula.

Pomwe pali boma la mphamvu lomwe limakondera anzawo, anthu abizinezi amayesetsa kuligwiritsa ntchito kuti liwapindulire okha. Akhoza kufuna malamulo omwe amachotsa opikisana nawo, kapena kuwapatsiratu mphamvu zonse. Ngakhale akhoza kuyesera kuyilimbikitsa mfundoyi ponena kuti iwateteza anthu ku katundu yemwe siwabwino, cholinga chawo chenicheni chimakhala kufuna kulamulira pamsika. Koma izi zitha kuwapatsa mphamvu yokakamiza zinthu zomwe sizikugwirizana ndi dziko la ufulu. Boma silikuyenera kukhala ndi mphamvu yokondera pa misika ndikupereka mphamvu

zonse ku kampani imodzi; koma, udindo wake ukuyenera kukhala wopititsa patsogolo ufulu ndi mpikisano.

Funso: Kodi mpikisano, phindu komanso kulengezetsa malonda n'kotayitsa nthawi?

Ayi. Phindu ndilomwe limalimbikitsa anthu kuchitapo kanthu, kufufuza mwayi ndi kupanga katundu ndi ntchito zomwe anthu ena amasankha kuti agule. Phindu limaonetsanso kuti zinthu zikugwiritsidwa ntchito kupanga katundu yemwe anthu m'dera akumuona kukhala ofunika kusiyana ndi katundu wosakonzedwayo.

Kulengezetsa malonda nkofunikira chifukwa kumawauza anthu za katundu watsopano ndi kuwonjezereka kwa ubwino komwe kwachitika pa katundu wakale. Mpikisano umawapatsa anthu chisankho pakati pa katundu osiyanasiyana, komanso kupangitsa ogulitsa kupanga katundu watsopano ndi kupereka katundu wabwino pantengo otsika. Popanda mpikisano, ogula akhoza kukhala opanda mphamvu. Anayenera kulandira chilichonse chomwe makampani amphamvu aganiza zowapatsa – kapena kukhala opanda kanthu.

Zamalonda

Chipambano mu dziko la ufulu pachuma sichitengera kulimbikira ntchito nthawi zonse – ngakhale zimathandiza nthawi zambiri. Uyenera kupereka katundu ndi ntchito zomwe anthu ena akufuna ndipo ali okonzeka kugula. Izi zimakhudza kukumana ndi zosayembekezereka– kuganizira katundu watsopano yemwe anthu angamufune – ndi kuika ndondomeko yayikulu yopangira katundu zomwe zingafune anthu ena operekera katundu, ogwira ntchito ndi otumiza katundu. Ndi anthu ochepa omwe amakonzeka kukumana ndi udindo komanso zosayembekezereka zimenezi; koma chipambano chope nekera cha kufunika kwa katundu ndi ndondomeko ya kapangidwe ka katunduyu, kulumikizana ndi chilimbikitso ndilo gawo lenileni la ochita malondawa. Amachita zinthu zazikulu zosayembekezereka, ndipo ngati anthu angagule katundu wawo, amapindula kwambiri.

Maziko a dziko la ufulu

Izi mapeto ake zimalimbikitsa kupanga katundu ndi kuwonjezera luso lopangira zinthu. Zimalimbikitsa anthu kupanga katundu watsopano komanso wabwino ndi ndondomeko poyembekezera kuti nawo azakwanitsa kupeza chuma chomwe azamalonda akale anapeza. Ndipo kuwonjezera ubwino ndi luso mosalekeza kukumapindulira makasitomala ndipo choncho dera lonse limapindula. Luso latsopano lomwe limathandizira anthu kuchepetsa ntchito kapena kupititsa patsogolo miyoyo yawo imabweretsa chitukuko ndikumwaza chuma kufikira patali koposa ndondomeko iliyonse ya boma.

Makasitomala amapindula ndi katundu komanso ntchito zomwe sakanatha kupeza kapena kupanga mwayiwo okha. Zimatengera kafukufuku ndi ukadaulo, mwachitsanzo, kupanga ndi kupereka mankhwala othandiza. Anthu paokha sangakhale ndi zipangizo komanso ukadaulo wopangira mankhwalawa womwe umafunikira – koma makampani opanga mankhwala alinawo. Ngakhale ogulitsa mankhwala m’dera atha kukhala ndi chidziwitso cha kagwiritsidwe ntchito, ubwino ndi kuipa kwa pafupifupi mankhwala mazana asanu kapena kuposera apo omwe alinawo. Makasitomala sangangokhala nawo ukadaulo woterewu – pokhapokha ngati angakhalenso ndi ukadaulo pa zakudya, zakumwa, zovala, nsapato ndi zina zonse zomwe amazifuna m’moyo wawo wa tsiku ndi tsiku.

Wochita za malonda atha kupeza chuma. Koma samachipeza podalira thukuta la wina. Ndalama zomwe amapeza zimachokera mu zomwe makasitomala amalipira mwakufuna kwawo. Amapeza chuma pothandiza ena, osati poika misonkho kapena kupondereza ena. Ndipo amakhalabe ndi chuma chawo pokhapokha ngati akutumikira zofuna za anthu. Kutu apitilize kupezabe chuma ayenera kuwamvetsetsetsa makasitomala awo ndi kuganizira zofuna zawo. Koteru nthawi zonse amakhala akuyang’ana mbali ina yomwe ikuperewera pofuna kuikwaniritsa. Ndi ndondomeko yokhazikika yofuna kukwaniritsa zofuna zamakasitomala.

Phindu ndi kuyerekeza

Kuyerekeza phindu, kumalimbikitsa opanga katundu – akuluakulu ndi ang’onoang’ono omwe – kuyesera zosayembekezera, kubweretsa

zinthu zatsopano, kuyendetsa ndi kugwira ntchito zotumikira ena. Ambiri omwe amatsutsa mfundo ya ufulu pachuma amayang'anira pansi ganizo la phindu – koma aliyense mwayife amafuna kupindula. Timalola zina zipite kuti tipeze zina zomwe timazona zofunikira kwambiri. Mwachitsanzo, timataya nthawi yathu kusamala mnyumba kuti tikhale ndi khomo laukhondo. Timaona kufunikira kwambiri kokhala ndi nyumba yaukhondo koposa mphamvu zogwiritsa ntchito posamala nyumbayo: kusiyanako ndiye phindu lathu. Siphindu la ndalama, koma mwanjira ina zili ngati wazamalonda yemwe akugula zinthu ndikupanga katundu yemwe akumugulitsa koposa m'mene adagulira zinthuzo. Ngakhale pamene tikuchita ntchito zachifundo kapena ntchito zina zam'dera mwathu – kutumikira mu gulu loyang'anira sukulu – timachita pa zofuna zathu, ngakhale mapeto ake atha kukhala akuti tikufuna ana onse akuderalo aphunzire. Chimenechonso ndi phindu (osati la ndalama) kwayife. Koma ndi phindu la ndalama lokha lomwe otsutsawa amaliona ndi kusagwirizana nalo. Izi ndi zosamveka komanso zosagwirizana.

Ndi chimodzimodzinso pamene kuyelekeza kukutsutsidwa. Kunena zoon, kuyembekezerasizikhudza misika yachuma yokha. Tonsefe timayekeza. Alimi amabzala mbewu mwachiyembekezo chokhala ndi mbewu yogulika pamsika. Timapita ku sukulu kuti tipeze maphunziro omwe amatithandiza kulembedwa ntchito mosavuta. Zonsezi ndi zongoyerekezera.

Pa nkhani zachuma, kuyerekezera ndikofunika kwambiri. Sitima zapanyanja sizikanamayenda ngati makapani a inshuransi ndi akatswiri sadali okonzeka kuyerekezera ndi kutsatira njira yabwino yomwe ingayende. Kapangidwe ka katundu masiku ano kamatengera migwirizano yayikulu komanso yanthawi yayitali – monga migwirizano yobweretsa katundu, kapena migwirizano yomanga ndi kukonza fakitale. Munthu opanga katundu payekha sangakwanitse kuyesera zonsezi. Koteru amaitanira ena kudzagula nawo mbali ya malonda awo. Uwu ndi mtundu wina wa kuyerekeza. M'misika yogulitsa umwini wa makampani, oyerekeza amagula ndi kugulitsa mbali za bizinezi zawo ndi chiyembekezo chopeza phindu, koma kuti atero

Maziko a dziko la ufulu

ayenera kukhala ndi ukadaulo odziwa makampani omwe akupanga nawo malonda ndi kuthekera kwawo m'tsogolo. Ukadaulowu umabweretsa uthenga ofunikira ku misikayi, ndi kuthandiza mitengo kufika mlingo wawo wovomerezeka mwachangu kusiyana ndi m'mene zikanakhala popanda uthengawu, kupangitsa msika wonse kukhala wabwino komanso womvetsetseka.

Kupanga phindu sichimodzimodzi ndi dyera. Anthu amasaka phindu ndi zolinga zawo, koma izi sizikufanana ndi dyera. Mlingo wina wa dyera ndiwofunikira ngati aliyense angakhalebe ndimoyo, kupewa kuvulala ndi kusamalira matupi athu. Koma dyera ndi nkhani ya makhalidwe, kusonyeza kuti wina akudzikonda moposa muyeso, mpaka kupweteka ena. M'dziko la ufulu, ogulitsa amakwaniritsa zofuna zawo pothandiza ena.

Bizinezi ndi ubale

Ngakhale zili zovuta, bizinezi si umoyo onse. Ngakhale munthu olimbikira kwambiri pa bizinezi m'dziko la ufulu ali ndi banja ndi zokonda zina monga masewero kapena zizolowezi, kapena magulu ndi mabungwe omwe amachita nawo zofanana. Wina angoyenera kuona mayiko omwe ntchito za malonda zimakhala mmanja mwa anthu wamba monga Italy, komwe ubale wapabanja umakhala wolimba kwambiri, kuti azindikire kuti banja ndi misika yazachuma zimayendera limodzi mosavuta.

Koma kukhala mu bizinezi sikuvomereza kupangira nkhanza anthu ena, komanso sikuvomereza kuwapweteka ena – izi nzokanidwa ndi mfundo yosapwetekana. Ndipo ubale opindula kwambiri ndi wochita ndi anzako omwe umapanga nawo bizinezi m'malo ogwira ntchito. Mwanjira ina, dziko la ufulu pa malonda limalimbikitsa ubale pakati pa anthu okhalira limodzi. Limawapatsa anthu chuma ndi nthawi yopangira zinthu zina, monga za chipembedzo, mabungwe am'dera ndi ntchito zachifundo.

M'mene misika imayendera

Dongosolo lolumikizirana pa mitengo

Misika yambiri imayenda kudzera mu ndalama. Patha kukhala msintho owonekeratu – kusinthanitsa – popanda ndalama: koma ndalama zimabweretsa njira yachangu. Ogulitsa atha kusinthanitsa katundu kapena ntchito ndi ndalama, ndikuyang'ana kaye chofunika kwambiri asanayisinthanitse ndi katundu komanso ntchito ina. Izi zikutanthauza kuti ometa tsitsi omwe ali ndi njala sakuyenera kuchita kukasakasaka wophika zinthu kuti amumete pofuna kuchita malonda.

Mitengo nthawi zambiri imaonetsedwa mu ndalama. Mitengo simlingo yokhazikika ya kufunika kwa chinthu, chifukwa kufunika kumakhala m'maganizo a okhudzidwa ndipo anthu osiyana amaona kufunika kwa chinthu mosiyananso. Komanso mitengo imanena chinachake chokhudza m'mene anthu akumufunira katundu komanso kusowa kwake. Amaonetsa mlingo umene anthu ali okonzeka kusinthanitsira chinthu china ndi chinzake.

Ngati chidziwitso cha kusowa kwa zinthu, mitengo imakhala yokwera kwambiri. ¹⁹Ndipo siimangoonetsera komwe katundu akufunika kwambiri. Mitengo yokwera imapereka chikoka kwa ogulitsa kuti afikire mlingo wofunikirawo. Poona mitengo yokwera, ogulitsa amafika pamsika kuti apeze phindu lomwe likuonekalo, poika chidwi pa zinthu monga antchito ndi mpamba pokwaniritsa zomwe zikufunikazo. Mitengo yotsika, imasonyetsa kuti katundu sakufunika wambiri ndipo atha kukagwira bwino ntchito kwina.

Munjira iyi, mitengo imagwira ntchito yofunikira kwambiri mu dziko la ufulu pachuma, kuthandiza kupititsa katundu komwe akufunikira kwambiri ndi kumuchotsa komwe aliko wochuluka. Imathandizanso kuchotsa zowonongeka: kuti apange phindu lochuluka, ogulitsa ayenera kupeza zipangizo zosalowa mthumba. Izi zimathandiza kusamalira zinthu ndi kuonetsetsa kuti zikugwiritsidwa ntchito moyenerera.

¹⁹ These points are made well in F. A. Hayek, *Individualism and Economic Order*, University of Chicago Press, Chicago, IL, 1949. For a brief summary, see Eamonn

Maziko a dziko la ufulu

Chotsatirachi chimafalikira ku misika yosiyanasiyana m’dziko lonse la ufulu pa chuma, komanso ku dziko lonse lapansi. Mwachitsanzo, tingoyerekeza kuti papezeka ntchito ina ya chitsulo. Mafakitale ayamba kufuna zitsulo zambiri. Akonzeka kulipira mtengo okwera kusiyana ndi kale. Mitengo yokwerayi iwapangitsa makampani amigodi kupanga zitsulo zambiri komanso ogulitsa zinthu zambiri pakamodzi kuyamba kupezeka nazo pamsika. Koma mofananirapo, ogwiritsa ntchito ena azitsulowo ayamba kufuna mlowam’ malo wa chitsulocho kusiyana ndi kumagula pamtengo okwera. Afuna zolowa mmalozo zochuluka kwambiri ndipo mtengo wakenso ukwera. Izi ziwapangitsa anthu kupanga zolowa m’ malo zo zochuluka, ndikupangitsa ogwiritsa ntchito kufuna zolowa mmalo za zolowa mmalo zoyambazo.

Munjira iyi, mitengo imapereka uthenga okhudza kusowa kwa chinthu mu ndondomeko yonse ya zachuma. Katswiri wazachuma wina wotchedwa F. A. Hayek adatchula njirayi kuti ‘dongosolo lolumikizana lalikulu’ la pamsika, nthawi zonse kusonyeza komwe katundu aliko wambiri ndi komwe akuperewera ndi kuwauza anthu komwe angaika moyenera ndalama ndi mphamvu zawo.

Misika siingakhale yabwino kwambiri

Ukawerenga mabuku okhudza zachuma, utha kuona ngati misika imadalira mpikisano wabwino kwambiri pakati pa ogulitsa ochuluka ofanana omwe akugulitsa katundu wofanana ndi makasitomala ofanana. Izi sizoon. Izi ndi zolembedwa zosokoneza. Choonadi chake nchakuti misika imayenda – ndipo ikhoza kuyenda pokhapokha – chifukwa anthu ndi katundu ndiwosiyana.

Ngati aliyense angakhale ndi zofunikira zofanana, palibe yemwe angapange malonda. Mbali zonse zikadaona kufunikira kwa katundu yemwe ali nawo mofanana, choncho kusinthana kukanakhala kopanda tanthauzo. Kusinthana kumakhalapo chifukwa sitigwirizana pa za kufunikira kwa chinthu. Ndiponso, ngati ogulitsa aliyense angagulitse malonda ofanana pa mtengo ofanananso, palibe chomwe makasitomala angasankhepo. Palibe ogulitsa yemwe angapose anzake ndikupanga phindu lochuluka.

Koma phindu lochuluka ndilomwe limalimbikitsa azamalonda kuti apambane. Amapanga izi potsitsa mtengo wa katundu wawo – monga kusintha kapangidwe ka zinthu. Koma chofunikira kwambiri, amapanga katundu wawo kukhala wabwino. Amamukonza mwaluso ndi kumusiyanitsa ndi wina. Amawapatsa ogula chinachake chatsopano komanso chabwino kuposa katundu yemwe anamuzolowera. Ndipo amawauza ogula zambiri za kusintha kwa katundu wawo kuti amukonde kusiyana ndi wina.

Izi zimapangitsa misika ya ufulu kukhala yosinthisintha modabwitsa – osati mosasintha, mouma ndi mosasuntha ngati galafu ya mabuku ofunika kugulitsidwa ndi kugulidwa. Ogulitsa katundu amakhala akusinthisintha luso kuti apange katundu wochititsa chidwi, ndipo makasitomala amakhala akufuna katundu wapamwamba mosalekeza.

Kusatheka kokonza ndondomeko pamodzi

Kuyesera kwa boma kuyendetsa zachuma ndi kupanga katundu yemwe anthu akufuna sikungagwirizane ndi kusinthisintha kwa dongosolo la misika limeneli.

Pali chikakamizo chochepa kwa makampani omwe amapatsidwa mphamvu yochita malonda ndi boma kuti apange zinthu mwaluso. Ndinso andale sangadziwe zenizeni zomwe anthu akufuna ndi kuzitenga zofunikira. Akhoza kupangitsa zisankho apo ndi apo, koma izi zili kutali ndi mpikisano wa pamsika, m'mene zisankho za ogula zimapereka kwa ogulitsa uthenga pafupipafupi wokhudza zomwe akufuna.

Kuti achite bwino, azamalonda ayenera kumvetsetsa makasitomala awo. Sangadikire zaka zambiri kuti amve maganizo awo pa katundu yense, monga limachitira boma pa zisankho. Ayenera kukhala tcheru pa zomwe makasitomala akufuna, ndi mtengo komanso kupezeka kwa ogulitsa ndi zinthu zopangira katundu. Ogulitsa malo ndi nyumba, mwachitsanso, amayenera kudziwa zomwe zikuchitika m'misika ya katundu – ndiwogula ati omwe akufuna nyumba za mtundu wina wake, mwachitsanzo – osati pa mwezi umodzi koma

Maziko a dziko la ufulu

tsiku ndi tsiku ngakhale pa ola lililonse. Palibe ulamuliro umodzi omwe ungamolere uthenga wosinthasinthawu, ndi kuchitapo kanthu usanasinthenso.

Anthu ena amaganiza kuti chifukwa choti mayiko a ufulu pachuma ulibe ulamuliro wochokera malo amodzi, uyenera kukhala wopanda dongosolo. Kunena zoono, misika imakhala yadongosolo. Potsatira malamulo ogwirizana akatundu ndi kusinthana, anthu amakhala ndi kuthekera kopanga malonda ndi kuchitira zinthu limodzi, ndi kuyembekeza zochita za ena, mosakaika. Misika imakhala yadongosolo kwambiri. Imagwiritsa ntchito akadaulo opezeka mosavuta ndi nzeru za anthu ochuluka, omwe onse amakonza ndodomeko zawo ndi kusintha molingana ndi ndodomeko za ena. Chikonzero chochuluka chimapezeka m'dziko la ufulu pa zachuma kusiyana ndi m'mayiko a ulamuliro womwe mphamvu zimakhala malo amodzi – zimangochitika kuti amapanga ndi anthu pawokha kusiyana ndi boma.

Funso: misika ya ufulu siyinalephereko kuteteza chilengedwe?

Ayi. Misika siyinalephereko. Palibe msika weniweni omwe umagulitsa katundu wachilengedwe. Misika imagwira ntchito bwino pamene zinthu zikusowa komanso pamene osalipira palibe, osati pamene zinthu zilipo zambiri kapena osalipira asakuchotsedwa. Anthu tsopano ayamba kuona kuti pathanso kukhala msika wa zachilengedwe. M'malo molola kuti nsomba zambiri zikololedwe mowononga, mwachitsanzo, mayiko ambiri amaika malire okhazikika ndikuika chilolezo chokololera gawo la nsombazo. Zilolezozi nzolimbikitsa malonda, ndipo misika imapezeka mwachangu, kupititsa patsogolo kugwiritsa bwino zinthu panthawi yomweyonso kulola kuti nsomba zikhalepo zochuluka.

Ndipo pamene anthu akulemerabe, kaamba ka ufulu wochita malonda, akhoza kukwanitsa kusamalira chilengedwe chawo. Dziko la China limavutika ndi kuwonongeka kwa mpweya chifukwa cha mafakitale ake, koma anthu kumeneko amaona kuti chofunikira ndi kutukuka pachuma kusiyana ndi mpweya

wabwino. Pamene akulemerabe, monga mayiko omwe anayamba kukhala ndi chuma, miyoyo ya anthu isintha ndipo azatha kukwanitsa kukhala ndi mafakitale omwe samadzawononga mpweya kwambiri.

Malonda othandizidwa ndi boma

Mayiko ochepa lero amakhulupirira kuti atha kukwanitsa kukhala ndi kuyendetsa ntchito zonse zopangira zinthu za m'dziko lawo. Ndongomeko zoyendetsera chuma m'mayiko ambiri ndizosakanikirana ndi m'mene boma limakhala ndi umwini wamakampani ena ndi kuyesera kutsogolera komanso kuyendetsa zochita zaena poika ndo-ndomeko, malamulo, kuthandizira makampani popanga zinthu, misonkho ndi kukhalanso ndi umwini.

Mu zaka zapitazi taona mayiko ambiri akutenga ndi kuyamba kuyang'anira gawo la mafakitale omwe anali ndi kufunikira kwapadera ndipo mayiko ambiri akupitirira kukhala ndi umwini komanso kuyendetsa makampaniwa – zomwe zitha kuphatikiza zolumikizanso anthu, zamayendedwe, mabanki, opanga zofunikira mmoyo, zamigodi ndi zina zotero.

Vuto ndilakuti umwini wa boma pa makampani otere nthawi zambiri umapereka mphamvu zambiri ku boma. Kuchuluka mphamvu kotere nthawi zambiri kumakula pofika poti munthu amalephera kuwayendetsa bwino. Koma sizitengera kuti mphamvuzo zili m'manja mwa boma kapena azamalonda oti siaboma; mapeto ake zimasokonekera ndipo anthu amapatsidwa katundu osakhala bwino pamtengo okwera.

Kufunikira kwakukulu kwa makampaniwa sichifukwa chokwanira kuti akhale m'manja mwaboma. Mabanki a m'mayiko achuma kwambiri sali m'manja mwaboma: ndipo kuwasintha kukhala m'manja mwaboma kukhoza kuwononga mabankiwa, ndi mabizinesi ndinso mabanja omwe amadalira pa iwo. Makampani amalonda, ogwira ntchito ngati opereka katundu kuboma kapena kwa anthu, tsopano amapereka ntchito zambiri zolumikizitsa anthu, zamayendedwe ndi zopereka zofunikira mmoyo padziko lonse lapansi.

Maziko a dziko la ufulu

Mayiko ambiri achotsa makampani ambiri m’manja mwaboma, kuvomereza kuti zinthu zofunikazi zitha kuperekedwa bwino ndimakampani opikisana omwe angaziyendetse mwaukadaulo ndi mpamba wawo.

Maboma aphunzira kuti atha kulamulira makampani mosadalira kuti akhale m’manja mwawo. Atha kungogulako mbali mu kampani yofunikira (yomwe ili m’manja mwa anthu), ndikugwiritsa ntchito ufulu wawo ngati m’modzi waeni kampaniyo kulamulira kampani zomwe iyenera kuchita ndi kusankha woyendetsa. Nthawi zina atha kudzipatsa ‘mbali yayikulu’ zomwe zimawapangitsa kulamula pa nkhani zofunika.

Kulowerera uku kutha kukanidwa m’mayiko a ufulu. Zimafanana ndi umwini waboma, kulola boma kupanga ziganizo pa kampani yomwe sanaigule. Eni ake – kuphatikizirapo anthu wamba omwe angaike ndalama zawo zomwe amasunga ndi penshoni mu makampani otere – amalandidwa chuma chawo. Ndipo kuthekera kwa katangale kumakhala kwakukulu – anzawo a andale atha kupatsidwa maudindo akuluakulu oyendetsa, mafakitale atha kuikidwa m’ malo omwe awakonda, ndipo phindu lake litha kugwiritsidwa ntchito kupindulira owatsatira.

Maboma atha kukhalanso ndi ulamuliro wamakampani omwe ali m’manja mwa anthu poika malamulo. Malamulo atha kuika malire kapena kulamulira m’mene makampani akuyenera kuyendera, zomwe akuyenera kupanga, mtengo omwe akuyenera kugulitsira katundu, komwe akuyenera kuika mabizinezi awo komanso kupereka mwayi wantchito, malipiro omwe akuyenera kupereka kwa antchito awo – ndi zina zambiri. Ulamuliro waboma oterewu ku makampani omwe sali m’manja mwa boma umapezeka kwambiri, ngakhale m’mayiko omwe amadzitcha a ufulu – koma ndizotsutsaniratu ndi mfundo za umwini wa katundu omwe ndi maziko enieni a dziko la ufulu weniweni.

Malonda pakati pa mayiko

Malonda ndi mchitidwe woteteza

Phindu lomwe limapezedwa ndi anthu pa ntchito zamalonda a ufulu

m'dziko lawo limapezekanso kwa anthuwa akachita malonda ndi mayiko ena. Malonda amawalola mayiko kukhazikika pa zomwe amazidziwa bwino kwambiri ndikutumiza zotsalazo ku mayiko ena omwe ali ndi kuthekera kopanga zina. Mwachitsanzo, gawo lalikulula la maluwa odula padziko lapansi, amachokera ku Kenya, komwe nthaka ndi nyengo ili yabwino kuwalima; pamene ku Chile, Australia, ndi France amadziwika bwino ndikutsogola popanga vinyo chifukwa cha nthaka ndi nyengo yawo komanso ukadaulo womwe akhala nawo kaamba kochitachita. Dziko la India, lomwe lili ndi anthu ophunzira bwino komanso otsika mtengo kuwalipira, lakhala lili dziko lofunikira pantchito za makompyuta. Malonda pakati pa mayiko amalola anthu kuika chidwi mbali ina ndi kukhala ndi mpamba monga zipangizo zomwe zimapangitsa kapangidwe ka katundu kukhala kotsika mtengo.

Ndipo pakuti zofunikira za anthu a m'mayiko osiyanasiyana zimasiyana kwambiri ndi zofunikira za anthu a m'dziko momwemo, kuthekera kwa mwayi opindula mbali zonse pamalonda ndikwakukulu. Mwachitsanzo, m'zaka za pakatikati, apaulendo aku Ulaya ankaliyira ndalama zochuluka kugula katundu monga tiyi yemwe ankamera mosavuta komanso yemwe anali wambiri ku India ndi China, kapena zokometsera chakudya zomwe zinali zotsika mtengo komanso zopezeka mosavuta m'mayiko apakati chakum'mawa. Lero anthu amayenda pa ndege pafupifupi theka ladziko lonse lapansi kukaona zomangidwa ku Venice kapena chikhalidwe chaku Thailand, kuyamikira kusiyana kwake ndi mayiko akwawo.

Dziko la ufulu limalola katundu wa m'mayiko osiyanasiyana. Limavomereza kusinthasinthwa kwa phindu la malonda komanso mmene malondawo amathandizira kuti chitukuko chifalikire. Njira ina ndiyo kutetezera, pamene mayiko amayesera kuteteza ogulitsa awo posalola katundu obwera kuchoka m'mayiko ena. Izi zimapangitsa ogulitsa m'dzikolo kukhala opanda phuma. Koma izi zikutanthauza kuti ogula m'dzikolo akukanizidwa katundu wabwino ndiwotsika mtengo yemwe amachokera m'mayiko akunja. Amalipira mitengo yokwera kwa ogulitsa am'dzikolo, ali ndi zisankho zochepa komanso ayenera kuzolowera kugwiritsa ntchito katundu osakhala bwino.

Maziko a dziko la ufulu

Kutetezera ndi kowononga

Pamene dziko likupanga chinthu lokha chomwe chikanatha kupangidwa bwino komanso motsikirapo m'mayiko ena, limawononga zinthu (kuphatikizirapo zachilengedwe). Adam Smith analongosolapo kuti kudzera nyumba zotetezera chilengedwe, zipatso za grepi zitha kulimidwa m'malo ozizira komanso amvula ku Scotland – koma pamtengo okwera makumi atatu kusiyana ndi kuzilima m'malo adzuwa aku France. Tiwonongerani zinthu – nthawi, ndalama ndi mphamvu – poyesera kupanga zinthu wekha zomwe wina angazipange bwino komanso motsikirapo mtengo²⁰?

Nzosadabwitsa, kuti opanga bwino katundu ena amaletsa mayiko ena kubweretsa katundu wawo kudzera mu ziletso, malire a mlingo wa katundu ndi misonkho. Amatha nawo kubwezera poika zotchingira zawo. Nkhondo zapamalonda zotere sizipindulira aliyense. Kumakhala kwabwino kwambiri – makamaka kwa anthu osaukitsitsa a m'mayikowa, omwe akuyenera kupindula kwambiri ndi katundu wotsika mtengo wochokera mmayiko ena – ngati zotchinga zonse zingachotsedwe ndikulola anthu kuchita malonda mmene akufunira.

Izi zikukhudzanso anthu obwera m'dziko. Mu dziko la ufulu boma silingaike zotchinga pa mayendedwe a anthu pakati pa mayiko. Anthu obwera m'dziko amabwera ndi mphamvu komanso maganizo atso-pano omwe amapindulira dziko lomwe akupitalo. Mwachitsanzo, kupita kwa anthu ku Ulaya ndi kumpoto kwa Amerika kunadzetsa chitukuko chachikulu. Kuchotsa mphamvu zomwe zakhala zikutsatidwa kwa zaka zambiri sikungakhale kosavuta, ndipo kutha kudzetsa mavuto mukanthawi kochepe: koma ichi chiyenera kukhalabe cholinga cha omwe amakhulupirira dziko la ufulu.

Mchitidwe wa malonda mwa ufulu

Mayiko omwe ali ndi ulamuliro wovomereza kuchita malonda momasuka amatukuka mwachangu ndikukhala achuma kwambiri kusiyana ndi omwe alibe. Taganizirani mizinda ing'onoing'ono monga Hong Kong ndi Singapore – palibe mwayiyo ili ndi

²⁰ Adam Smith, *The Wealth of Nations*, 1776, Bowok IV, ch. II.

zachilengedwe zowathandizira. M'zaka zam'ma 1960, inali mizinda yosauka ngati mayiko ambiri aku Afrika komanso Carribbean omwe anali ndi zachilengedwe zambiri. Lero, analemera kwambiri kaamba ka malonda ndi ufulu pa zachuma.

Kufalikira kwa malonda kwachepetsa umphawi padziko lonse lapansi kwambiri. Anthu ena amaopa kuti kulola katundu wina kubwera kuchokera m'mayiko ena, komanso makampani akunja, zitha kupondezera anthu a m'dzikolo – monga 'bizinezi zazing'ono zopeza ndalama zochepa' zopanga nsapato ndi zovala. Choona nchakuti palibe amakakamiza munthu kugwira ntchito m'mafakitale; koma anthu amasankha kugwira m'mafakitale potsata malipiro okhazikika kusiyana ndi ntchito yolemetsa m'minda dzuwa likuswa mtengo nkupeza phindu lochepa. M'mayiko monga Vietnam, momwe mwabwera mafakitale akunja, ogwira ntchito m'mafakitalewa pano atha kukwanitsa kugula njinga zamoto, wailesi za kanema ndi zina zosangalatsa zomwe sankaziganizira nkomwe.

Pafupifupi katundu aliyense wapamwamba lero – monga foni yam'manja kapena kompyuta yam'manja – imafuna zinthu, luso ndi ukadaulo kuchokera m'mayiko a padziko lapansi. Wolunzanitsa lusoyo akhoza kukhala waku California koma opanga katunduyo atha kukhala anthu aku Hong Kong ndi ena aku China. Zitsulo ndi zina zogwiritsidwa ntchito zitha kuchoka ku mgodi wamaiko aku Asia, Australia, kapena kum'mwera kwa Amerika. Katunduyo atha kutumizidwa kudzera pa sitima zapa njanji zaku Greece kapena ndege zaku Netherlands. Koma ogwiritsa ntchito ndi anthu onse apadziko lapansi.

Pamene anthu akuchita malonda ndi anthu adziko lina, amafika powamvetsetsa bwino, kapena kuwapatsa ulemu kumene. Ochita malonda sangakwanitse kudziwona ofunikira kuposa nzika zamayiko ena kapena anthu amtundu wina. Kuti apindule, ayenera kuchita malonda mwamtendere ngati ogulitsa, othandizana nawo pochita malonda kapena makasitomala. Malonda pakati pa mayiko amadzetsa kumvana ndi mtendere, zomwe zili ndi phindu lake lochuluka. Nzosadabwitsa kuti mayiko a ufulu ndi omasuka kwambiri ndiwomwe amachita malonda mwaufulu komanso momasuka.

6 KATUNDU NDI CHILUNGAMO

Pa mutu wachinayi tinaona kuti ‘chilungamo’ chili ndi tanthauzo lapadera – m’mene anthu ayenera kukhalira molemekezana wina ndi mnzake, kusiyanana ndi mmene phindu la zochita zawo liyenera kugawidwira pakati pawo. Koma malamulo omwe amatsogolera m’mene anthu akuyenera kukhalira wina ndi mnzake ndiwovuta. Kusunga ndi kulimbikitsa malamulo amakhalidwewa kumafuna zikhulupiriro zina ndi mabungwe ena am’dera - zinthu monga katundu, mphamvu ya lamulo ndi kulemekeza ufulu wa ena.

Katundu wa anthu osati boma

Tanthauzo la katundu

Kuthekera kwa anthu kukhala ndi katundu ndi nsanamira ya dziko la ufulu. Umwini wa katundu umatanthauza kuti uli ndi kuthekera kokhala ndi chinthu ndi kuchilamulira – ndipo ukhoza osalola anthu ena kutengapo gawo pa chimenechi– uli ndi mphamvu yowachotsera ena. Utha kusangalala nacho, kubwereketsa, kugulitsa, kuchipereka kwa ena kapena kuchiwononga, koma anthu ena sangagwiritse ntchito kapena kutenga popanda chilolezo chako. Katundu wako sangalandidwe popanda dongosolo.

Anthu atha kukhala ndi katundu, chimodzimodzinso magulu, monga anthu apabanja, anthu ochitira bizinezi pamodzi ndi makampani, ndi boma komanso nthambi zaboma.

Nthawi zonse katundu sichinthu chogwirika chokha kapena chosanthika monga malo kapena nyumba. Chitha kukhala chinthu choyenda, monga chiweto, galimoto kapena chovala. Chitha kukhalanso chinthu chosagwirika. Chitha kukhala katundu wamunzeru monga chizindikiro kapena ufulu wogwiritsa ntchito chinthu chomwe walembe kapena kujambula, kapena chitetezo pa chinthu chomwe unakonza. Chitha kukhalanso ndalama zomwe unaika mu kampani, ngongole yomwe munthu wina anabwereka kwa iwe kapena ndalama zomwe wasunga. Itha kukhala lizi yotenga malo amunthu kwakanthawi kapena ufulu wa wailesi kugwiritsa ntchito malo omvekerana

ena ake. Choncho, katundu, kwenikweni sichintha chosasuntha komanso chogwirika.

Katundu akhozanso kupangidwa. Lole yayikulu kapena chovala chitha kusonkhanitsidwa ndi mbali zosiyanasiyana kupanga katundu watsopano. Chiweto chiberekedwa ndi kusamaliridwa kufikira kukula. Anthu amalemba mabuku atsopano kapena kukonza njira zatsopano zosungira ndalama. Luso lamakono la dijito lapangitsa kuti njira zolumikizana kudzera pafoni zichuluke – mtundu watsopano wa katundu.

Chinanso chofunikira nchakuti, katundu wako akuphatikizanso ufulu pa thupi lako ndi ufulu wodyerera zipatso za thukuta lako. M'dziko la ufulu sungamangidwe kapena kuikidwa mndende popanda chifukwa chomveka bwino. Sungakakamizidwe kumugwirira ntchito munthu wina. Ndipo anthu ena sakuloledwa kuba chomwe wapanga ndi luso, luntha lako, kudziwa kwako kapena mphamvu zako.

Katundu ndi chitukuko

Kupereka umwini wakatundu kwa anthu kunayamba kalekale chiyambire mbiri ya anthu, ngakhale kwakhala kusakulemekezedwa. Ku Sparta kalelo, ganizo la katundu wamunthu silinkawerengeredwa. Mu zaka za posachedwapa, mayiko monga Russia ndi China anayeserapo umwini wagulu wa munda yikuluyikulu ndi mafakitale. Koma ndi kudzera mu kuvomereza umwini wa katundu kwa anthu wamba, chitetezo chake, zomwe zinadzetsa malonda atsopanowa – kuwonjezera chuma kwambiri pakati pa mayiko omwe amachita malonda.

Nzosavuta kuona chifukwa chake. Katswiri woona za ubale wa zolengedwa wotchedwa Garrett Hardin analemba buku lotchedwa '*the tragedy of the commons*'²¹. Pamene anthu ali ndi umwini wachinthu, amakondwera kwambiri pakuchisunga ndi kuchisamalira kusiyana ndi pomwe alibe. Munda wa munthu umalimidwa bwino kusiyana ndi munda olimidwa ndi gulu. Masitepe anyumba zosanjikizana zokhala anthu ambiri amakhala auve komanso owonongeka,

²¹ Garrett Hardin, 'The tragedy of the com'mons', Science, 162(3859), 1968, pp. 1243–8.

Maziko a dziko la ufulu

ngakhale zipinda zogona za anthuwo zili zosamala bwino. Anthu samaona chifukwa chogwiritsa ntchito nthawi ndi mphamvu zawo pa chinthu chomwe sichawo, chifukwa anthu ena azapeza nawo phindu ngakhale asanagwire ntchito iliyonse.

Kuteteza katundu komanso kulemekeza umwini wa katundu kumapangitsa anthu kukulitsa mpamba. Alimi ndiwothekera kubzala mbeu, kulima minda ndi kugula mathirekitale ngati zokolola zonse zili zawo. Azamalonda atha kulolera kuika ndalama zawo m' mafakitale, zida ndi njira zopangira katundu ngati angaganize mwaiwo okha m'mene katundu wawo angagwiritsidwire ntchito komanso kudziwa kuti palibe wina ali ndi ufulu owalanda. Ngati ufulu okhala ndi katundu uli wotetezedwa ndi kulemekezedwa, anthu amakhala ndi mpamba wochulukira ndipo phindu limakwera, zomwe zimathandiza dziko lonse. Koma ngati katundu angabedwe kapena kuwonongedwa ndi ena, kapena wina atha kutenga zinthu zomwe zapangidwa, palibe cholimbikitsa anthu kuika luso lawo, nthawi yawo, mphamvu zawo ndi ukadaulo wawo kuti apange zinthu – ndipo dera lonse limavutika.

Katundu ndi ufulu wina

Ufulu womwe anthu amasangalala nawo mudziko la ufulu wagona pa umwini wa katundu. Popanda anthu kukhala ndi katundu wawo sipangakhale ufulu.

Mwachitsanzo, ufulu wa anthu kuyankhula maganizo awo, kukhala pagulu ndi anzawo komanso kutengapo mbali pa nkhani zandale. Ngati sipangakhale umwini wa chuma – ngati maboma ena amalumulira katundu yense – opikisana angakope bwanji anthu kuti adzavavotere? Kuti awauze anthu mfundo zawo, ayenera kulipira nyumba zikuluzikulu zokumaniramo anthu, kusindikiza mapepala ogawira anthu ndi kuulutsa maganizo awo. Koma ngati boma lili ndi umwini wa malo onse okumanirana anthu, kuyang'anira zoyenera kusindikiza ndi mapepala, ndi kuyendetsa nyumba zonse zoulutsira mawu, litha kuletsa wina aliyense kukopa anthu mosavuta²². (ngati oimrirayo amadzudzula boma kapena mfundo zake, kuthekera

²² A point made well in F. A. Hayek, *The Road to Serfdom*, Routledge, London, 1944..

kochitiridwa izi n'kwakukulu). Kuwonjezera apo, ngati anthu alibe umwini wakatundu, palibe chomwe chingaletse boma kupondereza omwe akulidzudzula powamanga kapena kuwapha kumene. (Ndizokhumudwitsa koma zitsanzo za izi sizachilendo)

Popanda katundu, palibe chilungamo. Pokhapokha ngati uli ndi ufulu pa thupi lako, ntchito yako ndi zomwe uli nazo, zitha kulandidwa popanda chipepeso. Ngati ulibe ufulu pa thupi lako, utha kumangidwa mosavuta, kuikidwa mundende ndi kuphedwa; ngati ulibe ufulu pa ntchito yako, utha kusandutsidwa kapolo; ngati ulibe ufulu pa katundu wako, utha kuberedwa. Patha kukhala popanda chitetezo chilichonse pa mchitidwe wolakwika.

Phindu labwino la katundu

Katundu, ndi chitetezo cha ufulu wa katundu, umampatsa munthu chitetezo ku mphamvu ya boma ndi kukakamizidwa ndi ena. Kukhala ndi katundu kumapatsa anthu kuthekera kodzitezeza, ndikupanga zisankho zawo, kupanga ndondomeko zawo, kukwaniritsa zokhumba zawo komanso kuyankhula maganizo awo, mosakakamizidwa ndi zofuna za ena, kaya anthu kapena boma.

Katundu, komanso malamulo a malonda ndi kusinthana omwe amabwera nawo, amawalola anthu kugwira ntchito limodzi mwamtendere mopindulira onse. Zimawathandiza kukhalirana wina ndi mnzake ndi kugawana zinthu zachilengedwe komanso zipatso za thukuta lawo potengera malamulo omwe adagwirizana, popanda mikangano, chisokonezo ndi kuumirizana.

Katundu samangopititsa patsogolo mgwirizano wa mtendere okha; amapangitsa mgwirizanowu kukhala wofunikira kwa wina aliyense yemwe akufuna kutukula mbali yake. Anthu sangangotenga chomwe akufuna pogwiritsa ntchito mphamvu. Katundu atha kupita kwina – kugulitsidwa, kubwerekedwa, kugawidwa, kapena kuperekedwa – pokhapokha mwini wake atavomereza. Mayiko a ufulu kwambiri ali ndi njira zokhwima zotetezera ufulu ofunikawu, monga malamulo obwezera ngongole ndi kulemekeza mgwirizano. Anthu a ufulu

Maziko a dziko la ufulu

amaona izi ngati njira yabwino yoperekera kwina katundu kusiyana kuti atengedwe mokakamiza kapena kuberedwa mwachinyengo.

Gawo ladera

Anthu amene ali ndi katundu samapindula okha pa zonsezi. Popititsa patsogolo mchitidwe woika ndalama mu mabizinezi, kupanga mpamba ndi malonda, dera lonse limapindula. Mwachitsanzo, anthu okhala mumzinda omwe alibe minda amadya, kaamba ka chilimbikitso cha alimi omwe amalima ndi kusamalira mbeu zawo ndi kuchita malonda mosaumirizidwa ndi makasitomala. Izi zili chomwechi chifukwa cha ufulu wa alimi wokhala ndi malo awo komanso mbeu zawo. Ndipo zotsatira za izi nzosiyana ndi m'mayiko amene ufulu pa katundu sunatetezedwe – mwachitsanzo, ku Zimbabwe mu ulamuliro wa Robert Mugabe, koma anthu ankalmibikitsidwa kutenga minda ya alimi okhazikika ngati yawo. M'mene alimi (ambiri achizungu) ankathawa, zotsatira zake sizinali kutukuka kwenikweni koma kubwerera m'mbuyo: popanda malamulo omveka bwino okhudza malo, kapangidwe kazinthu kanatsika ndipo anthu okhala m'mizinda anasowa chakudya.

M'dziko la ufulu, kuteteza ufulu wa anthu kukhala ndi katundu ndi udindo wofunikira wa boma. Umathandiza anthu kudziteteza okha ku mchitidwe wokakamizidwa ndi zigawenga komanso ndi olamulira kapena andale ochita bwino. Kupereka umwini wa katundu umampatsa aliyense gawo mudera komanso chidwi chogwirizana mwamtendere. Aliyense amapindula ndi ufulu pa katundu zomwe zimalimbikitsa kusamala ndi kugwiritsa ntchito bwino katundu wako, kupangitsa kuti mpamba upangidwe ndi kukhazikika. Umwini wa katundu mudziko la ufulu simwayi kwa anthu ochepa okha. Ndiwoyenera aliyense ndipo zimapindulira aliyense.

Malamulo achilungamo

Kupeza chilungamo

Chilungamo chimaimirira malamulo omwe mphoto ndi chilango zimaperekedwa. Chimatengera m'mene timamvera ngati anthu za

zomwe anthu akuyenera kulandira potsatira zomwe achita. Mwachitsanzo, ngati munthu wavulaza mnzake mwadala, anthu ambiri amagwirizana kuti akuyenera kumpepesa ovulalayo komanso kupereka chilango pa cholakwikacho.

Malamulo achilungamo sichinthu chomwe tingangokhazikitsa paife tokha. Ndi gawo la umunthu wathu. Anthu ena amakhulupirira kuti lamulo lachilengedweli limaperekedwa kwaife ndi Namalenga ndipo limavumbulutsidwa kwa ife kudzera mu chipembedzo chathu. Ena, monga katswiri wazachuma komanso kaganizidwe kozama wotchedwa F. A. Hayek, ali ndi ganizo la kusintha pakokha kwa zinthu, ponena kuti malamulo achilungamo akula limodzi nafe chifukwa amatithandiza kukhala mwamtendere limodzi ngati anthu ochitira zinthu pamodzi. Njira iliyonseyo, zikuoneka kuti tili ndi kumva kwachibadwa kwa chilungamo zomwe zimapititsa patsogolo mgwirizano ndi dziko loyenda bwino. Tikanakhala tilibe kumva kotero komanso kusamva kulakwiridwa – tikanakhala osachitapo kanthu pamene anthu aberedwa kapena kuphedwa – sitikanakhala moyo nthawi yayitali.

Nthambi yopanga malamulo komanso akhothi m'dziko la ufulu kotero sangalamulire kuti chilungamo chikhale chani. Malamulo alionse omwe angaganizire sangagwire ntchito bwino kusiyana ndi omwe ali gawo la chilengedwe chathu. Chomwe angayembekezere kuchita ndikupeza chenicheni chomwe malamulo achilungamo ali²³.

Wina atha kuona izi mmene malamulo ochokera ku chikhalidwe amagwirira ntchito komanso dongosolo la mmene malamulo amayendera kudera. Milandu pakati pa anthu – milandu ya malire pakati pa anthu oyandikana, mwachitsanzo – imatengeredwa ku khothi. Khothi liyenera kugamula mwachilungamo, potengera mmene mlanduwo ulili. Mlandu wa malire wina utha kukhala ofanana munjira ina komanso osiyana munjira ina, ndipo khothi limayetsetsa mwanjira ina kuti ligamulenso mwachilungamo. Oweruza mlandu samangopereka chigamulo mopanda dongosolo. Amagwiritsa ntchito

²³ This point is made in F. A. Hayek, *The Mirage of Social Justice*, University of Chicago Press, Chicago, IL, 1978.

Maziko a dziko la ufulu

mfundo zakale zovomerezeka ku milandu yatsopano. Ndipo kudzera munjira yoyesera komanso yayitali chonchi, pang'onopang'ono amafika pogwirizana za khalidwe la anthu oyandikana lomwe lili la chilungamo komanso lomwe lilibe chilungamo.

Chilungamo si lamulo, khalidwe kapena kufanana

Nsanamira yofunikira kwambiri ya malamulo achilungamo m'dziko la ufulu ndiyakuti ayenera kufikira kwa aliyense mofanana. Anthu osiyana mu zochitika zofanana ayenera kuthandizidwa mofanana.

Malamulo ndi chilungamo sinthawi zonse amakhala chinthu chofanana. Mwachitsanzo, malamulo sangathandize anthu nthawi zonse mofanana. Atha kupangidwa ndi andale odziwika pazifukwa zofuna kuthandiza anzawo ndi kupweteka adani awo. Awa ndi malamulo olakwika.

Chilungamo ndi makhalidwe sizinthu zofanananso. Anthu ambiri atha kuona kugonana kwa anthu asanalowe m'banja kuti simakhalidwe oyenera. Koma zimenezo sizikupangitsa mchitidwewo kukhala wosalungama. Palibe aliyense yemwe amapwetekedwa ndi mchitidwe wogwirizana ngati uwu; koteropotengera mfundo yosapwetekana, ndikulakwa kupereka chilango kwa anthu omwe akuchita mchitidwewu. Komanso malamulo omwe amachita izi siachilungamo. Ngati lamulo lingapereke chilango kwa anthu chifukwa akuliona khalidwe lawo kuti ndilolakwika, sipangakhale ufulu kwa wina aliyense.

Chimodzimodzi kufanana, sichimodzimodzi ndi chilungamo. Chifukwa choti ena ndiachuma ena ndiwosauka sichikupanga dera kukhala lopanda chilungamo. Dera la anthu osiyana litha kukhala lachilungamo mofanana ndi dera la anthu ofanana. Ngati anthu akupeza katundu wawo movomerezeka komanso mopanda kuopseza, akuchita izi mwachilungamo.

Anthu ena omwe amatsutsa mfundo yokhala ndi katundu wa anthu wamba amati katundu otero amatha kuchokera ku mchitidwe wakuba. Izi sizooona. Anthu oyamba omwe anaswa mphanje pa ntchire losalimidwa komanso losafunidwa sanapweteke wina aliyense. Choncho ngati anapindula pochita ulimi kapena kupezapo miyala

yamtengo wapatali, unali mwayi wawo: palibe aliyense anapwetekedwa, kotero palibe cholakwika chomwe chinachitika. Chimodzimodzi, ngati wochita malonda wayambitsa chinthu chatsopano kapena njira yopangira zinthu yatsopano, nkukhala ndi chuma atagulitsa zinthuzo kwa anthu ofuna, palibe yemwe wapwetekedwa: mosiyanita, dziko lonse limapindula ndi chatsopanochi.

Kulimbikitsa chilungamo

Cholinga chachikulu cha dziko la ufulu ndi kuchepetsa kugwiritsa ntchito mphamvu. Koma chilungamo chiyenera kulimbikitsidwa penapake. Ngati anthu akupweteka anzawo, timayembekezera kuti alandire chilango monga chindapusa kapena kupititsidwa kundende. Zomwe zikutanthauza kugwiritsa ntchito mphamvu pa wolakwayo. Ngati chilungamo chingakhalepo, kukakamiza kwinakwake ndikovomerezeka.

Dziko la ufulu limathana ndi kusungulumwaku popereka mphamvu yokakamiza kwa adindo ena. Okhawo ndiwomwe angagwiritse ntchito mphamvu, komanso pokhapokha akulimbikitsa chilungamo ndi chitetezo cha nzika za dziko kwa adani akunja ndi amkati mwa dziko omwe. Kugwiritsa ntchito mphamvu anthu ena ndikosaloledwa

Ngati boma lingakhale ndi mphamvu zonse pokakamiza, liyenera kukhala ndi malire. Boma limapangidwa ndi anthu, ndipo palibe munthu angakhulupiridwe kuti angagwiritse ntchito mphamvu zokakamiza mosakondera. Mayesero ozigwiritsa ntchito mwakufuna kwake ndi aakulu.

Motero, dongosolo la chilungamo m'dziko la ufulu limaphatikiza malamulo okhwima oika malire pakagwiritsidwe ntchito ka mphamvu zokakamiza za adindo. Mwachitsanzo, payenera kukhala malamulo okhwima pa mphamvu za atsogoleri pofufuza ndi kumanga, m'mene milandu iyenera kuzengedwera, komanso mmene zilango ziyenera kuperekedwera. Malamulo akapangidwe ka zinthuwa akukhudza mmene ziganizo zimapangidwira, osati chomwe chagamulidwa. Malamulo awa ayenera kutsatidwa kuti dongosolo loweruzira milandu likhale losakondera komanso lachilungamo.

Maziko a dziko la ufulu

Ziopsezo za chilungamo

Ndondomeko imeneyi iyenera kukhala yamphamvu ngati anthu angazengedwe milandu mwachilungamo ndi atsogoleri omwe ali ndi mphamvu zokakamiza. Zimalakwika mosavuta, ngakhale ndi anthu omwe akuganizira kuti akuchita izi mwachilungamo. Mwachitsanzo, Oweruza milandu, nthawi zina amaganiza kuti ntchito yawo ndikupanga zotsatira kukhala zosakondera m'malo motsata ndondomeko zoweruzira milandu. Koma mchitidwe wofuna kusakondera poweruza milandu umapanga maganizo a oweruza kukhala oposa chilungamo. Komanso zimapangitsa zotsatira za makhothi kukhala zosadziwikiratu: mlandu wofanana utha kupatsidwa zilango zosiyana, motengera oweruza wina. Ndipo zimapangitsa olamula kukhala ndi mphamvu pa zotsatira za makhothi: ngati angachite katangale kapena kuopseza oweruza, atha kusinthitsa chilango cha anthu. Koma ngati pali mfundo zokhwima zomwe zikuyenera kutsatidwa poweruza mlandu uliwonse, mphamvu izi zimathetsedwa. Ichi ndi chitetezo champhamvu kwa omwe amapita kukhothi.

Njira ina yomwe imasokoneza kaperekedwe ka chilungamo ndi ganizo la 'chilungamo cham'dera'. Kupanga mwadala njira zogawira ndi kufananitsa chuma ndi ndalama zimatsutsana ndi mfundo za katundu ndi chilungamo. Pofuna kugawana mofanana, katundu ayenera kutengedwa m'manja mwa anthu ena ndi kuperekedwa kwa ena. Malamulo aumwini omwe amapatsa anthu ufulu okhala ndi katundu ndi kumupereka m'mene asankhira, ayenera kuphwanyidwa. Komanso, tikangopereka mphamvu zonse kwa atsogoleri, palibe angakhale otetezeka. Ntchito zamalonda zidzalowanso pansi: munthu afuniranji kuyesetsa kapena kuika mphamvu zake kuti apeze katundu, ngati adindo angadzamulande?

Malamulo enieni omwe amagwira ntchito kunkhani yaumwini wa katundu samakhala odziwikiratu nthawi zonse. Kodi umwini wanga pa malo ukundipatsa ufulu wogwiritsa ntchito miyala yamtengo wapatali ili pansi pakepo? Kodi ukundilola kuletsa anthu kuulutsa ndege pamwamba pakepo? Kodi ndingaletse fakitale yomwe yaya-ndikana nawo kuwononga mpweya wanga kaamba ka utsi wake?

Zonsezi ziyenera kuganiziridwa²⁴. Ndipo m’dziko la ufulu zimayesedwa, ndipo zikupitirira kuyesedwa ndi kukonzedwa ndi makhothi, ndi oweruza osakondera omwe amayesetsa kutsatira malamulo enieni achilungamo.

Chilungamo chachibadwa

M’dziko la ufulu, mchitidwe wonse wopanga malamulo ndi kuone-tsetsa kuti akutsatidwa ukuyenera kutsata mfundo za chilungamo – mfundo zomwe ndizochokera ku umunthu wathu moti zimatchedwa chilungamo chachibadwa.

Choyamba, lamulo liyenera kukhala lodziwika, lomveka bwino ndi losakaikitsa. Ngati lamulo lili lachinsinsi kapena likusinthasintha, anthu sangadziwe ngati akuliswa, kotero sangadziteteze kuti asaimbidwe mlandu.

Malamulo ayeneranso kukhala odziwikiratu. Anthu sakuyenera kumangoziganizira pomwe lamulo likugwira ntchito ndipomwe lisakugwira ntchito, ndi zotsatira zake zokuswa lamulolo. Ngakhale m’mayiko ooneka a ufulu, malamulo amayambitsidwa nthawi zambiri pa cholinga chimodzi – monga kuthetsa mchitidwe wa uchifwamba kapena umbava ogwirizana – akatero amagwiritsidwira ntchito pa cholinga china chosiyaniranatu. Nzika zitha kumalandira zilango-zokhwima pa milandu yomwe ili yaying’ono.

Chachiwiri, malamulo sangakhale oyang’ana m’mbuyo. Ayenera kugwira ntchito pa zochitika mtsogolo. Kupanda apo, anthu atha kupezeka akuzengedwa milandu yazomwe anachita zimene zinali zoyenera munthawi imeneyo. Koma, mayiko ooneka ngati afulu amalephera pamenepa. Mwachitsanzo, lamulo lamu 2008 ku United Kingdom linasintha lamulo lopewa msonkho munjira yomwe inakhudza anthu zikwi zitanu omwe ankachita moyenera nthawi imeneyo.

Lamulo lachitanu la chilungamo ndilakuti malamulo sangafunse anthu kupanga zinthu zosatheka, chifukwa izi zipangitsa kukhala

²⁴ This point is raised by Milton Friedman and Rose Friedman, *Capitalism and Freedom*, University of Chicago Press, Chicago, IL, 1962.

Maziko a dziko la ufulu

kovuta kuti anthu apewe kuphwanya malamulo. Ngakhale mayiko otchedwa a ufulu amalephera mayeso amenewa, makamaka pomwe malamulo akutsutsana: mwakuti malamulo oona za ngozi za moto akhoza kufuna mwini wake kuika zotetezera ku moto pa nyumba zomwe malamulo oona za ndondomeko amaletsa kusinthidwa – mwanjira iliyonse, mwini nyumbayo akuswa lamulo. Mosokoneza kwambiri, maboma opanda chilungamo atha kugwiritsa ntchito malamulo osatheka mwadala pofuna kuzunza adani awo.

Lamulo lina lofunikira la chilungamo cha chibadwa ndilo ganizo la kusalakwa. Palibe yemwe angatengedwe ngati olakwa pokhapokha atatsimikizidwa motero, ngakhale mlandu ungakhale oonekeratu. Izi zikutanthauza kuti zikutengera adindo kuti asonyeze kulakwa kwawo osati kuti asonyeze kusalakwa kwawo. Izi zimapangitsa boma kuvutika kuti lizunze adani ake ndi milandu yokonzerana: milandu yonse iyenera kutsimikizidwa ndi akhothi anthu asanalandire chilango.

Mfundo yomaliza yofunikira ndiyakuti oweruza milandu ndi makhothi ayenera kukhala oima paokha mosalamuliridwa ndi atsogoleri andale. Payenera kukhala kusiyana kwa mphamvu pakati pa opanga malamulo ndi omwe amatanthauzira ndi kupereka chiweruzo. Oweruza milandu sakuyenera kungokhala mthumwi za andale: maganizo awo pandale akuyenera kukhala osafunikira ndi m'mene akugamulira milandu. Ngati oweruza milandu ali anzawo a andale mokuti amatha kuwalamulira kapena kuwaopseza, ndekuti ndondomeko za khothi zimatumikira andale osati chilungamo chenicheni. Mayiko a ufulu kawirikawiri amakhala ndi nthumwi zoima pazokha zomwe zimasankha oweruza milandu, kapena kuwasankha kwamuyaya, zomwe zimachepetsa mphamvu za andale pa iwo.

Mphamvu ya lamulo

Tanthauzo la mphamvu ya lamulo

Palibe chomwe chimasiyanitsa bwino mayiko a ufulu ndi opanda ufulu koposa mphamvu ya lamulo. Ili ndi ganizo lakuti nzika ziyenera kulamuliridwa ndi malamulo omveka bwino komanso

ofikira aliyense osati maganizo chabe a mafumu kapena andale. Opanga malamulo sangangochita kanthu mmene akufunira. Malamulo awo ayenera kufikira kwa aliyense, kuphatikiza iwo eni.

Cholinga cha mphamvu ya lamulo ndikuteteza anthu ku mchitidwe wogwiritsa udyo mphamvu. Ngati tingalipitse boma mphamvu zonse, tiyenera kuonetsetsa kuti mphamvu zikugwiritsidwa ntchito ku cholinga chenicheni, modziwikiratu, mosakaikitsa komanso kuti dera lonse lipindule, osati kagulu kochepa.

Mphamvu ya malamulo imaonetsetsanso kuti omwe ali ndi udindo akulandiranso chilango chofanana akalakwa monga aliyense. Mayiko ambiri amapereka chitetezo kwa atsogoleri awo atsopano ndi akale omwe kuti asazengedwe milandu – ndipo mapeto ake, atsogoleri ambiri oterewa athawa chilungamo. Ngakhale nkwabwino kuteteza atsogoleri adziko – ndi aliyense – ku nkhani zongowapekera (kapena zoipitsirana mbiri pa ndale) ndi kuzengedwa kosiyanasiyana, palibe chifukwa chowatetezera ku chilungamo chenicheni.

Mphamvu ya lamulo, kotero, imagona pa mfundo zofikira aliyense komanso zokhalitsa, kusiyanana ndi ziganizo zosinthasinthana komanso zongopangidwa ndi atsogoleri. Izi zimatitsimikizira chilungamo chachibadwa kudzera m’ malamulo monga kufanana pa lamulo, dongosolo lonse la malamulo, kuima paokha kwa makhothi, chilungamo chakhungu, *habeas corpus* (kusungidwa nthawi yayitali osazengedwa mlandu), osazunzidwa ndi adindo (monga kuzengedwa mlandu womwewo kambirimбири), kuganiziridwa kuti ndiwosalakwa (monga kutengedwa osalakwa mpaka utapezedwa olakwa ndi kupatsidwa chilango) ndi kudziwikiratu, kukhazikika, ndi kuthekera kwa malamulo. Komanso chofunikira kwambiri, omwe amapanga malamulo nawonso ayenera kuwatsatira ngati wina aliyense. Dziko silingakhale la ufulu ngati anthu ena, kaya amapatsidwa ulemu motani, sakufunsidwa kuti alongosole pa zomwe achita.

Kuteteza mphamvu ya lamulo

Mayiko ali ndi njira zosiyanasiyana zotetezera mphamvu ya lamulo kuwonongedwa ndiwomwe ali m’maudindo. Izi zikuphatikiza malamulo oyendetsera dziko olembedwa, ndondomeko zoyendetsera

Maziko a dziko la ufulu

chilungamo potengera malamulo achikhalidwe ndi zomwe zigamulo zam'mbuyo, ndi kutsatira chilungamo cha chibadwa.

Malamulo oyendetsera dziko olembedwa akhoza kulimbikitsa mphamvu ya lamulo. Koma nzophweka kwambiri kupanga malamulo oyendetsera dziko pamene dziko likuyamba kumene, pamene nzika zikukumana pamodzi koyamba, kusiyana ndi m'dziko lokhazikika kale, komwe osankhika ndi ena ofuna zaiwo okha ali ndi mphamvu ndipo ali ndi kuthekera kosintha malamulo atsopano kuti awapindulire iwo okha.

Mphamvu ya lamulo ithanso kuthandizidwa podutsa zaka pamene milandu yosiyanasiyana ikutengeredwa ku khoti. Anthu atha kutsutsana ndi zigamulo za opanga malamulo ndi adindo, ndi kuyesa chilungamo chawo ndi kuvomerezeka kwawo ku khoti. Mwapang'onopang'ono, zitsanzo za zomwe zakambidwa zimasonyezeratu malire a adindo.

Njira yachitatu yopititsira patsogolo mphamvu ya lamulo ndi kulimbikitsa kukambirana za malamulo achilungamo ndi mfundo zokhazikitsa mgwirizano wa m'dziko. Ngati ufulu woyankhula maganizo ako ulipo, komanso kuti aliyense ndiwololedwa kuyankhulapo maganizo amenewa, kumakhala kovuta kuti atsogoleri atembenuze kamvetsedwe kake mowakomera iwo.

Mfundo yayikulu yomwe imatuluka mu kukambirana za mphamvu ya lamulo ndiyakuti, ngati anthu akubwera pamodzi koyamba kuti asankhe mfundo zomwe zikuyenera kuwalamulira, palibe angavomere kuti azikakamizidwa ndi ena, kupatula munjira zina – monga chilango ukaba kapena chiwawa – zomwe angazione kukhala zofunika kwa iwo kwanthawi yayitali. Koteru titha kuganizira molondola kuti mayiko onse a ufulu akuyenera kutsatira malamulo ovomerezeka kwa aliyense omwe amaletsa kukakamizana ndi kuletsa kagulu ka anthu kukhala ndi kuthekera kopondereza anzawo.

Kuyendetsa chilungamo

Ngakhale pali njira zambiri zosankhidwa pofuna kuteteza mphamvu ya lamulo, pali njira zina zapadera zomwe zimathandiza kwambiri.

Oweruza milandu ayenera kukhala oima paokha pa iwo eni komanso pandale. Kupanda kutero ndondomeko ya makhothi siyingalemekezede, zolakwika zambiri zitha kumachitidwa mu dzina lachilungamo. M'mayiko ambiri, oweruza milandu ambiri samalipidwa mokwanira, samakhulupirika komanso samayang'aniridwa mokwana: kotero amapereka chiganizo potengera ziphuphu zawo osati lamulo. M'malo mwake, oweruza milandu ayenera kulipidwa mokwanira komanso kuunikidwa pafupipafupi kuti katangale asakhale ofunika kapena kuloleredwa.

Ndondomeko ya chilungamo iyenera kuthandizidwa ndi kayendetsedwe kabwino ka makhothi. M'mayiko ambiri zitha kutenga miyezi kapena zaka kuti ngakhale mlandu wawung'ono ufike ku khothi chifukwa cha mndandanda wa adindo omwe nkhaniyo ikuyenera kudutsamo komanso kupanda chidwi kwa adindo kuti ayendetse mlanduwo. Ndondomeko yoweruzira milandu potengera milandu yam'mbuyo imafunika kufikirika msanga milandu yakale ndi ziweruzo, kotero milandu yopita kukhothi siyimakhala yosafunikira chifukwa palibe pomwe anasunga ziweruzo za milandu zakale.

M'mayiko ambiri, apolisi alinso mbali ya vuto m'malo mokhala yakho. Chifukwa cha mphamvu zawo zogwira ndi kumanga, atha kulakwira kwakukulu anthu ndi kudzipindulira okha kudzera mu ziphuphu. Apolisi apamsewu opereka chindapusa chochepa ku milandu yeniyeni kapena yongoganiziridwa ndi zofanana ndi zomwe zikukambidwazi. Zimakhala mbali ya khalidwe lochitika – koma pamene mfundo ya ziphuphu yavomerezedwa, palibe lamulo lingaletse choipa chilichonse. Apolisi ayenera kuphunzitsidwa bwino ndikuyang'aniridwa, makamaka ndi bungwe loima palokha lomwe lingapatsidwe mphamvu kufufuza ndi kuchitapo kanthu pa madandaulo okhudza apolisiwa.

Momwemonso maudindo ayenera kusankhidwa moyenerera, osati kaamba ka kukonderedwa ndi andale. Akuyenera kufotokozero bwino. Kupanga ziganizo pofuna phindu pandale kapena phindu la munthu kuyenera kulandira chilango.

Maziko a dziko la ufulu

Kuti chilungamo ndi mphamvu ya lamulo zigwire ntchito, zisankho ziyenera kuyendetsedwa mosakondera. Payenera kukhala ufulu wolankhula kuti oimirira omwe akutsutsa atsogoleri akhoza kuima ndi kuyankhulapo maganizo awo. Payeneranso kukhala mavoti achinsinsi komanso bungwe loima palokha loyendetsa zisankho kuti lionetsetse kuti malire a zisankho agawidwa mosakondera ndipo zisankho zikupangidwa mwachilungamo.

Chilungamo ndi kutukuka pa chuma

Mphamvu ya lamulo ndiyofunika pa chuma komanso pankhani ya ubale wa anthu. Chaka chilichonse, banki yayikulu padziko lonse lapansi imaika pamndandanda mayiko molingana ndi kuthekera kochita nawo malonda. Kupereka chikoka cha mabizinezi akunja ndi kuphweketsa ntchito zamalonda m'dziko, ndi chinthu chofunika kwambiri pa chuma komanso chitukuko cha anthu onse. Mndandandawu umatengera kusabisa pamsonkho komanso malamulo, mlingo wa katangale pakati pa adindo, ndi m'mene anthu amayambira bizinezi mosavuta, kulembetsa katundu, kupanga malonda ndi anthu amayiko ena, kulephera kubweza ngongole ndi zina zotero.

Dziko la Singapore, lomwe lili dziko la ufulu kwambiri pa chuma (ngakhale lili ndi ufulu ochepa pa kakhaliidwe ka anthu), lakhala pamwamba pa mndandandawu dziko lonse lapansi zaka zisanu ndi ziwiri zapitazi, motsatizana ndi mayiko ena a ufulu monga Hong Kong, New Zealand, Denmark, the United Kingdom ndi United States. Kutsatira apo pakubwera dziko la Korea, dziko lina la ufulu pachuma koma la ufulu ochepa pa kakhaliidwe ka anthu. Pansi pa mndandandawu pali mayiko omwe ufulu ndi mphamvu ya lamulo nzofooka kwambiri— monga Congo, Venezuela, Zimbabwe, Iraq, Cameroon, Bolivia ndi Uzbekistan.

Chiopsezo ku mphamvu ya lamulo

M'mayiko ambiri, makamaka ongotukuka kumene, ndondomeko zosiyanasiyana za chilungamo zimapezeka. Kuwonjezera pa malamulo adziko ndi ndondomeko za chilungamo, kawirikawiri pamakhalanso

ndondomeko za malamulo a kudera, mtundu ndi chipembedzo, ngakhalenso malamulo a padera kapena malamulo a mgwirizano pakati pa anthu.

Katangale amakhalapo kwambiri mu kayendetsedwe ka boma. Ndongomeko zamalamulo za kudera, za chipembedzo, kapena za anthu oima paokha nthawi zambiri zimakhazikika kwambiri mu chilungamo cha chibadwa, kotero zimavomerezedwa ndi ambiri. Mosiyanita, ndondomeko za boma, mosiyana, zinangokhazikitsidwa ndi atsamunda kapena omwe anatenga ulamuliro. Zikhoza kukhala zosavomerezeka kwenikweni ndi ambiri, koma mphamvu zake ndi anthu ozitsatira zimatsalira kwa munthu aliyense kuti azigwiritse ntchito molakwika.

Anthu omwe ali m'boma komanso ogwira ntchito m'makhothi aboma samaona cholakwika kugwiritsa ntchito molakwika mphamvu zaboma. Asirikali, apolisi ndi adindo amalandira ziphuphu. Andale ali ndi kuthekerera kobera boma kuti athandize dera lakwawo, kapena iwo eni. Koma zomwe zimatengedwa kukhala zolakwika pa umoyo wa munthu ziyeneranso kuonedwa zolakwika kugulu kwa anthunso.

M'malo amene kuyenda ndi kulumikizana nkovuta komanso nkhani zakudera zili zofunika changu komanso zovutirapo, kuphatikiza ndondomekozi kukhoza kukhala ganizo labwino. Koma cholinga chiyenera kukhala chakuti ndondomeko zonse za chilungamo zikhale ndi mphamvu ndi kuvomereza kwa malamulo akudera, kumvetsetsa ndi mfundo za malamulo adziko, komanso kusayang'ana mbali kwa mphamvu ya lamulo.

Ufulu wa anthu

Kutanthauzira ufulu wa munthu

Kuchokera mu kukambirana za chilungamo pakubwera ganizo la chilungamo²⁵. Ili ndi ganizo lakuti anthu ali ndi ufulu wowayenera kaamba ka umunthu wawo – ufulu omwe, ngati lamulo lachibadwa,

²⁵ For more on this, see Nigel Ashford, *Principles for a Free Society*, Jarl Hjalmarson Foundation, Stockholm, 2003.

Maziko a dziko la ufulu

umapititsa patsogolo kayendetsedwe kabwino ka dera, koma ufulu omwe umavomerezedwa padziko lonse lapansi (kugwira ntchito pali-ponse ndi kwa aliyense) ndi osamanidwa (sungangosiyidwa kapena kukanizidwa ndi ena)

Ufulu wa anthuwu utha kuchulidwa bwino ngati kumasuka kwa anthu. Amaphatikiza kumasuka kwina ngati umwini wa katundu, kudzidalira ndi umwini wa thupi lako ndi ntchito yako, ufulu oyenda ndi kukhala komwe ukufuna, komanso ufulu opembedza chipembedzo chako. Zotsatira zake ndi kupereka malire a mmene boma lingachitire ndi anthu.

Mwatsoka, ‘ufulu wa anthu’ umasokonezedwa nthawi zambiri ndi ufulu pamalamulo omwe umaperekedwa mu ndondomeko ya ndale kapena potengera chikhalidwe cha m’dera. Mwachitsanzo, Malamulo owapatsa anthu ogwira ntchito masiku opuma, si ufulu wa munthu chifukwa siwadziko lonse lapansi. Umagwira ntchito kwa olembedwa ntchito okha komanso m’mayiko okhawo omwe kusangalatsaku amakukwanitsa. Ndiponso utha kuchotsedwa, ogwira ntchito atha osatenga masiku opuma powasinthanitsa ndi ndalama, osataya ufulu uliwonse. Chimodzimodzi, malamulo a malipiro ofanana kwa amuna ndi akazi omwe si ufulu wamunthu chifukwa sakudandaula ufulu wamunthu koma ndi khumbo lokakamiza la olemba ntchito.

Ufulu wa gulu la anthu si ufulu wa munthu. Sumagwira ntchito pa aliyense. Kuthandizidwa mwapadera koperekedwa, monga, kwa anthu omwe anayamba kukhala m’dziko la Amerika ndi mwayi chabe operekedwa ndi malamulo: anthu ena alibe mwayi umenewo. Chinthu sichingakhale ufulu wamunthu ngati sichikuyang’anira umunthu wamunthu koma umembala wokha gulu lapadera.

Kumasuka, ufulu ndi udindo

Ndikofunika kumvetsetsa zinthu zimenezi. Kusokoneza ufulu wa anthu ndi makhalidwe a kudera ndi mwayi operekedwa ndi lamulo zimapereka mphamvu zolakwika ku ganizo lachiwirili ndi kuponde-reza ganizo loyambali. Ngakhale zinthu zina – malipiro ofanana, malipiro amasiku opuma, ngakhale kupereka ulemu mwapadera kwagulu losawerengedwa konse – zitha kukhala zokhumbika, chilungamo ndi chakuti sichilichonse chokhumbika chomwe chili ufulu wa munthu.

Maziko a dziko la ufulu

Ufulu wa munthu umatsimikiza kumasuka kwathu – sumapereka chikakamizo pa wina aliyense. Kumasuka poyankhula, mwachitsanzo, sikumayika udindo kapena ntchito pa aliyense koposa udindo ndi ntchito youlemekeza. Palibe yemwe akuyenera kukupatsa malo osindikiza nkhani zako mu nyuzipepala, kapena pologalamu pa wailesi kuti maganizo ako aulutsidwe kapena kuthandiza kuti uyankhuledi momasuka, kapena kumvetsera zomwe unganene.

Mosiyana, chilamulo cha ufulu wa anthu cha bungwe la Mgwirizano wa mayiko onse dziko lapansi adaika maphunziro aulere. Koma maphunziro aulere siufulu wamunthu chifukwa izi zikutanthauza kuti ena akuyenera kulipira. Kupereka maphunziro kuli ndi mtengo wake – nthawi, mphamvu, zophunzitsira ndi ndalama zonse zimagwiritsidwa ntchito powapereka. Mu dziko lenileni la ufulu, palibe yemwe ali ndi ufulu olandira maphunziro mwaulere, chifukwa izi ziika udindo pa anthu ena kuti apereke zinthu zotero. (komabe, anthu ambiri akhoza kutengapo mbali kugawana mtengowo: koma dziko la ufulu silingawakakamize.)

Nthawi zambiri, anthu amakamba za ufulu osatchulapo, kapena kuzindikira chabe, za udindo omwe ali nawo paena, chiumirizo chomwe chimafunika kuti ugwire ntchito, ndi kuwononga kwakukulu komwe chiumirizochi chimapanga.

Mobwerezanso, palibe ufulu wa umoyo m'dziko la ufulu: zimene zikutanthauza kuti anthu ena ali ndi udindo othandiza anzawo, pamene udindo okhawo uli wosawapweteka. Koma izi sizikutanthauza kuti anthu osauka kapena aulumali ndiwopsinjika kwambiri kuposa mu chikhalidwe chosamalira umoyo wa anthu. Msonkho wa ndalama zoyang'anira umoyo ikhoza kubwezeretsa m'mbuyo ntchito ndi zamalonda, kupangitsa dziko lonse kusauka, ndipo kupindula pa umoyo kukhoza kulimbikitsa moyo wodalira. Ndipo mabungwe azachifundo m'mayiko achuma komanso a ufulu atha kuthandiza bwino osowa kusiyana ndi mabungwe olamuliridwa ndi boma.

7. DZIKO LOSAKAKAMIZIKA

Kulamula popanda lamulo

Dziko la ufulu liitha kudziyendetsa lokha popanda kufuna boma lalikulu. Izi zitha kumveka zodabwitsa, koma umoyo wamunthu uli ndi zitsanzo. Monga katswiri pa kayendetsedwe kazachuma waku America Daniel B. Klein akuonera, utha kuganiza za malo ochitira masewero othamanga ndi nsapato zamateyala– ndi anthu pafupifupi zana kapena kuposera apo kuchokera kwa ana kufikira agogo, ndi mateyala oikidwa pansu pa nsapato zawo opanda zipewa zotetezera, zoteteza m’ mabondo kapena maphunziro othamangira, onse kumazungulira pa simenti youma pa mlingo wosiyanasiyana – patha kukhala ngozi zosiyanasiyana. Koma, chilungamo chake, otsetserekawa amakwanitsa kupeza njira yawo mozunguliramo, kupewa anzawo, popanda kuika malire a liwiro, zizindikiro za pokhotera ndi magetsi oimitsira²⁶. Sizifunika wina wa ndondomeko kapena opanga mfundo kuwauza liwiro lomwe angathamangire. Poziyang’anira iwo eni, ndi kupereka ulemu kwa ena, amakwanitsa cholinga chawo chosangalala kwina akupewa kukhulana.

Ngakhale mochititsa chidwi, chiyankhulo cha anthu ndicholongosoka ndi chotithandiza kwambiri, ngakhale sichinakonzedwe ndi ulamuliro uliwonse. Malamulo achiyankhulo omwe amachipangitsa chiyankhulo kugwira ntchito akula paokha m’zaka mazana zapitazi, chifukwa amatithandiza kumvetsetsa wina ndi mnzake. Timawatsata malamulowa ngakhale ali osamvetsetseka bwino komanso ovuta ndipo titha kuvutika kuti tiwalembe bwino. Palibe bungwe la boma lomwe lingapange malamulo ovuta choncho, ochenjera ndi ogwira bwino ntchito. Malamulowa akhala akusintha ndi ife.

Magawo ambiri a moyo wamunthu amayenda chonchi. Posatengera kuuzidwa ndi adindo m’mene zikuyenera kukhalira, anthu timachita mwadongosolo, mobwerezabwereza, modziwikiratu, pongotsata malamulo okhazikika omwe takula nawo kukhala mbali imodzi ya

²⁶ Daniel B. Klein, ‘Rinkonomics: A window on spontaneous order’, Online Library of Liberty (Articles), 2006.

moyo wathu. Powatsatira, timapanga malamulo am’dera otithandiza kwambiri. Mwachitsanzo, malamulo osavutawa omwe amatilola kupanga malonda ndi anthu ena mwantendere, apangitsa msika wa mayiko onse padziko lapansi omwe kudzera mwayiwo, dziko lonse limachitira zinthu limodzi.

Mayiko otsogozedwa ndi lamulo

Malamulo pakati pa anthu m’dziko la ufulu amawapatsa anthu mpata kwambiri kusiyana ndi omwe amakhala m’dziko lolamulidwa ndi boma. Anthu omasuka atha kupanga kalikonse pa zinthu zambiri zomwe sizoletsedwa kwenikweni, kusiyana ndi kupanikizidwa kupanga zochepa zomwe adindo amaloleza. Izi zikutanthauza kuti mayiko a ufulu atha kukhala otakasuka ndi ophunzitsika, kuvomereza mosavuta kasinthidwe ka zinthu kusiyana ndi kudikira kulamuliridwa.

Malamulo awa – monga malamulo okhudza umwini ndi katundu pamalonda – amakhala ndi nzeru zina, zomwe zimapezedwa pakapita zaka, zokhudza zomwe zikugwira ndi zomwe sizikugwira. Amasintha pamene nyengo zasintha, kusonyeza mfundo zomwe zapezeka poyesera ndi kulakwitsa mu zaka zapitazi mu kukhalira limodzi kwa anthu. Amakhudza makhalidwe a mmene anthu akuyenera kuchitira ndi ena, malamulo achikhalidwe omwe amayesera kufotokoza malamulo achibadwa polemba, ndi malamulo akudera omwe apezedwa pozenga milandu yosiyanasiyana.

Dziko lotsogozedwa ndi malamulo komanso losakakamizika silongokhala lomasuka poyambitsa zinthu zachilendo komanso lophunzitsika kokha; litha kukhala losokonekera kwambiri kusiyana ndi la ulamuliro ochoka malo amodzi. Monga chiyankhulo, chitha kukhala chovutirapo moti palibe mwaife angalongosole malamulo ake – koma zinthu zimayendabe bwino kwambiri. Dziko loyendera malamulo a adindo sililephera kuikidwa malire, mu kukula komanso zochitika, ku zomwe adindo ochepawa aziganiza. Koma dera lokhazikidwa pa malamulo omwe apangidwa potsatira zochita zochulukira za anthu m’zaka zambirimbiri limakhala ndi nzeru zakuya komanso zotambasuka. Dziko loyendetsedwa kuchokera pakati limayendera nzeru za

Maziko a dziko la ufulu

anthu ochepa; dera loyendetsedwa ndi malamulo limabweretsa pamodzi nzeru za anthu ambiri.

Choncho kulakwitsa komwe amapanga adindo m'boma, ndikwakuti akhoza kupanga ndondomeko ya dera kapena chuma mwabwino komanso mwanzeru kuposa malamulo atsiku ndi tsiku am'dera ndi machitachita azachuma. Posawerengera ndi posintha nzeru zopezeka mu malamulo ovutawa, amasintha zinthu kukhala zoipirabe.

Nzeru ndi mphamvu zomwazika

Nzeru zachibadwidwe za dziko losakakamizika komanso lotso-gozedwa ndi malamulo sizikhalapo kuchokera pa malo ena. Zimappezeka ndi anthu ochulukira mu zochita zawo za tsiku ndi tsiku. Poti mphamvu nzomwazika, anthuwo atha kuyesera zawo, mayeso awo ang'onoang'ono pokhala m'moyo. Atha kuyesera zosayembekezereka komanso mwayi zomwe zingaopseze iwo okha. Koma ngati zomwe ayesera zingapindule, aliyense ali ndi mwayi otengera ndi kupindula nawo. Izi zimapititsa patsogolo kuyesera ndi kutengera zinthu zomwe zikusintha, kulipatsa mwayi dziko losakakamizika kupindula kwakukulu m'dziko losinthatintha. Mosiyantsa, adindo aboma, amapanga zisankho m'malo mwa aliyense, kotero kuika pa chiopsezo moyo ndi chuma cha aliyense. Kotero ayenera kuchita mosamala kusiyana ndi anthu a ufulu – kapena amatha kulakwitsa kwambiri. Mapeto ake, mayiko opanda ufulu amasintha ndi kuchita bwino mochedwa.

Komabe, dziko ndi kayendetsedwe ka chuma ka ufulu sizingakhale za ngwiro. Ndi chipatso cha zochita za anthu (ngakhale sizokonzana munthu) ndipo anthu sangakhale angwiro. Sitingalose zakutsogolo, mwachitsanzo, kotero timalakwitsa poyesera kufikira kusinthikako. Ndipo uthenga omwe aliyense mwaife alinawo ndiwochepa komanso wotengera kudera. Koma m'dziko lomwe anthu ali ndi ufulu ochitira zinthu limodzi, uthenga woche pawu komanso wotengera kuderawu umayendetsa nzeru zamphamvu komanso dziko lomwe latengera zinthu komanso zachuma.

M'dziko la ufulu, anthu ayenera kupeza njira zawo zotolerana ndi ena – omwe nawonso akuyesera kutengera zochita za aliyense. Izi ndingat pa sitieshoni ya njanji yotangwanika munthawi yomwe aliyense akuyesera kuzipezera njira yake mu imodzi mwa zipata zotulukira zochuluka, kapena kulowa mu imodzi mwanjira zolowera ndi kukapeza sitima yomwe akufuna kuyendera. Aliyense maso amayang'ana komwe akupita, ngakhale njira yawo mwina siyikhala yolondoleratu komwe akupita. Ayenera kulowanalowera ndi anthu ena, omwe nawo akuchita chimodzimodzi, kusintha njira pomwe ena akulowa munjira yawo. Zitha kuoneka ngati chisokonezo, koma aliyense amakafika komwe akupita popanda kukangana. Ngati adindo ena akanati aziwauza anthu ochuluka chotere mu sitieshoniyo kwenikweni komwe akupita komanso nthawi yonyamuka, zikanatenga maola ambiri kapena masiku, ngakhale mmodzi mwaiwo asananyamuke kupita kulikonse. Vutoli ndilalikulu kwambiri kuti lingathetsedwe ndi atsogoleri. Koma dziko losakakamizika limathetsa vutoli mosavuta ndinso munthawi yake.

Kulolerana

Tanthauzo la kulolerana

Munjira iyi, anthu mu dziko la ufulu ayenera kuzolowera zochita za ena. Kotero nkofunika kuti anthu aonetse kulolerana ndi anthu ena – kuphatikizira omwe zochita zawo ndi makhalidwe awo samagwirizana nawo kapena amaoneka odabwitsa.

Mu dziko la ufulu sitingaletse munthu kupanga zinthu chifukwa chakuti sitikugwirizana nazo. Tikhoza kulowererapo ngati zochita zawo zili ndi kuthekera kovulaza ena. John Stuart Mill ananenetsa kuti izi zikutanthauza kuvulala kwathupi. Ngati kuvulala kungaphatikize zinthu zina monga kuzizimuka, kunyansidwa ndi chikhalidwe kapena kuchititsidwa manyazi, ndekuti pafupifupi chochita chilichonse chikanakhala choletsedwa kotero tikhalanso opanda ufulu konse. Mu njira iliyonse, mkwiyo wa anthu amene amafuna kuletsa khalidwelo ukhala ofanana ndi mkwiyo wa anthu omwe akudana ndi kuti ufulu wawo ochita khalidwelo uletsedwe. Sizitengera kuti mbali

Maziko a dziko la ufulu

iliyonse yakhumudwa motani koma palibe njira yovomerezeka yowaweruzira. Popeza dziko la ufulu sililola kuti milandu ithetsedwe ndi mphamvu, mbali iliyonse ingoyenera ilolere maganizo, khalidwe, ndi mchitidwe wa ena.

Izi zikusiyana ndi kusachitapo kanthu pa makhalidwe. Kholo lomwe silikuletsa khalidwe loipa la mwana wake silikuchita izi mwa kulolerana, koma likulekerera kuphunzitsa mwana khalidwe. Ngati aku-luakulu akuchita zinthu modabwitsa, tili ndi ufulu onse oyankhula ndi kuyesa kuwapempha kuchita mosiyana – ngakhale sikuti ndi mowakakamiza.

Kulolerana sichimodzimodzi ndi makhalidwe ovomerezeka– ganizo lakuti makhalidwe onse ndi ovomerezeka chifukwa anthu amatsutsana za makhalidwewa ndipo palibe njira yovomerezeka yosankhira pakati pa makhalidwewa. Tili ndi kuthekera konse kokhulupirira kuti khalidwe kapena chipembedzo chathu ndichabwino kuposa ena – koma osati kukakamiza maganizo athu pa wina aliyense.

Kulolerana, kusakanikirana ndi chisankho

Kulolera anthu ena kutha kukhala kovuta pamene chiwerengero cha anthu chikukhala chosakanikirana kwambiri. Kuphweka koyenda pakati pa mayiko, kuchotsa kwa ziletso zolowera m’dziko ndi kubwera pamodzi kwa ntchito zachuma ndi zifukwa zina zomwe zapan-gitsa anthu m’mayiko ambiri kukhala osakanikirana kusiyana ndi m’mene analili zaka zingapo zapitazo.

Anthu amati kuchulutsa zisankho kukhoza kupangitsa magulu osiyana potengera mitundu, chikhalidwe, dziko, chiyankhulo, ndi chipembedzo kukhala osiyana kwambiri, kusungira mkwiyo omwe ungalowetse pansu kulolerana. Mwachitsanzo, makolo atha kufuna ana awo akule limodzi ndi ana amtundu umodzi, ndipo ngati anga-sankhe sukulu zawo patha kukhala mwayi waukulu wa tsankho kusiyana ndi pomwe ana akanaphunzira sukulu zomwe zaikidwa ndi boma.

Chilungamo chake, sukulu zizingaphatikizane bwino ngati boma

lingasankhire malo asukulu, chifukwa ana ambiri amapita ku sukulu yomwe alinayo pafupi. Ndipo chifukwa chakuti anthu amtundu umodzi amakhala moyandikana, chiwerengero cha ana pa sukuluyo sichikhala chosakanikirana. Koma ngati makolo angasankhe sukulu, nawonso atha kusankha sukulu zotalikana nazo, kapena zomwe zili ndi ubwino wina omwe amawuona kufunikira kuposa mtundu, monga maphunziro, zamaimbidwe kapena kuthekera kwa chiyanikhulo.

Tsankho la mitundu ndilokhazikika, ndipo anthu amakonda kusankha anzawo komanso kugwira ntchito ndi anzawo ochokera ku gulu limodzi. Koma pali kusiyana pa izi ndi kusalolera anthu ena. Mikangano ikuluikulu pakati pa mitundu ili m'madera omwe gulu lina limakanizidwa ufulu ndi mwayi wina – mwanjira ina, pamene mfundo za dziko la ufulu zaphwanyidwa.

Chiopsezo chazikhulupiriro cha kulolerana

Chiopsezo chachikulu cha kulolerana ndi anthu ena ndi zikhulupiriro za chikhalidwe, mfundo zotsatira polamulira, ndi chipembedzo. Anthu ambiri omwe ali ndi mfundo zokhwima pa chipembedzo, atha kuona ukwati pakati pa amuna ndi akazi okhaokha kapena kugonana kwa anthu omwe sanalowe m'banja ngati chonyansa, chochititsa manyazi, chodabwitsa kapena zosemphana ndi chikhalidwe. Athanso kuganizira zinthu monga kulemekeza zinthu zopatulika, kusema zifaniziro za milungu, kukana malemba ena m'baibulo, kukana nsanamira ya chipembedzocho kapena kuona chipembedzo china kuti n'choipa kwambiri. Ichi atha kuchiona kuti n'chifukwa chokwanira kuti khalidwe limeneli lithetsedwe kapena kupatsidwa chilango.

Koma ngakhale zochita za munthu zinganyanse kapena kuipira ena, ndinso m'mene chingaonekere choipa potengera chipembedzo, palibe yemwe ali ndi ufulu odziletsa ngati sizikuvulaza kapena kuika moyo wa ena pa chiopsezo. Komanso, izi sizikuletsa mamembala a chipembedzocho kudzudzula machitidwe amenewa komanso kukamba zotsutsana ndi chipembedzocho, kapena kuwachotsa anthu ena mu chipembedzocho – pokhapokha ngati sakuopsezeka kapena kupwetekedwa. Komanso izi sizikulola aliyense, kuphatikizira boma,

Maziko a dziko la ufulu

kuletsa, kufufuza, kumanga, kuika mundende, kuzunza, kuthamangitsa kapena kunyonga aliyense kapena gulu lililonse chifukwa cha maganizo kapena zochitazi.

Malemba a maziko azipembedzo zapadziko lapansi amavomereza kulolerana ndi anthu ena, ngakhale nthawi zina adindo amawatambasula mosiyana kukwaniritsa zofuna zawo. Mayiko achitsamunda omwe anatenga ulamuliro m'malo ambiri anatenga ndi chipembedzo chomwe, kukhotetsa makhalidwe ndi malamulo awo kuti akutumikira kayendetsedwe kawo ka dziko. Maboma ena olamulidwa mwamphamvu ayesera kuponderezeratu chipembedzo, kuchiona ngati mdani ku mfundo zawo zoyendetsera dziko ndi ulamuliro wawo. Koma izi zilibe kanthu mu dziko la ufulu ngati zikhulupiriro zikukambidwazi ndi zachipembedzo kapena mfundo zotsatira polamulira. Sizikuperekabe mphamvu iliyonse kuwakakamiza ena omwe zochita, khalidwe kapena chipembedzo ndi mfundo zawo zili zosiyana.

Kulondola kwa ndale

Pali chiopsezo chakuchenjera cha kulolerana: kulondola pa ndale. Apa ndipomwe mpanipani pa ndale kapena m'dera umaikidwa pa anthu kuti avomere maganizo a anthu osankhidwa. Nthawi zambiri, anthu omwe amatsutsana ndi maganizo omwe alipo amaipitsiridwa mbiri kuti ndi oukira kapena oipa, ndi cholinga chopanganso maganizo awowo kukhala oukira komanso oipa. Izi zimapangitsa kuti maganizo awowa asagwiritsidwe ntchito mmalo mokuti awakambirane. Izi zimasonyeza kuti maganizo a anthu odziwikawa amakhala ofunikira kusiyana ndi m'mene alili.

Njira iyi imadalira kuumiriza kochenjera, m'mene omwe ali ndi maganizo osiyana amadetsedwa kuti zikhale zowavuta kuchita bwino m'dera. Mwachitsanzo, akatswiri pamaphunziro omwe amatsutsa umboni wa munthu kupangitsa kusintha kwa chilengedwe atha kukanizidwa mwayi wa ntchito kapena kukwezedwa udindo ku sukulu zaukachenjede. Mu dziko la ufulu, olemba ntchito sali omangidwa kulemba ntchito omwe sakugwirizana nawo; kapena anyumba zoulutsa mawu kuulutsa nkhani zosokoneza. Koma pamene

mabungwe azamaphunziro kapena nyumba zoulutsira mawu zikuyendetsedwa ndi boma kapena gawo lalikulu lili mmanja mwa boma, kusawerengera maganizo a anthu ochepawa kumakhala kuumiriza kwenikweni.

Kulolerana ndi kufuna choona

Kulolerana m'dziko la ufulu kumaposa kulolerana chipembedzo kapena mfundo zosiyana zotsatira polamulira. Mwachitsanzo, kumaphatikiza ufulu omasuka – m'mayankhulidwe, zolemba, kuulutsa mawu kapena kugwiritsa ntchito zida zina – zomwe m'malo mwake zimaonetsa kusapezeka kwa kauniuni.

Anthu ena atha kuliona dziko lopanda kauniuni ngati lodetsa nkhawa kwambiri. Ambiri atha kudabwa kwambiri ndi mawu, zithunzi, zoyankhula, ndi maganizo omwe angabweretsedwe poyera m'dziko la ufulu. Koma m'dziko la ufulu sitiletsa kuyankhula momasuka kapena kutchinga maganizo amunthu, ngakhale pafupifupi tonse mwaife tisagwirizane ndizomwe zanenedwazo, kuziona zolakwika kapena kukhulupirira kuti ndi zoipa.

Koma pali nthawi zina zomwe pali chiletso pa ufulu wa kuyankhula momasuka ngati zomwe zanenedwa zingapereke chiopsezo pa ena – monga kukuwa 'Moto!' ku fiyeta. Tikhoza kumulanga moyenera yemwe angapangitse anthu kuvulala kotero. Mofanananso, timateteza ana ku mawu kapena zithunzi zomwe tikuona kuti zingawawononge maganizo. Sitingalole kulengezetsa malonda amankhwala ozunguza bongo, kuti zikhale pa zikwangwani zoyandikira sukulu. Ndipo pali kufunika kwambiri kowapatsa anthu uthenga – monga kupatula kanema mosiyanasiyana – kuti anthu asadzidzimuke poona zinthu zomwe zingawakhumudwitse.

Izi ndi zosiyana kwambiri ndi kauniuni weniweni – kuletsa mawu ena, zinthunzi, mfundo ndi maganizo kuti zisaulutsidwe konse. Sipangakhale kuletsa uku m'dziko la ufulu weniweni chifukwa dziko la ufulu limakhazikika pa kumasukirana ndi chisankho. Anthu ayenera kudziwa mwayi womwe alinawo ngati angasankhe

Maziko a dziko la ufulu

mozindikira ndi kuyesera maganizo atsopano omwe angatukule tsogolo la wina aliyense. Kauniuni kumatsekereza mwayo wonsewo ndi zisankhozi ndipo mapeto ake kutimana chitukuko.

Komanso sitingakhulupirire ochita kauniuni. Choonadi ndi udindo ndi zinthu zosiyana. Olamula atha kukhala ndi zifukwa zawo – monga kudziteteza – poletsa maganizo ena kuulutsidwa. Komanso ngakhale ochita kauniuni atakhala ndi kufunira zabwino mtundu onse wa anthu, nawonso amalakwitsa. Alibe umwini onse pa nzeru, kapena kuzindikira kwapadera kwa chomwe chili choona ndi chomwe sichili choona. Ndikukambirana, mtsutso ndi kuchitachita kokha komwe kungaonetse izi. Ochita kauniuni atha kupondereza chilungamo molakwitsa chabe. Sangadziwiretu ngati akupondereza maganizo omwe angadzapezeke kukhala oona. Maganizo ena atha kukhala olakwika, koma kukhala ndi mlingo wa chilungamo, chomwe chingapangitse mfundooyo kukhala yofunikira. Choonadi cha maganizo ena chitha kudziwikiratu pakapita nthawi.

Njira yomwe tingaonetsetse kuti sitikupondereza choona komanso maganizo ofunika ndi polola maganizo onse kuti aulutsidwe, pokhulupirira kuti kuyenera kapena kuperewera kwawo kudziwika kudzera mukukambirana. Zomwe zikutanthauza kulola anthu kuyankhula mbali yawo, ngakhale pa nkhani zomwe ambiri akuziona kukhala zachilungamo. Choonadi chitha kulimbikitsidwa ndi mpikisano woterewu. Nchifukwa chake, kuchoka mu 1587 mpaka 1983, Mpingo wa Katolika unasankha woimilira ‘satana’ potsutsana ndi munthu amene wasankhidwa kukhala oyera. Ndikofunika kuonetsera zikhulupiriro zathu kuti anthu athe kufunsa. Ngati tikukhulupirira kuti ena analakwitsa pa maganizo awo, maganizowo ayenera kulandiridwa ndi kutsutsidwa, osati kungokhala osachitapo kanthu.

Kuchokera pa Socrates kupita mtsogolo, mbiri ili ndi zitsanzo za anthu omwe anazunzidwa chifukwa cha maganizo awo. Kuzunzidwa kotero kumachititsa anthu kukhala chete nthawi zambiri, ngakhale maganizo awo kumapeto amadzakhala olondola. Poopa mkwiyo wa Mpingo wa Katolika, Nicolaus Copernicus sanasindikize maganizo

Maziko a dziko la ufulu

ake okuti maiko amazungulira dzuwa kufikira atatsala pang'ono kumwalira m'chaka cha 1543. Otsatira wake Galileo Galilei anaimbidwa mlandu ndi bwalo la Mpingo ndipo anakhala masiku ake onse otsala mndende yapakhomo.

Kuopsezedwa kotere kumatsekereza choonadi, kukambirana ndi chitukuko. Kumapweteka dziko ngakhalenso opanduka omwe amazunzika.

Ngati tingangovomereza maganizo alionse popanda kukambirana kulikonse, maganizowa akhala pa maziko osatetezeka. Kuvomezedwa kwawo ndikosaganizira bwino. Zimangokhala nkhambakamwa chabe osati choonadi chenicheni. Ndipo pamene maganizo atsopano apambana, pakhoza kukhala chisokonezo.

Zitha kukhala zokhumudwitsa pamene anthu akamba zinthu zomwe sitikugwirizana nazo konse, kuyankhula maganizo omwe tikukhulupirira kuti ndiwolakwika, kuchita zinthu zomwe timazona zoda bwitsa, kapena kunyoza makhalidwe ndi zikhulupiriro za zipembedzo chathu. Koma kulolera kwathu pa izi kumaonetsa kukhulupirika kwathu ku ufulu, ndi chikhulupiriro chathu kuti tipite patsogolo kwambiri, ndi kupeza choona chatsopano mwachangu, polola maganizo osiyanasiyana kukambidwa osati kuponderezedwa.

Zoletsa

Titha kukhala okwiya ngati zambiri zomwe zimatisangalatsa m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku zitaletsedwa. Mwatsoka zambiri za izo zinaletsedwa kale²⁷.

Lamulo la kusapwetekana limati tilibe ufulu oletsa zochita za ena pokhapokha ngati zili ndi kuthekera kotipweteka kapena kupweteka ena. Koma zochita zambiri zimaletsedwa potengera kuti zipweteka omwe akuchitawo. Ichi ndi chifukwa chomwe amaletsera mankhwala ozunguza bongo, kusuta, mowa ndi zina zambiri. Vuto ndilakuti chifukwa chopulumutsira anthu kuti asadzipweteke kukhoza kupangitsa kuti chochita chilichonse chiletsedwe. Ndikosavuta

²⁷ For an excellent discussion of prohibitions, see John Meadowcroft (ed.), *Prohibitions*, Institute of Economic Affairs, London, 2008.

Maziko a dziko la ufulu

kunena kuti anthu amapwetekeka kapena kukhala pa chiopsezo pakumwa zotsekemera, kudya zamafuta kwambiri, kutenga mbali m'masewero oopsa, kupanga uhule kapena ukwati wa amuna ndi akazi okhaokha, kuyamba kutsatira chipembedzo china kapena kufunsa mafunso adindo. Potengera ndi anthu omwe amakamba izi, kungotaya mfundoyi sipangadutse nthawi yayitali kutinso ufulu uponderezedwe.

Zoletsa nthawi zambiri zimakhalanso ndi zotsatira zowononga. Polimbikitsa kufunika kwa zinthu zina kukhala zam'chibisira, kumakhala kovuta kuziyang'anira komanso kuzilamulira, ndipo zigawenga zikhoza kulowerera pomapereka katunduyu. Mwachitsanzo, Dziko la United States, limavutikabe ndi kupezeka kwa zigawenga zomwe mphamvu zawo zinakula mu zaka zana lapitalo, pamene kugulitsa mowa unali mlandu. Kupitiriza mchitidwe wosavomerezeka wa juga ndi uhule mbali zambiri za dziko la USA kwapititsanso patsogolo mchitidwe wa zigawengawu, omwe umakhala kalikiliki kupereka zinthuzi kuti akwaniritse kufunika kwake.

Kuletsa kumapangitsanso kukhala kovuta kuti anthu amvetsetse zotsatira za khalidwe lawo. Anthu amafunabe mankhwala ozunguza bongo, koma ngati mankhwalawa ndiwosaloledwa zimakhala zovuta kuti anthu apeze uthenga wokwanira okhudza kuopsa kwawo. Komanso ndikovuta kuti ogwiritsa ntchito aone ubwino wa chomwe akugula. Kumakhalanso kovuta kwa anthu omwe amadalira mankhwala ozunguza bongo kupeza thandizo la chipatala kapena mudera, popeza kutero ndikudzipereka ku zolakwa zomwe akuchita. Ndipo anthuwa amatha kukumana ndi zovuta zina, monga kutenga matenda a Edzi pogwiritsa ntchito masingano osaphitsidwa, chifukwa cha kusavomerezeka kwa mankhwala ozunguza bongo, kumapangitsa kukhala kovuta kuti atengeredwe malo otetezeka. Zotsatira zake nzakuti kuwononga kwambiri kwa mankhwala ozunguza bongo kumadza chifukwa chakuti ndiwosaloledwa²⁸.

Zoletsa ngati izi zimapereka mwina kwa anthu achilungamo omwe saona vuto kutenga mongosangalatsidwa chabe mankhwala ozunguza

²⁸ A point made strongly in Milton Friedman and Rose Friedman, *Capitalism and Freedom*, Chicago University Press, Chicago, IL, 1962.

bongo, kapena kupanga juga, kapena kumwa mowa kunyumba ndi anzawo, zomwe sizivulaza munthu aliyense. Ndipo polisokoneza lamulo ndi milandu ing'onoing'onoyi, amatha kupalamula yayikulu kwambiri komanso yowononga.

Kuletsa sikumatheka. Kuletsa kwa zakumwa zoledzeletsa ku United States kunadzetsa mchitidwe wokumwa m'chibisira komwe kunali kovuta kukuyang'anira. Malamulo okhwima pa mankhwala ozunguza bongo ndi zilango zikuluzikulu pogulitsa mankhwala ozunguza bongo padziko lapansi sikunaletse malondawa omwe amayerekezewa kukhala a ndalama zankhaninkhani.

Kuyesera kuletsa khalidwe lachizolowezi ndi kutaya nthawi chabe. Ndipo ndi chiopsezo ku ufulu chifukwa payenera kukhala mchitidwe wamphamvu woyang'anira komanso zipangizo zochitira zonsezi ngati tikufuna kukwaniritsa. Izi zimangopatutsa zipangizo zoonetsetsa kuti malamulo akutsatidwa mmalo mofufuza ndi kuzenga milandu yeniyeni. Zitha kuperekanso mwayi wa katangale pakati pa apolisi ndi akhothi; ngakhale ena sangapwetekeke ndi juga kapena kugwiritsa ntchito mankhwala ozunguza bongo, zilango zake zitha kukhala zazikulu, kupangitsa adindo kulandira ziphuphu zikuluzikulu kwa omwe akhudzidwawo.

Funso: Kodi sitikuyenera kuwateteza anthu kwa iwo eni?

Ayi. Mukufuna 'kutetezedwa' kwa inu eni? Kapena mukufuna kupanga ziganizo panokha m'mene mukuyenera kukhalira moyo wanu? Kulola boma kutipangira zisankho za chabwino kapena choipa ndi kosakwanira: tili pabwino ife eni kusiyana ndi adindo kuweruza zomwe tikupanga. Ndipo ndizoopsa: boma likhoza kuyamba kuletsa zinthu zomwe aliyense akugwirizana nazo kuti ndizolakwika, koma ngati mfundoyi ingavomerezedwe, boma litha kuletsa chilichonse.

Kodi tikuyenera kuletsedwa kufwentha mankhwala ozunguza bongo a kokeni, kusuta fodya, kumwa mowa, kudya zamafuta ambiri, kumwa zakumwa za shuga wambiri? Kodi tikuyenera kuletsedwa ndi malamulo kuchita masewero olimbitsa thupi, kusiya kuchita masewero oopsa, ndi kupita kutchalitchi? Kodi

Maziko a dziko la ufulu

tikuyenera kuletsewa kuwerenga mabuku oopsa kapena kudzudzula atsogoleri? Yankho mu dziko la ufulu ndi ayi. Ngati anthu akunyoza makhalidwe athu kapena kuchita chinthu choopsa, tiyenera kungowauza. Koma ngati sakupweteka wina aliyense, tilibe ufulu owaletsa.

Khalidwe lapagulu ndi lakumbali

Malamulo adziko la ufulu amawongolera khalidwe lapagulu – m'mene anthu akuyenera kukhalira ndi anzawo. Koma khalidwe la kumbali – lokhudza munthu yemwe akuchitayo – limakhala lakumbali komweko. Limakhudza malamulo ngati likupweteka ena.

Koma m'dziko la ufulu ndizofunika kuonetsetsa kuti kupwetekedwa kukunenedwako ndi kwenikweni. Kodi anthu ayenera kuloledwa kugulitsa ziphe? Popeza ziphe zimagwira ntchito zosiyanasiyana zomwe sizikhudzanso anthu, titha kuwononga zinthu kwambiri pole-tseratu kumugulitsa kusiyana ndi kumulola. Pakhoza kungokhala dongosolo lolemba mayina a omwe akugulitsa ndi kugula mankhwalawa, kuti wogwiritsa ntchito azidziwika; koma osati kuposera apo.²⁹

Kodi payenera kukhala lamulo loletsa kuledzera pagulu? Kapena kuletse kuyendetsa nyumba zokhala mahule komanso zochitira juga? Eya, koma ngati zikudzetsa ziwawa, ndi chifukwa chake mayiko ambiri amasankha kuwapatsa ziphaso. Koma gawo lalikulu la zochita izi limakhudza anthu okhawo omwe akuchita. Anthu ena atha kunyasidwa kungowaganizira chabe, koma ngati tingalole zochitazi kuletsewa chifukwa cha chilichonse osati kuvulazidwa kwa anthu ena, palibe chochita cha munthu chomwe chingatetezedwe kwa anthu oona za makhalidwe ovomerezeka.

Kodi anthu ayenera kuloledwa kupanga malonda masiku oyere-tsedwa? Kapena kukhala ndi mitala? Izi ndi zawo, osati zathu; sizipweteka munthu aliyense. Malamulo a dziko la ufulu alipo kuti ateteze ndi kupititsa patsogolo ufulu wa anthu, osati kukhazikitsa makhalidwe a anthu ena pa ena.

²⁹ This and the following points are made well in John Stuart Mill, *On Liberty*, 1859, in John Stuart Mill, *On Liberty and other Essays*, Oxford University Press, Oxford, 2008.

Maziko a dziko la ufulu

Ngakhale zili choncho, mu dziko la ufulu anthu ndiwololedwa kukhazikitsa malamulo awo pa katundu wawo, pokhapokha ngati lamulo losapwetekana silinaswedwe. M'mayiko ambiri, malo opita anthu ambiri (monga masitolo akuluakulu ogulitsira zinthu) amayang'aniridwa ndi anthu wamba osati atsogoleri andale. Nchifukwa chake mchaka cha 2005 malo ogulitsira zinthu ku Bluewater kumwera chakum'mawa kwa England analetsa kulumbira, kusuta, kutaya mapepala, ndi kuvala zovala zobisa nkhope (monga majuzi achipewa). Ku Bournville, pakati pa dziko la England, - mzinda wa mafakitale opangidwa ndi George Cadbury opanga chokoleti ndi oyendetsedwa ndi bungwe lomwe silaboma unatsatira mfundo yake – kugulitsa mowa poyera ndikoletsedwa. Pakuti ku Bluewater ndi Bournville zili mmanja mwa anthu wamba, amatsatira ufulu wawo.

Vuto la khalidwe la kusadzikonda

Anthu ambiri amasokenekera ndi ganizo lakuti mayiko a ufulu komanso ufulu pa chuma amayendetsedwa potengera kudzikonda kwa omwe akutenga nawo mbali. Atha kufunitsitsa dziko loyendetsedwa ndi anthu osadzikonda – okhudzika ndi zofuna komanso ubwino wa ena. Koma izi zimabweretsanso mavuto ambiri kuposa mavuto omwe akuthetsa³⁰.

Palibe mlozo wothandizira ena

Poyambirira, tingadziwe bwanji chomwe chofuna cha anthu ena? Tilibe kuthekera kofikira zomwe akuganiza kapena zofuna. Ngati tingayesere kuchita zomwe akufuna, titha kulakwitsa kwambiri. Aliyense amene walandirapo mphatso yosiyansiratu ndi zomwe zinali kumtima kwawo pa tsiku lomwe anabadwa akudziwa za m'mene banja ndi anzawo angaweruzire molakwika zomwe munthu amakonda. Khalidwe lopereka likuoneka losakwanira kukhala tsinde loyendetsera dziko lonse.

Ndizovutanso kufufuza zinthu zomwe anthu ena akutipatsa. Timalandira mphatso ndi kuthokoza, ngakhale tikudana nazo. Izi

³⁰ For a fuller explanation of this, see Mawo Yushi, 'The paradox of morality', in Tom G. Palmer, *The Morality of Capitalism*, Students for Liberty and Atlas Foundation, Arlington, VA, 2011.

Maziko a dziko la ufulu

zikutanthauza kuti anthu m’dziko losadzikonda sangaphunzire cheni-cheni chimene ena akufuna. Izi nzosiyana kwambiri ndi dziko lachuma chokhazikitsidwa pa kudzikonda, komwe ngati makasitomala sangapeze zenizeni zomwe akufuna kwa ogulitsa, amatero, ndikuo- pseza kutengera mabizinezi awo kwina. Kudzikonda kumaika chidwi pa ogulitsa kuti apereke zenizeni zomwe makasitomala akufuna pantengo otsika.

Kusadzikonda kumadzetsa mikangano

Ngati kuyesera kuthandiza anthu mwadala chinali cholinga cha kuchita malonda, pakanakhala mikangano pakati pa ogula ndi ogulitsa ngati m’mene zilili lero m’dziko lodzikondali. Ogula akanafuna mitengo yokwera kuti apindulitse ogulitsa. Ogulitsa akanapereka mitengo yotsika kuti apindulire ogula. Ili ndingati kalilole chabe wa zomwe zikuchitika m’masiku alero.

Pa nkhani za malonda, anthu odzikonda amakhala pa mkangano wina ndi nzake, koma atha kuthetsa mavuto awo ponenererana. Ngati cholinga chokhacho chili kupindulira ena, pakanakhala popanda njira yothetsera mikanganoyi. Aliyense wosadzikonda akanatha kufun- tsitsa kuti wina apindule. Poti palibe aliyense ofuna kupindula pa chochitikachi, kufunikira mwachangu kwa zofuna zawo sikungawa- thandize kuti agwirizane.

Kudzikonda ndi phindu

Kudzikonda kumaika chidwi pa ogulitsa – ndi ogulanso –poonetsetsa kuti phindu lomwe alipeze likuposa mtengo ogulira. Opereka zinthu wosadzikonda yemwe anagwira ntchito osalandirapo kanthu atha kupereka chithunzithunzi cholakwika kwa aliyense– chithunzithunzi chakuti nthawi ndi luso lawo lilibe mtengo uliwonse. Makasitomala omwe angatenge chithunzithunzichi mwapamwamba, atha kuvutitsa wopereka katunduyo ndi zofuna zawo. Operekawa atha kukhala opanda njira yokanira kuwathandiza anthuwa, ngakhale phindu lake lingakhale lofanana kapena lotsika mosiyanyitsa ndi ndalama zomwe alowetsa.

Osoka nsapato, mwachitsanzo, atha kukhala ndi chimzere cha anthu oti awakonzere katundu wawo. Mu msika wachuma wa anthu odzikonda, amalonda otere atha kuwauziratu makasitomala mosapsatira kuti katundu wawo siofunika kukonzedwa; apo ayi atha kunena mtengo okwera kwambiri kuti kasitomala angofika posiya yekha. Msika umapanga zomwe zikufunidwa, ndi kuika chidwi pa chomwe chili chofunikira.

M'dziko losadzikonda, anthu atha kuthamangira kukawathandiza oyandikana nawo ntchito zosiyanasiyana – monga kumanga nyumba. Koma pachilungamo pake komanso kutengera zomwe zingalowe, kutha kukhala kwabwino kuti oyandikana nawowo apite pamsika, ndikukalemba ntchito m'misiri weniweni, kusiyana ndi kudalira anzawo omwe ndiwosatha ntchitoyo. Kuluza kotere kumabwezerezedwa ngati oyandikana nawoyo angagwiritse bwino ntchito luso lawolopa ntchito zina. Msika umalimbikitsa anthu kuika nthawi ndi mphamvu zawo komwe zikufunika kwambiri.

Funso: Kodi sitingalamulire mitengo ya zinthu kuti anthu osauka akwanitse kugula zinthu?

Ayi. Mitengo imazindikiritsa kusowa kwa zinthu. Imatiuza komwe ziliko zambiri ndi komwe ziliko zochepa. Imawauza opanga katundu kuti ndi katundu wina akufunika wambiri, ndinso ogula kuti akuyenera kuti achepetse ndi kuyang'ana wina wolowa m'malo. Kulumulira mitengo ya zinthu kumapondereza zizindikirozi kotero kufunika kwa zinthu kumaposa kupezeka kwake mapeto ake pamakhala kusowa. Izi zimapangitsa kugawa pang'onopang'ono katundu wosowayo, zomwensu sizikwanira.

Chitsanzo ulamuliro pa nyumba zobwereketsa, unapangidwa kuti anthu athe kufikira nyumbazi. Koma zomwe amapanga ndi kuwononga nyumbazi kapena kuwonjezera vuto la kusapezeka kwa nyumbazi, pamene eni nyumbazi aganiza zolandira ndalama zomwe amapeza zimakhala zosagwirizana, choncho amachotsa katundu wawo pa msika wobwereketsa nyumba. Ngati anthu sangakwanitse kupeza zina zofunikira, njira yabwino sikulowerera

Maziko a dziko la ufulu

pamsika koma kuwapatsa ndalama – kudzera mu mabungwe oima paokha ochita zachifundo kapena ngongole kudzera mu ndondomeko yoperekedwa kuchokera ku misonkho. Atha kugula zinthuzi mofanana ndi mopikisana pa msika ngati wina aliyense.

Makhalidwe a pamsika

Potengera kuti dziko la ufulu pa misika limakhazikika pa kudzikonda sikukupangitsa msikawu kukhala opanda khalidwe. M’misika, anthu atha kutukuka pogwirizana ndi anzawo powapatsa zomwe akufuna. Khalidwe lotsutsana ndi kukhala limodzi ndi anthu ena limapatsidwa chilango: nchifukwa chiyani munthu angapange malonda ndi munthu wamwano pamene pali anthu ena ambirimbiri omwe atha kumvana nawo, omwe ali olola kuchita malonda?

Palinso malamulo oonetsetsa kuti misika ikuyenda bwino popanda kuumirizana. Koma malamulo okhazikitsidwawa sangathane ndi mlandu uliwonse. Misika siilephera kuyendera chikhulupiriro, ndipo imapereka phindu kwa omwe ali ndi mbiri yabwino pokhala okhulupirika ndi odalirika. Ngakhale choyendetsa misikayi chili kudzikonda, misika imapititsa patsogolo khalidwe lopindulira aliyense mogwirizana.

Udindo wa kampani mu dera

Anthu ambiri amafuna amalonda azichita zabwino ndi kupititsa patsogolo udindo wa kampani mu dera. Makampani akuluakulu m’mayiko osiyanasiyana pano amasindikiza nkhani zokhudza zomwe akuchita kuti akhale nzika zabwino.

Koma ndi anthu okha omwe angakhale okhulupirika kapena osakhulupirika, akhalidwe labwino kapena loipa. Magulu alibe khalidwe lawolawo. Dziko, mzinda, mtundu kapena gulu la anthu ndi kampani silingakhale ndi khalidwe kapena lopanda khalidwe – ndi anthu ake basi. Mosapsatira, titha kufuna atsogoleri abizinezi kukhazikitsa chikhalidwe chabwino mumakampani awo. Koma makhalidwe ndi udindo zimaonekera mu zochitika – ndipo ndi anthu amene amachita osati gulu.

Maziko a dziko la ufulu

Gulu loona za udindo wa makampani m’dera ndi njira yoyesera kupereka udindo woyang’anira anthu komanso mapologalamu othandiza umoyo anthu ku bizinesi. Mabizinezi amayesera kuonetsera kukhulupirika kwawo pothandiza sukulu zomwe zili m’deramo, magulu am’dera ndi zina. Litha kukhala ganizo labwino pa bizinezi kupanga izi: chifukwa mapeto ake kampaniyi idzafuna kulemba ntchito ophunzira m’sukuluzi kotero kukonza ubale wabwino ndi iwo utha kuthandiza kuti ntchitoyo idzakhale yosavuta. Koma ili liyenera kukhala ganizo lopangidwa ndi eni komanso akuluakulu abizineziwa, osati kuwakakamiza kuti aonetse makhalidwe abwino.

Ngati mabizinezi akanakhala ndi mpikisano weniweni, sipakana-pezeka ndalama iliyonse yotsala yothandizira ntchito zam’dera zomwe sizinathandize kutukula chuma cha bizineziyo. Ngati makampani ali ndi ndalama zothandizira ntchitozi, ndi chisonyezo chakuti msika sukuyenda bwino (mwachitsanzo, malamulo aboma akuteteza makampaniwa ku mpikisano). Pa msika woonadi wampikisano, makampani otere atha kugwetsedwa ndi makampani omwe anathandiza ntchito zam’dera, ndi kuchepetsa phindu lomwe likanapezeka.

Ochita bizinesi sakwanitsanso kuonetsetsa kuti ndalama zomwe amathandizira kudera zikugwira bwino ntchito yake. Amatha kulangizidwa bwino kuti aike chidwi pa ntchito yawo yopanga phindu popereka katundu ndi zinthu zomwe anthu akufunitsitsa – zomwe mapeto ake zingatukule chuma ndi kupanga ntchito mwachifundo kukhala yosavuta.

Maziko a dziko la ufulu

8 KUPEREKA UMWINI KWA ANTHU OIMA PAOKHA NDI KULUMIKIZANA KWA MAYIKO ONSE

Kusamuka kwa anthu ndi luso lamakono

Dziko lotseguka

Madera omwe anali akutali kwambiri dziko lapansi, sali akutalinso pano. Wailesi za kanema, wailesi, intaneti ndi njira zina zolumikizirana zimabweretsa pamodzi zikhalidwe zina, makhalidwe, mitundu, anthu, maiko ndi njira zoyendetsera boma pafupi nafe. Maulendo a mlengalenga ndi maulendo a pansi achangu amapangitsa kuthekera kwa munthu kukafika malo ambiri.

Izi zapangitsa kukhala kovuta kuti boma libise zofooka zake. Pali-benso malo aliwonse m’nyumba zaaboma omwe ali ngati chipupa choyembekezera kutchingira nzika kusadziwa zofooka zake. Tithokoze kulumikizana komwe kulipo padziko lonse kudzera m’masamba amchezo pa intaneti kapena wailesi za kanema zakunja zopezeka pa satalayiti, nzika za m’dziko zikudziwiratu kale za kupezeka kwa mwayi wabwino kwambiri m’mayiko ena.

Mapeto ake, mayiko ambiri asiya kuyesera kwawo kukhala ozitsekera ku dziko lonse lapansi. Anayambano kutseguka kwa alendo ochokera m’mayiko ena odzaona malo ndi alendo ena. Mu zaka makumi ochepa apitawo, mayiko akuluakulu monga Russia, Vietnam, Burma (Myanmar) ndi ena ambiri akhala otsekuka kwambiri ku mayiko ena onse pa dziko lapansi. Lero, anthu asanu mwa anthu zana alionse ku Afghanistan akhalako kunjwa kwa dzikolo kwa kanthawi m’moyo wawo.

Kusinthana maganizo

Si anthu okha omwe amayendayenda padziko lapansili – maganizonso amayenda nawo limodzi. Alendo odzaona malo amabwera ndi nkhani za mayiko osiyanasiyana, momwe anthu a ufulu amachitira zinthu, kuganiza ndi kuyankhula. Anthu m’mayikowa amapitanso m’mayiko enawa ndipo amakapeza kuti zomwe zimanenedwazi ndi

Maziko a dziko la ufulu

zoon. Ngati anthu ali ndi mwayi wa intaneti kapena wailesi ya kanema ya satalayiti, nkhani zomwe amamva zimatsimikizidwa ndi zomwe akuona pa kanema.

Malonda alinso ndi zotsatira zomwezi. Pamene dziko latseguka ku malonda ndi mayiko ena, nzika zake zimapezeka zikuchita malonda, ndi kupanga ubale ndi anthu azikhalidwe zina, komanso kumvetsetsa njira zina zokhalira.

Izi zimakakamiza boma kutseguka kwambiri. Anthu omwe amaona ndi kudziwa za ufulu weniweni amamvetsetsa mphamvu yake yaikulu yopititsa patsogolo chitukuko ndi kufalitsa kuchita bwinoku. Amafunanso kuti chitukuko ndi kuchita bwino zikhale zawo. Luso lamakono, malonda, kuyendayenda, kuona malo osangalatsa, ndi misika ya mayiko onse zonsezi ndi nsanamira zadziko la ufulu.

Kupititsa patsogolo dziko la ufulu

Osati kuchotsa mphamvu zoyendetsera chuma kwa atsogoleri kupita kwa anthu wamba

Kupanga dziko la ufulu komwe kunalibe sintchito yophweka. Maboma atsopano ndi mabungwe am'mayiko osiyanasiyana amafuna kusintha kwakukulu monga kusintha dongosolo lonse lamaudindo, kapena kuchotsa m'manja mwa boma ntchito zamakampani akuluakulu.

Nthawi zambiri, njira iyi imadzetsa chisokonezo. Ndi khalidwe logwiritsa ntchito ulamuliro kupindulira munthu mwini lilipobe, komanso kusamvetsetsa kwa anthu za misika ndi mpikisano, njira zambiri zopereka mphamvu zoyendetsera bizinezi kwa anthu oima paokha (monga m'mene anachitira ku Mexico mzaka zam'ma 1980) zimangochotsa mphamvuzi m'manja mwa boma ndi kupereka kwa anzawo a anthu andale. Kwa anthu, mphamvu zoperekedwa kwa anzawo sizisiyana ndi m'mene mphamvu zinali ku boma m'mbuyo. Komanso poti kusintha dongosolo la zachilungamo kutha kutenga zaka zambiri, kukondera kotereku kutha kudutsa osatsutsidwa ndi akhothi. Koteru anthu amangozowera mavuto obwera ndi makampani omwe achoka m'manja mwa bomawa ngati m'mene anali

Maziko a dziko la ufulu

m’manja mwa boma. Ena amafika pongokhulupirira kuti ndi anthu otsutsiratu ndi ofuna kusintha zinthu omwe angabweretse njira yatsopano yomwe ingapindulire anthu onse kusiyana ndi kagulu kochepe ka anthu odziwika.

Zolimbikitsa ufulu kuchokera pansi

Njira yosintha ntchito zachuma kuchoka kwa atsogoleri kupita ku anthu zalephera chifukwa zayesera kusintha kaonekedwe ka mabungwe aboma osasintha makhalidwe enieni, zochita, ndi zolimbikitsa zomwe zinawapanga ndi kuwathandizira.

Luso lopanga zinthu ndi kutukuka kwa dziko la ufulu limakula kuchoka mu ndondomeko za malamulo ndi makhalidwe zomwe zimaonetsera m’mene anthu akuyenera kukhalira ndi kugwirizana momasuka. Ngati tingabweretse ndondomeko za malamulo ochitira zinthu, ndi kuwamasula anthu kuyendetsa miyoyo yawo mogwirizana ndi malamulowa, ndekuti mphamvu zachibadwa ndi khumbo la anthu onse liyendetsa kusinthaku bwino lomwe.

Kungoyerekeza, mwachitsanso, kuti tipange kophweka anthu kuyamba bizinezi zatsopano, kukhala ndi umwini ndi kuyendetsa bizinezi molimba mtima, kukhala ndi umwini wakatundu wotetezeka, kupanga mpamba ogwira ntchito ndi kupanga malonda momasuka. Pochita izi, tipanga malamulo ndi chilimbikitso chomwe chibweretse kutukuka pachuma komanso kupititsa patsogolo kusintha kwa dera. Anthu ayamba mabizinezi ang’onoang’ono, kuphunzira kachitidwe ka bizinezi, ndi kutukuka – kupambana osangoti pachuma kokha komanso kudzikhulupirira kwambiri. Dziko lodzikhulupirira kwambiri litha kukhala ndi kuthekera koposa pothana ndi mavuto akuluakulu okhudza mabungwe monga kusintha dongosolo la maudio ndi makampani aboma.

Kotero sitiyenera kuyambira pamwamba kuti tisinthe nthambi zonse za boma. Tiyenera kuyambira pansi kuti tisanthule zilimbikitso zomwe zingayendetse kusinthaku kudzera mu nthambi zonsezo³¹.

³¹ I am grateful to Peter Young and Stephen J. Mastey of Adam Smith International for their expert insights on this.

Kugwira ntchito kwa ufulu wa katundu

Ufulu wa katundu ku Peru

Chitsanzo chosangalatsa ndiko kusintha kwa ufulu wokhala ndi katundu ku Peru, komwe kunatsogozedwa ndi katswiri pankhani zachuma wotchedwa Hernando de Soto kumayambiriro kwa zaka zam' ma 1990. De Soto anadandaula kuti chifukwa cha kuchuluka kwa adindo komanso katangale, zinkatha kutenga pafupifupi chaka kuti munthu alembetse bizinezi yatsopano. Kunali kovutanso kwambiri kukhala ndi katundu. Mapeto ake anali akuti azamalonda aang'onoang'ono samakhala ndi munda, bizinezi kapena nyumba yawo. Izi zinapangitsa kukhala kovuta kuti apeze ngongole zotukula malonda awo. Sakanatha kugulitsa malo kapena bizinezi yawo. Ndipo sakanagwiritsa ntchito makhothi pamilandu yawo ya katundu kapena bizinezi.

Zotsatira zake zinali mbali ziwiri zakayendetsedwe kachuma ku Peru, imodzi yogwirizana ndi malamulo ndi yosangalala ndi phindu lonse pachuma ndinso kutetezedwa ndi lamulo, ndi mbali ina ya mamiliyoni azamalonda aumphawi wadzaoneni chifukwa nyumba ndi bizinezi zawo zinali zosavomerezeka pa malamulo. Boma linataya misonkho chifukwa linkalephera kuunikira kapena kutolera misonkho pa mabizinezi ena ang'onoang'ono owonjezerekawo. Ndipo popanda chitetezo chilichonse pa lamulo, azamalondawa amaponderezedwa mosavuta ndi mbava komanso gulu la chicommunist lotchedwa *Shining Path guerrilla*.

Yakho limene De Soto ndi ena anakhazikitsa lidali kuchotsa malamulo a maudindo ambiri omwe atsatidwa polembetsa bizinezi yatsopano, komanso kuchotsetsa ziphaso ndi zilolezo zambiri zomwe zimayenera kutengedwa kuti uyendetse bizineziyi. Panalinsu kusintha pa malamulo amalolo zomwe zinapangitsa mabanja oposa miliyoni imodzi ku Peru kukhala ndi umwini wa malo koyamba. Mapeto ake, kuthekera kwa bizinezi zing'onozing'ono kunakula, chifukwa eniake ankatha kupeza ngongole kuti akulitse bizinezi zawo ndi kugula komanso kugulitsa katundu. Pamene anthu anali ndi kuthekera kopeza

Maziko a dziko la ufulu

mpamba ndi kusunga ndalama, nyumba zawo zinasintha kukhala zapamwamba ndipo makolo anayamba kulipira ndalama zambiri pa maphunziro a ana awo.

Kusinthaku sikuti kunalibe otsutsa. Anthu ena amanena kuti kupereka umwini wamalo kwa munthu sikwabwino chifukwa nkovuta kutsimikiza mwini wake chinthucho poyambirira. Ena amati kupereka maloku kunapindulira achuma koposa osauka omwe anali ndi malo ochepa; kupereka maloku kunatenga malo amakolo awo omwe alimi osauka amadalira; kapena kuti kuperekaku kunaphwanya malire a mgwirizano omwe – ngakhale unali osavomerezeka –umagwira ntchito bwino. Ena anati kusintha kwa malamulo a maloku sikunali yankho lenileni ndipo zolepheretsa zazikulu za chitukuko pachuma ndi zofooka zomwe chikhalidwe cha anthu chinaika pa zofuna zawo.

Sikophweka kukhazikitsa msika ogwira bwino ntchito komwe kunalibe. Ndikosavuta kupanga nsuzi wa nsomba kuchokera mosungira nsomba, koma ndikovuta kupanga mosungira nsomba kuchokera mu nsuzi wa nsomba. Ngakhale zili choncho, mayiko ena ayesera kutengera kusintha kwa ku Peru, ndipo De Soto mwiniwake walangiza mayiko ambiri, ku Latin America komanso ku Africa.

Zosintha zina zothandizira

Koma pamene ufulu wa katundu wogwira bwino ntchito pa chuma uli wofunikira, zina zothandizira kusinthaku ndizofunikanso. Mwachitsanzo, pakufunika kukhala misika yangongole yogwira bwino ntchito, yomwe malamulo ovuta ndi maudindo akhoza kulephera kusokoneza. (chitsanzo chabwino cha ngongolezi ndi Banki ya Grameen ku Bangladesh, yomwe imapereka ngongole zing’onozing’ono ku mabizinezi akumudzi – kuphatikizapo ngongole zomwe amayi amalonda omwe alibe malo atha kuyambitsa bizinesi yomalipiritsa mafoni pogwiritsa ntchito foni zosayendera nthambo.)

Pakuyenera kukhala ndi ndondomeko ya malamulo yokhulupirika ndi yogwira bwino ntchito, kuti anthu atha kuthetsa milandu mofulumira ndi modalirika. Sitikuyenera kudikira aphungu opanga malamulo kuti aganizire ndi kuvomereza zosintha zina ku ndondomeko

ya malamulo oyendetsera dziko. Malamulo akudera, ochokera mu milandu ya anthu, ndiachangu kwambiri, ndipo patha kukhala dongosolo la malamulo akudera omwe aikidwa kale m'malo ndi bungwe lokhazikika lomwe lili ndi zotsatira zokhazikika za milandu yam'mbuyo lomwe likugwirizana ndi mmene anthu akumudzi amadziwira chilungamo. Koma sitikuyenera kuika malamulo ofotokoza mmene mabizinezi angayendere, monga ndondomeko ya eni bizinezi, udindo wa munthu pangongole, ufulu eni bizinesi, komanso ndondomeko zoyenera kutsatidwa pomwe ndalama zatha.

Tiyeneranso kuchepetsa malamulo omwe amaletsa kubwera kwa ena m'misika kuti maganizo atsopano abwere. Mwachitsanzo, olamulira ku Nepal, dziko lomwe linkangopanga lokha zamalonda zisanafike zaka zam'ma 1950, linakaniratu ganizo logulitsa kampani yoyendetsa zamafoni chifukwa chakuti anthu adzachita mantha ndi ganizo loti iziyendetsedwa ndi kampani yomwe siyaboma. Koma anavomereza kupereka ziphaso zakuti makampani atsopano atha kubwera. Makampani obwerawa akhala akuchita bwino mokuti dziko la Nepal lili ndidongosolo la mafoni lotsogola kwambiri.

Pamene zitsanzo zambiri zikuchulukira za mabizinezi ang'onoang'ono ndi amalonda atsopano olowa pamsika, kuchulukitsa mwayi wa ntchito ndi kuwonjezera chitukuko, kupititsa patsogolo ntchito zothandizira makasitomala, ndi anthu ambirinso omwe angamvetsetse kuthekera kwakukulu kwa ufulu kopanga chuma ndi ndalama. Anthu ambiri akathandizira ganizoli, ndi anthu ochepa womwe angafune njira zosintha koma zokakamiza kwenikweni.

Kusintha pa zaulimi

Chitsanzo cha mphamvu ya kugwira ntchito kwa ufulu okhala ndi katundu ndi kusintha pa zamalimidwe ku Soviet Russia, China ndi Vietnam. Maboma awo a chicommunist anakhazikitsa ntchito zawulimi pa umwini wamalo wagulu ndi minda ya malonda. Iwowa analamulira ufulu ogwira ndi kugwiritsa ntchito malo ndi kukhazikitsa ndondomeko yosakondera yogawira zinthu. Koma zinthu sizinayende. Maguluwo anali aakulu, ovuta kuyendetsa komanso a maudindo

Maziko a dziko la ufulu

ambiri. Ndipo chifukwa choti munthu amayenera kugawana phindu la zomwe wakolola ndi ena, anali ndi chilimbikitso chochepa kuti alimbikire kapena kuti apeze zambiri.

Ngakhale sankafuna kusiya mfundo yaumwini wapaguluyi, dziko la China linaphwanya ndondomeko yaku Sovietiyi mu zaka zam'ma 1970. Udindo wa pabanja unabwera m'malo mwake, omwe unapangitsa mabanja kugwira ntchito mu minda yawoyawo. Izi zinabweze-reta kulumikizana pakati pa mphamvu ndi phindu. Ntchito za ulimi ku China zinapita patsogolo kwambiri. Zokolola zakumunda mu zaka zam'ma 1980 zinachuluka kwambiri, ndi kukula kwa zisanu pa zana lililonse pa chimanga, zisanu ndi zitatu pa zana lililonse pa thonje ndi khumi ndi zinayi pa zana lililonse pa mbewu zopangira mafuta³².

Koma chitukuko chofulumirachi sichinakhalitse. Njirayi inali ndi zofooka zake. Poyesera kufananitsa kusiyana ubwino wa malo, adindo anawapatsa mabanja minda ing'onoing'ono yambirimbi kusiyana ndi kungopereka umodzi waukulu. Ndipo mphamvu zabanja limodzi kumwazidwa pa minda isanu kapena isanu ndi umodzi, kunali kosatheka kubweretsa njira zatsopano. Ngakhale njira zoika malire amindayi zinkatenga malo aakulu oyenera kulima. Ndipo ndondomeko yogawayi siinayang'anire kusiyana kwa zokolola za mabanjawa.

Kotero anaganiza zosasintha umwini wa minda, koma kubweretsa njira ya ufulu pakagwiritsidwe ntchito ka malo – kuwapatsa mabanja ufulu wa nthawi yayitali kuti agwire ntchito pa malo, kupeza zokolola ndi ndalama kuchokera ku malowo, ndi kudzawasiyira ena ufuluwo.

Komanso, njira iyi siyinali yosalakwika potengera ndi maganizo a mfundo za msika wa ufulu kapena ufulu pa katundu. Kugula kwa boma komanso ndondomeko yokhazikitsa mitengo kunachotsa kuthekera kwa mlimi kupanga ziganizo paiwo okha ndi kusangalala ndi phindu la thukuta lake. Popanda msika weniweni m'dzikolo, kubweretsa pamodzi kwa minda ing'onoing'ono kunali kovuta.

³² For details, see Wolfgang Kasper, 'The Sichuan experiment', *Australian Journal of Chinese Affairs*, 7, February 1981, pp. 163–72.

Koma pang'onopang'ono msika wa kagwiritsidwe ntchito ka malo unatsegulidwa.

Mu chigawo cha Meitan kumpoto kwa Guizhou, mwachitsanzo, anthu am'mudzi ndi adindo anakhazikitsa mlingo wa nthawi yomwe munthu angagwiritsire ntchito malo kukhala zaka makumi awiri, kuwathandiza mabanja kupanga ndondomeko zamtsogolo. Alimi anapatsidwa mphamvu zopereka mwakufuna kwawo kapena kusinthana nthawi yawo kapena kuphatikiza minda yawo. Ndipo panali zilimbikitso zokaswa mphanje malo osalimidwa. Mapeto ake, malo ambiri anakhala akulimidwa, ubwino wa nthaka unapita patsogolo chifukwa mabanja amalisamalira bwino ndiponso zida zatsopano zinabweretsedwa. Mu chaka cha 1995, boma lidalimbikitsa midzi ina kutsatira chitsanzo chaku Meitan, ndipo chinachake chofanana ndi ufulu pa katundu okhudza malo chinayamba kufala.

Ufulu wa madzi

Madzi ndi chinthu china chosowa chomwe ufulu pa katundu ungagawe bwino kusiyana ndi boma. Kunzambwe kwa dziko la United States komwe kumasowa madzi, chiopsezo cha ng'amba chinali chosasowa nthawi inayake – osati chifukwa cha kusowa kwa madzi koma chifukwa cha ndondomeko yowagawira. Omwe amatunga madzi moyambirira mu mtsinje, mwachitsanzo, anali ndi mwayi kusiyana ndi obwera mochedwa; koma kuti akhale nawobe ufuluwu, amayenera kumatungabe – ngakhale pamene madziwo sakufunikira kwenikweni.

Mu zaka zam'ma 1990, madera monga ku Montana ndi Arizona anayamba kuwalola anthu kupanga malonda ndi ufulu wawo wa madzi. Ngakhale padakali malamulo ambiri omwe amatchingira msikawu, zathandiza kuonetsetsa kuti madzi akupita kwa owagwiritsa ntchito enieni. Chifukwa chakuti ufulu wa madzi utha kugulidwa kapena kugulitsidwa, omwe amagwiritsa ntchito madzi pang'ono (omwe angagwiritse ntchito madzi ochepa kapena kubwereza kuwagwiritsa ntchito) pano atha kupereka ufulu wawo otunga madzi abwino kwa omwe akuwafunitsitsa. Uwu ndiwo ubwino wa

Maziko a dziko la ufulu

ndondomekoyi chifukwa ufulu wa madzi wafikira kunzambwe kwa dziko lonse la United States.

Njira zoperekeru umwini wa bizinezi kwa anthu wamba

Mafakitale oyendetsedwa ndi boma amakhala ndi mphamvu zonse, zimene sizipereka mpata kwa makasitomala. Kotero atha (ndipo amatero) kupereka mitengo yokwera kwambiri pa katundu yemwe siwabwino. Ngakhale angatalikirane ndi olamulira, kuyendetsedwa ndi bungwe lina, amakhalabe akulamulidwa ndi kagulu kochepa ka anthu odziwika bwino kapena anzawo.

Mwachitsanzo, Gulu la ‘bonyads’ ku Iran, ndi magulu omwe amatengedwa kuti ndiwohandiza mwachifundo ndipo ali ndi mphamvu pa mlingo wa magawo asanu pa magawo nzana alionse a chuma cha ku Iran, pa kutukula katundu, zaulimi, makampani opanga zinthu ndi zokhudza maulendo a pamadzi. Linakhazikitsidwa poyambirira ndi Shah, ndipo anadzudzulidwa kuti simagulu enieni achifundo koma njira za boma zopezera phindu. Koma, kutatha kusintha kwa ulamuliro m’chaka cha 1979, boma lomwe linabweralo linawaona maguluwa kukhala abwino kwambiri kuti asawasiye. Kotero anakhalabe, anakonderedwa mwapadera pa nkhani ya misonkho, ndi kuthandizidwa magawo ena ndi boma pa zochita zawo: ndipo katundu yense yemwe amalandidwa kwa anthu amaphatikizidwa kwayiwo. Iwowa alipo kuti athandize osauka, koma omwe ankapindula kwambiri anali am’maudindo.

Kupereka mphamvu kwa anthu wamba zoyendetsa mabizinezi aboma kuyenera kubweretsa zotsatira zosintha za umwini wa anthu ndi mpikisano ndi mabizinezi omwe mphamvu zonse zili ndi adindo, ndi kuchotsa katangale nkubweretsa malonda ochitidwa mosabisa. Zikhozanso kuthandiza kubwezeretsa mpamba wa mafakitale kwa anthu. Koma kuti zonsezi zikwaniritsidwe zitengera masomphenya, kulimba mtima ndi kupanga mfundo mosamala.

Palibe njira imodzi. Kupereka mphamvu kwa anthu wamba zoyendetsa mabizinezi aboma ndi nkhani yandale komanso ya zachuma.

Maziko a dziko la ufulu

Fakitale iliyonse ndiyosiyana ndipo njira yake iyenera kukhalanso yosiyana. Mafakitale ndiosiyana zochita ndi kukula, ndipo tili ndi magulu osiyanasiyana okana kusinthaku. Kotero njira yosinthira mafakitale opereka zinthu zofunikira monga za madzi kapena magetsi, zomwe chiwerengero chonse cha anthu chimadalira, iyenera kusiyana ndi mafakitale opanga zinthu omwe anthu ochepa ndiwo amakhudzidwa.

Pa nkhani ya bizinesi zing'onozing'ono, zitha kukhala zomveka kuwagulitsa kwa ochita malonda, makamaka ochokera m'mayiko akunja omwe atha kubwera ndi maganizo atsopano ndi mpamba. Koma kugulitsa makampani aboma kwa anthu ochokera kunja kutha kukhala kovuta.

Kwa malonda aakulu, kutha kukhala kofunika kumwaza umwini kwa anthu ambiri powagulitsa masheya. Koma izi zitha kufuna maphunziro ambiri, chifukwa patha kukhala msika wogulitsa masheya wochepea ndipo anthu ambiri sangadziwe kuti masheyawa ndi chani. Litagwa boma la Soviet Union, dziko la Russia linayamba kugulitsa 'ziphaso zaumwini' wamakampani aboma, zomwe zinathandizira kwambiri kuwapatsa anthu masheya ofanana mu kampani zaboma. Koma ambiri anagulitsa masheyawa motsika kwambiri, mapeto ake ulamuliro wamabizinezi unapita m'manja mwa kagulu katsopano kodziwika bwino.

Kuyambitsa mfundo za misika

Ndi kofunika kwambiri kuphwanya mphamvu za umwini wamakampani ngati mbali imodzi yopereka mphamvu kwa anthu oima paokha zoyendetsera bizinezi za boma. Maboma atha kuganiza kuti apeza phindu lambiri pogulitsa mabizinezi adakali ndi mphamvu, koma anthu ambiri amadana ndi mphamvu zotere. Ngati kampani yomwe imayendetsedwa ndi boma yagawidwa kukhala magawo angapo opikisana, boma ndi anthu onse adzapindula pakapita nthawi. Mabizinezi atsopanowa akhala amphamvu kwambiri, osinthika, komanso opanga zinthu mwaluso kusiyana ndi makampani omwe ankatsogozedwa ndi boma m'mbuyomo.

Maziko a dziko la ufulu

Kuchotsa ntchito zoyendetsa mafoni m’manja mwa boma kupita kwa anthu oima paokha ku Guatemala m’chaka cha 1996 kunasonyeza kufunika kwa mpikisano pa kachitidwe ka zinthu. Kumeneko, msika oyendetsa mafoni unatsegulidwa kuti makampani azipikisana ndi kampani yomwe inali ndi mwayi onsewo m’dzikolo isanagulitsidwe. Malo amlengalenganso anagulitsidwa, kupereka ufulu wa katundu ku gawo la mphamvu ya magetsi komanso yokoka ndi kumata zinthu, zomwe makampani atsopano olumikizitsa anthu amagula ndi kugwiritsa ntchito mosavuta. Mapeto ake anali kukula kwambiri kwa mpikisano, kubweretsa zisankho zambiri ndi kufikira patali. Mtengo unatsika kwambiri mu chigawo chaku Latin America, ndipo chiwengero cha anthu ogwiritsa ntchito mafoni chinakwera mazanamazana muzaka zosaposa khumi³³.

Kuchita molondola

Pali kudziwa kwakukulu kochokera m’mayiko akunja – ndi ukadaulo – zomwe zingathandize osintha zinthu kuti ndale ndi njira zosinthira umwini wa bizinezi zaboma ziyende bwino.

Chinthu chofunikira kwambiri n’chakuti ndondomeko yake ikhale yochitika poyera ndipo anthu onse aloledwe kutenga nawo mbali. Kupanda kutero, kusinthaku sikungavomeredzedwe ndi onse. Mwachitsanzo, maboma ena ku Africa achotsa m’manja mwaboma mafakitale oyendetsa za madzi ndi magetsi poitana makampani akunja, koma osapereka mwayi kuti anthu am’dzikolo akhale ndi umwini. Uku sikupusa pandale kokha, koma kutsutsananso ndi mfundo ya dziko la ufulu ya kuthandizana mofanana.

Kuwonjezera apo, ngati umwini ukuchepetsedwa m’malo momwazidwa, pali chopsezo cha makampani ochotsedwa m’manja mwabomawa kubwereranso n’kumalamuliridwa ndi anzawo a omwe ali m’boma. Izi zidzawononga ganizo logulitsa makampani a boma mtsogolo ndikubwezera m’mbuyo ntchito yoyambitsa mfundo

³³ See Wayne A. Leighton, ‘Getting privatisation right: a case study’, Institute of Economic Affairs blog, London, 2013.

zochitira malonda ku mbali zina zoyendetsedwa ndi boma. Anthu ayenera kutsimikiziridwa kuti ndondomeko iliyonse yatsopano yomwe ingabwere idzathandiza makasitomala. osati kagulu kochepa ka anthu akatangale. Kuyambitsa mpikisano, komanso mwachangu, ndi njira yabwino yotsimikizira izi.

Ntchito zotumikira anthu popanda boma

Pali kaganizidwe kena koti ntchito zotumikira anthu zina zitha kuperekedwa ndi boma lokha – makamaka zotumikira anthu monga zaumoyo, maphunziro ndi umoyo wa anthu.

Anthu ena amati ntchito zotumikirazi nzofunikira kwambiri moti siziyenera kuikidwa pamsika. Kunena zoono, nzofunika kwambiri moti siziyenera kusiyidwa m’manja mwaboma. Pamene opereka ntchito zotumikira anthu akupatsidwa ndalama kuchoka ku misonkho, oyendetsa ake sakuyenera kukondweretsa makasitomala kuti apeze ndalama, monga makampani omwe siaboma angachitire. Amapezera ndalama zoyendetsera ponyengerera andale kapena kuopseza kuti asiya kugwira ntchito ngati zofuna zawo sizikwaniritsidwa. Chidwi chawo chili pa boma osati anthu.

Makampani omwe siaboma amakhala pa mpikisano waukulu kusiyana ndi makampani aboma. Nthawi zambiri, kupikisana ndi makampani aboma sikulolelwa. Koterok makampani othandiza anthu aboma safunikanso kukhala ndi upangiri wapadera kapena kuyesetsa kuti kutumikira kwawo kugwirizane ndi makono, chifukwa makasitomala awo alibe kulikonse komwe angakadandaule.

Koma ngakhale maboma ambiri amafuna kuyendetsa okha ntchito zotumikira anthuzi, anthu amapeza njira zawo zachidule. Pali zitsanzo zambiri padziko lonse lapansi kumene mabungwe omwe siaboma ndi ena osavomerezeka amapereka kwa anthu chithandizo chofunikirachi – komanso kupereka bwino.

Maphunziro popanda boma

Titenge maphunziro mwachitsanzo. Anthu amaganiza kuti maphunziro asukulu zomwe sizaboma ndi a anthu achuma okha. Koma kafukufuku

Maziko a dziko la ufulu

wa zaka ziwiri yemwe anachitika ku India, Ghana, Nigeria ndi Kenya ndi katswiri pa maphunziro Porofesa James Tooley anapeza zosemphanana ndi izi. M'malo osaukitsitsa kwambiri m'mayikowa, ana asukulu ambiri amapita ku sukulu zomwe sizaboma. M'malo osaukitsitsa kwambiri aku Hyderabad, Accra, ndi Lagos, sukulu imodzi pa zitatu zilizonse kapena kuchepera apo zinali zaboma. Ana awiri pa atatu aliwonse kapena kuposera apo ankapita ku sukulu zomwe sizaboma, zambiri mwayizo zosavomerezedwa ndi boma. Anthu wamba ndiwomwe anali eni a sukulu zomwe sizabomazi. Ochepa kwambiri ndiwomwe amalandira thandizo lachifundo ndipo palibe sukulu yomwe imathandizidwa ndi boma – sukulu zinkathandizidwa ndi fizi yochokera kwa makolo, yomwe inalinsyo yochepa kwambiri³⁴.

Ngakhale zinali choncho, Tooley anapeza kuti kupambana kunali kokwererapo mu sukulu zomwe sizabomazi. Ku Hyderabad, wapakati okhonza masamu anali pamwamba kasanu kuyerekeza ndi okhonza waku sukulu zaboma – ngakhale malipiro a aphunzitsi a sukulu zomwe sizabomazi anali ochepera pafupifupi theka ndi kota ndi a aphunzitsi amsukulu zaboma. Muyezo wa zina unali okwererapo mofanana. Tooley anapeza aphunzitsi amsukulu zaboma akugona pa desiki. Ndipo kujomba kwa aphunzitsi kunali kwakukulu mu sukulu zaboma. Sukulu zomwe sizabomazi zinali ndima bolodi abwino, malo osewerera, madesiki, madzi akumwa ndi zimbuzi. (theka la sukulu zaboma zokha zinali ndi zimbuzi, kusiyantsa ndi sukulu makumi asanu ndi anayi ndi mphambu zisanu ndi imodzi (96%) kapena kuposa apo za sukulu zomwe sizaboma.) Mlingo wa ana oyenera kuphunzitsidwa ndi mphunzitsi mmodzi unali pafupifupi theka lamlingo wa sukulu za boma.

Boma linkaoneka ngati silikudziwa za kufunika kwa maphunziro operekedwa ndi sukulu zomwe sizaboma m'madera a anthu osauka. Boma la China linalembe mu kaundula mwake sukulu 44 zokha mu

³⁴ See James Towoley, *The Beautiful Tree: A Personal Journey into How the World's Poorest People Are Educating Themselves*, Cato Institute, Washington, DC, 2009.

Maziko a dziko la ufulu

dera lamapiri la Gansu, ngakhale kafukufuku wa Tooley anapeza sukulu zokwana 696, zomwe 593 zinkathandiza ana 61,000 m'midzi yakutali kwambiri. Sukulu zambiri zinkayendetsedwa ndi makolo komanso anthu am'mudzi. Sukulu zimayenda ngakhale malipiro a anthu mdera la Gansu anali pa \$150 pa chaka. Ngakhale ku Kibera, mdziko la Kenya – malo okhala anthu ochuluka kwambiri kum'mwera kwa Sahara kwa Africa, komwe kuli anthu pafupifupi 750000 – Tooley anapezako sukulu zomwe sizaboma zokwana 76 zomwe zinkaphunzitsa ana okwana 12000.

Kunena zoon, ngakhale m'malo osaukitsitsa pa dziko lapansi, sukulu zomwe sizaboma zitha ndipo zikupereka maphunziro apamwamba kusiyana ndi sukulu zaboma. Ndipo mtengo wake ndiwotsika kwambiri kuti mabanja osauka akwanitse. Boma likuoneka kuti sili-kufunikiratu pamaphunziro konse.

Sizodabwitsa kuti mayiko achuma, omwe ali ndi sukulu zambiri zoyendetsedwa ndi boma, amakhala ndi chidwi chobweretsa mpikisanowu ndi chisankho cha makolo pa maphunziro. M'chaka cha 1991, dziko la Sweden linabweretsa ndondomeko yatsopano yomwe boma linapitiriza kulipira zofunikira pa maphunziro, koma magulu ena ofuna kupeza phindu ndi osafuna phindu oima paokha anali ndi kuthekera koyambitsa sukulu zawo kuti apeze ndalama zoyendetse-razi, potengera ndi kuchuluka kwa ana omwe anali nawo. Ngakhale otsutsa monga bungwe lomenyera ufulu wa aphunzitsi omwe sankagwirizana nako kusinthaku poyambirira, pano linavomereza, izi zakhudza kuyendetsa bwino, upangiri watsopano ndi ubwino wa sukulu zoposa chikwi zatsopano zomwe zinayambitsidwa – makamaka m'madera ovuta ndi osaukitsitsa. Pano mayiko ambiri akuyambitsa ndondomeko yomweyi.

Chisamaliro cha zaumoyo opanda boma

Chisamaliro cha zaumoyo ndi ntchito inanso yofunikira kwambiri yomwe m'mayiko ambiri amasiyira boma – lomwe limatetezedwa nthawi zambiri kwa opikisana nawo pokhala ndi malamulo olikomera, kuthandizidwa ndi ndalama za misonkho komanso ndi malamulo ena.

Maziko a dziko la ufulu

Izinso zimaika chidwi cha ogwira ntchito m'boma pa kupeza ndalama zambiri ndi mwayi waukulu m'bomamo, kusiyana ndi kuthandiza bwino odwala.

Dziko la United States limadzudzulidwa nthawi zambiri chifukwa cha kukwera mtengo kwa ndondomeko yake yaufulu yoperekera chithandizo cha zaumoyo wa anthu. Ndiyokwera mtengo; koma chilungamo chake ndi imodzi mwa ndondomeko zoyendetsedwa bwino kwambiri padziko lapansi, ndipo ndalama zomwe limapereka pa chaka ndi zochulukira pa nambala yachitatu dziko lonse lapansi (pambuyo pa Norway ndi Luxembourg). Msonkho ndi malamulo ena amaika inshuransi ya chisamaliro cha zaumoyo kwa ogwira ntchito – zomwe zimawasiya anthu kukhala osatetezeka pamene akusaka ntchito. Koma ogwira ntchito (molimbikitsidwa ndi madokotala) amafuna kuyezedwa ndi chithandizo chomwe sichoyenerera panthawiyi chifukwa amadziwa kuti amalipira ndi owalemba ntchito osati iwo eni. Malamulowa amanenanso zomwe zikuyenera kuphatikizidwa mu inshuransi ya chipatala ndi m'mene ikuyenera kugulitsidwira (mwachitsanzo, kuika malire kwa okhoma inshuransi kuti izigwira ntchito mu dera lakwawo lokha, kuwalepheretsa kuti asawononge ndalama zambiri). Chimodzimodzi, mchitidwe wa azachipatala umayendetsedwa ndi zoyenera zomwe zimakonzedwa kwambiri ndi madokotala omwewo – kuloleza ntchito yawo kuchepetsa chwerengero cha madokotala ndi kukhala ndi malipiro awo okwera. Ndongomeko zonsezi (ndi zina zambiri) zikuwonjezera pa mtengo wa chisamaliro cha zaumoyo ku United States.

Mosiyana, dziko la Singapore – dziko laling'ono lomwe ndilolemera kuposa dziko la USA – limagwiritsa ntchito ndalama zomwe zikulowa pa mlingo wa kasanu ndi kamodzi pofanizira ndalama zomwe dziko la America limagwiritsa ntchito pa ndondomeko zothandizira ntchito zaumoyo. Zimangofuna mabanja asunge ndalama za mlingo wa imodzi pa zisanu zilizonse za ndalama yomwe amapeza ku chisamaliro cha umoyo wawo, kupuma pa ntchito, mtengo wa nyumba (ngakhale pali pologalamu yaboma yothandizira zofunikira zazikulu za chipatala). Pakuti anthu akusunga mu thumba la zaumoyo zikuwapangitsa kuti apeze chithandizo chabwino, ndi madokotala

akufuna kwawo ndi zipatala zogwirizana ndi ndalama zawo. Ku Switzerland, kulibe inshuransi yoyendetsedwa ndi boma: anthu amagula inshuransi ndi chithandizo cha kuchipatala kwa omwe siaboma. Ntchito yaboma ndi kuthandizira— osati kwa opereka chithandizowa koma kwa odwala omwe sangakwanitse kulipira chisamaliro cha umoyo wawo. Kotero, kusiyana ndi nzika zaku America, nzika zaku Switzerland zimaonetsetsa kuti zipeze chithandizo chogwirizana ndi ndalama zomwe amalipira pa chisamaliro cha zau-moyo. Mayiko ambiri aku ulaya amaona ndondomeko ya chisamaliro cha zaumoyo yoperekedwa kwa aliyense ya ku Switzerland kuti ndi yapamwamba kwambiri padziko lonse lapansi.

Kusamalira umoyo popanda boma

Njira yabwino yosamalira umoyo wamunthu osauka ndiyokhala ndi ntchito yolipidwa. Koma ndondomeko za boma zoyang'anira umoyo wamunthu zimawononga ntchito. Mbali zambiri ku Ulaya, inshuransi ya umoyo imapatsidwa ndalama kuchokera ku msonkho wina pa ogwira ntchito, zomwe zimakweza mtengo kwa olemba anthu ntchito ndikuwapangitsa kuti alembenso antchito anthu atsopano. Izi zikutanthauza anthu ambiri osagwira ntchito kupindulira pa ogwira ntchito, zomwe zimafuna kuti msonkho ukwere kuti ndalamazo zipezeke, zomwe zimapangitsa kuti anthu asalembedwe ambiri. Ndi njira yobwerera m'mbuyo.

Sweden lidali dziko la ufulu, la msonkho ochepa komanso lotukuka kwambiri kufikira zaka makumi angapo zomwe zinadutsa. Koma kwa zaka makumi awiri linayamba kuika misonkho yokwera kuti apeze ndalama zoyendetsera mapologalamu azaumoyo. (Ndithudi, m'chaka cha 1976, olemba mabuku wina waku Sweden anadandaula kuti msokho wake wakwera kufika mlingo pa 102 pa 100 iliyonse!) Misonkho yokwera chonchi inali yosalimbikitsa kugwira ntchito ndi kuchita malonda. Izi zinapangitsa dziko la Sweden kuti lisatukuke kwa zaka makumi awiri, kufikira pamene mfundoyi inayamba kusinthidwa mu zaka zam'ma 1990.

Mayiko a ufulu amakhala olemera; ndipo mayiko achuma amakonda

Maziko a dziko la ufulu

kupereka ndalama zambiri kuthandiza omwe ndiosowa. Uwu ndi mkhalidwe wabwino kusiyana ndikuti maboma azitenga ndalama kwa anthu kudzera mu msonkho ndi kugwiritsa ntchito pa mapologalamu a umoyo omwe iwo awakonza okha – ndipo osangoti chifukwa boma limakonda kupereka phindu kwa anzawo ndi kuika misonkho yokwera pa adani awo. Ntchito yachifundo yeniyeni ndiyodzipereka kuchokera kwa munthu kupita kwa wina, osati kukakamizidwa.

Vuto lina la ndondomeko zaboma zosamalira umoyo wa anthu ndi m'mene amakhazikitsira khalidwe lodalira. Chifukwa cha kukula, komanso kuyendetsedwa ndi ogwira ntchito m'boma, zimayendetsedwa kwambiri motengera malamulo, osati kafukufuku wa munthu pa zofuna ndi kuthekera kwa othandizidwa, monga m'mene opereka mwachifundo enieni amachitira. Izi zimawalimbikitsa anthu kusewera ndi malamulo kuti akhale oyenera chithandizo. Nthawi zina, mabanja osauka amaipitsa zomwe akukumana nazo kuti akhale oloedwa kulandira phindu lochuluka – motsutsana ndi zomwe tikufuna kukwaniritsa. M'mayiko akale koma aakulu pa chisamaliro cha umoyo wa anthu monga United Kingdom, adindo ayamba kuona 'kudalira kwa m'badwo wachitatu' – mabanja kudalira chithandizo zomwe makolo ndi agogo awo ankachitanso.

Kudzithandiza kwa munthu yekha, kothandizidwa ndi azachifundo ena, ndikwabwino, njira yolimbikitsa ndi yokhazikika. Dziko la UK lidali ndi ndondomeko yabwino yoyang'anira umoyo wa ogwira ntchito chisadafike chaka cha 1940, pamene boma loyang'anira umoyo wa anthu lidayichotsa. Awa adali mabungwe abwino, m'mene anthu ankatha kupereka ndalama pa sabata iliyonse posinthanitsa ndi phindu monga, malipiro pamene usakugwira ntchito, inshuransi ya chipatala, ngakhale ndalama zogwiritsa ntchito pa maliro. Nthawi zambiri ankaika chidwi pa ntchito zina, kuti akwaniritse zofuna za antchitowo. Mamiliyoni amabanja, makamaka mabanja osauka, ankasankha kulowa nawo limodzi mwa mabungwewa. Chisamaliro cha umoyo wa onse, popanda boma, ndichotheka.

Kudzutsanso gawo lothandiza anthu

Anthu ambiri omwe amakhala m'mayiko momwe ndondomeko zosamalira umoyo wa anthu ndi zapamwamba kwambiri amati kupereka kwachifundo kwa anthu wamba sikungalowe m'malo mwa chithandizo chomwe chimatoleredwa kuchokera kumisonkho ndi ndalama zomwe anthu amalandira akapuma pantchito. Ndikosavuta kuti boma lioneke lopatsa ndi ndalama zaeni, ndipo pamakhala chilimbikitso chomwe chimapangitsa andale kulonjeza zithandizo zikuluzikulu, chonsecho akudziwa kuti mibadwo yomwe ikubwera ndiyomwe idzalipire. Ichi chingakhale chifukwa chabwino chochosera andale mu ndondomeko zothandiza anthu. Komanso kuwonjezera apo, ngati thandizo laboma lili lochuluka, chilimbikitso cha mabanja kuti adzipezere chakudya chitha kukhala chochepa ndinso cha anthu kuti asankhe ntchito m'malo mongodalira thandizolo – chifukwa zikutanthauza kuti omwe ali pantchito ayenera kupereka msonkho ochuluka kuti ithandizire ndondomeko zosamalira umoyo wa anthuyi. Ngakhale cholinga chili chabwino, mapeto ake ndiwochotsa anthu chiyembekezo ndi khumbo ndi kuwayika m'moyo omangodalira.

Mayiko omwe akufuna kuyenda munjira ya ufulu ayenera kuyamba kuphwanya ndondomeko zikuluzikulu zosamalira umoyo wa anthu kukhala zazing'ono komanso zokomera anthu akudera. Zitha kukhala mosankha munthu m'modzi pomutsekulira buku laku banki. Izi zitha kupangitsa mabanja kuzindikira udindo wawo, komanso kumvetsetsa kuti akuthandizidwa ndi opereka msonkho enieni osati ndondomeko yosadziwika bwino. Ndipo ndondomekoyi ikamwazidwa chonchi, zimathandiza kuti iziyendetsedwa bwino ndi mabungwe omwe siaboma.

Chitsanzo ndi ndondomeko ya penshoni m'dziko la Chile. Mchaka cha 1989, dzikoli lidagawa ndondomeko yake yomwe inkalephereka komanso yokondera kukhala yolandirira ku banki. Ogwira ntchito amayenera kusunga ndalama kukonzekera kupuma pa ntchito, koma amatha kusankha pakati pa makampani angapo omwe siaboma kuti awasungire ndalama zawo. Ndongomekoyi idapititsa patsogolo

Maziko a dziko la ufulu

udindo wa munthu posunga ndalama, komanso kupereka ndalama zabwino kwa ogwira ntchito, ndipo mayiko angapo adatengera.

Chitsanzo china chabwino ndi ndondomeko yaku Singapore yosungira ndalama zodzithandizira ukafuna chisamaliro cha chipatala, yomwe imaika udindo pa munthu ndi mabanja, kuwalimbikitsa anthu kudzipezera okha chithandizo umoyo wawo ndi zina. Mabungwe a m'dziko la United Kingdom othandiza anthu achikulire ndi chitsanzo chinanso chomwe chitha kutsatidwanso mosavuta pogawa chithandizo chaboma ku akaunti yamunthu ya kubanki.

Pamene njira yolephera yaboma yasinthidwa motere, pali chilimbikitso chachikulu kuti anthu afunefune ntchito ndi kudzidalira paokha ndi thandizo lochoka kumabanja awo, kusiyana ndi kudalira boma. Patha kufunikabe thandizo ndi ntchito zachifundo zomwe sizaboma, koma likhala pa mlingo woti litha kuyendetsedwa mosavuta. Ndipo, monga taonera, ufulu ndi misonkho yochepera ndi njira yabwino yowapatsira anthu chifuniro ndi chuma choti akhale opatsa, cholinga chimene boma lalikulu ndi la misonkho yokwera limachotsa.

Kulumikizana kwa mayiko onse ndi malonda

Phindu lofalikira ku mayiko onse

Monga dziko la Nepal, mayiko ambiri ndiwokhudzidwa ndi m'mene kukula kwa misika yofalikira padziko lonse kungawakhudzire. Koma kukhuzika kwambiriku nkolakwika, ndipo ubwino wa kufalikira kumayiko onse ndi malonda ndi waukulu.

Tithokoze njira zoyendetsera mitengo ya zinthu pamsika, pano titha kuchita malonda molunjika kapena molambalala ndi anthu a padziko lonse lapansi. Zovala zomwe timavala, chakudya chomwe timadya, zida zomwe zili mnyumba zathu, m'maofesi ndi m'mafakitale, zonsezi ndi zopangidwa m'mayiko ambirimbiri akutali.

Koma misika ya padziko lonse imathandiza kufalikira mbali zonse. Sikuti zimangolola mayiko olemera kugula zinthu kuchokera m'mayiko osiyanasiyana. Zimathanso kuthandiza anthu omwe anali m'madera akutali kupititsa patsogolo zokhumba zawo pofikitsa katundu wawo pamsika wa mayiko akunja ndi katundu wawo. Ndi

Maziko a dziko la ufulu

mbewu zANJI, mwachitsanzo, zomwe mlimi wakumudzi akuyenera kulima? M'mbuyomu, uthenga wa mitengo ya mbewu umachokera kwa amalonda am'midzi ndi mabungwe aboma, omwenso amakhala ndi zofuna zawo. Mitengo ya katundu m'misika yakumidzi inkatha kusintha nthawi iliyonse, motengera zinthu zina monga nyengo. Ndipo misika yakudera siyinali ya dongosolo. Lero, mlimi atha kungotenga foni yake yammanja ndikuona pa matsamba a intaneti angapo omwe amaonetsa mitengo pamsika – kuphatikizanso mitengo yamtzogolo – pafupifupi ya mbewu iliyonse, mu misika yosaweregeka padziko lonse lapansi. Alimi kulikonse akhoza kugulitsa m'misika ya mayiko akunja, yadongosolo, pa mitengo yodziwikiratu.

Kutseguka kwa dziko la New Zealand

New Zealand ndi chitsanzo cha dziko lomwe lidatembenuka posiya malamulo ena azachuma ndi malonda. Mu zaka zam'ma 1980, dzikoli lidali pamavuto aakulu okhudza zachuma chifukwa cha malamulowa. Koma, kuyambira m'chaka cha 1984, linasiya kuteteza ndi kumasula msika wake wamalonda kumayiko onse, ndikutsegula misika yawo ku mpikisano wamayiko onse. Kuthandizira gawo lina kumakampani ndi ku ulimi kudachotsedwa. Malamulo m'misika yam'dzikomo anachotsedwa, kuphatikiza misika yolembe ntchito anthu yomwe idali ndi malamulo kwambiri: kulowa mu bungwe la omenyera ufulu wa ogwira ntchito sikunali kokakamiza. ndipo migwirizano idasiyidwa kukhala pakati pa ogwira ntchito ndi mabwana awo.

Kupenekera kochokera kwa onyengerera, azamaphunziro, atsogoleri amipingo, ndi atsogoleri omenyera ufulu – kuti kuchotsa malamulo kupangitsa anthu kuti azigwira ntchito kwambiri ndi kulipidwa mochepe– kunakhala kosalondola. Malipiro a mlingo woyerekeza a anthu adakwera. Migwirizano ya malipiro inamvetsetseka mwachangu kwambiri. Kusowa kwa ntchito kudatsika – ndipo kudatsika kwambiri pakati pa nzika, anthu obwera ndi magulu ena osauka ndi omwe adalibe mwayi. New Zealand linakhala limodzi mwa mayiko a ufulu ndi a mpikisano kwambiri padziko lapansi³⁵.

³⁵ For an outline by the architect of these reforms, see Roger Douglas, *Toward Prosperity*, David Bateman, Auckland, NZ, 1987.

Maziko a dziko la ufulu

Kudziwika kwa chikhalidwe

Anthu ena amada nkhawa kuti mchitidwe wochita malonda padziko lonse ukhoza kuwononga chizindikiro ndi chikhalidwe chapadera cha mayiko. Mwapadera kufalikira kwa zizindikiro za katundu waku America zimapereka nkhawa kuti mayiko omwe ankaoneka mosiyana ayamba kuoneka mofanana, kuti katundu waku Ulaya ndi makhalidwe zikwirira katundu ndi makhalidwe a mayiko ena, ndipo kuti mayiko achikhalidwe chokhazikika azindikira atasinthidwa ndi mayiko omwe ali aang'ono.

Zoonadi, nkhani zachuma ndi chikhalidwe cha anthu zikusintha. Katundu yemwe adali opezeka m'dziko limodzi lokha pano akupezeka m'misewu ya mayiko onse. Izi sizikutanthauza kuti zisankho ndi kusiyanasiyana kwa zinthu zikutha. Mosiyana ndi izi, zikutanthauza kuti pano anthu am'dziko lililonse ali ndi chisankho chochuluka kusiyana ndi mmene zinalili kale. Mwachitsanzo, nzika zaku United Kingdom, sizingavutikenso ndi chakudya chosakoma komanso chophikidwa mopitirira muyezo chomwe dziko lawo lidatichuka nacho. Pano atha kupeza mogulitsa zakudya mitundu yosiyanasiyana ya zakudya zam'mayiko monga India, Vietnam, Latin America, Iran, Mongolia, Poland ndi mayiko ena. Ndiponso ena padziko lonse lapansi akusangalala chifukwa cha mwayi wa zisankho zambirimbiriwu – zisankho zomwe zinali za okhawa omwe adali achuma chomwe chimawathandiza kupita m'mayiko ena. Sikuti zikhalidwe zikutayika; koma zikufalikira kuti aliyense atha kusangalala nazo.

Chikhalidwe sichikhala chosasinthika, monga m'mene omwe amafuna kuchiteteza ku kufalikira kwa zinthu m'mayiko onse amanenera. Chikhalidwe cha dziko chimasintha nthawi zonse, ndipo pamene chikhalidwe chikukhala chenicheni ndi champhamvu, ndipomwe chimatulutsa maganizo atsopano komanso kusintha kwambiri. Luso, nyimbo, zolembalemba, zokonda ndi mavalidwe azikhalidwe za mayiko ambiri lero zitha kukhala zosadziwika kwa anthu omwe anakhala mchikhalidwecho zaka zana zapitazo.

Zikhalidwe zimapindula polumikizana ndi zikhalidwe zina, kuwalola anthu kusankha zinthu zomwe zikugwirizana ndi nthawi ndi miyoyo yawo. Pochita malonda ndi mayiko ena timaona ndikumvetsetsa zachikhalidwe cha mayiko akunja zomwe timazona zofunika ndi kuzitenga kuti ziphatikizane ndi zathu. Koma dongosolo la kusintha kumeneku linkachitikabe kuyambira kale mwinanso wina aliyense asanakambe za kufalitsa zinthu m'mayiko ena.

Ndipo kusintha kwambiri komwe timakudandawula, kutayika kwa magawo abwino a chikhalidwe chathu, sichifukwa cha mphamvu ya chikhalidwe cha mayiko akunja koma ndi zotsatira za kutukuka. Miyambo yakale, zikhalidwe ndi kuvala kosonyeza dziko lathu kunasowa, osati chifukwa cha kufalikira kwa zinthu m'mayiko onse, koma chifukwa choti moyo pawokha ukusintha. Zisangalalo zomwe zinkaonetsera nyengo zosiyanasiyana zinali zofunika m'madera a anthu omwe ankadalira ulimi, koma pano zilibe tanthauzo kwenikweni ndi dziko lomwe pafupifupi theka la anthu likukhala m'mizinda³⁶.

Koma mwina zimakhala bwino kuti zikhalidwe zisinthe. Zikhalidwe za m'mayiko ambiri zinaumirizidwa pa anthu ndi omwe amawalamulira, ndipo zikhalidwe zambiri zam'mayiko ambiri opanda ufulu ndi zowononga. Tikuyenera kulandira ganizo lakuti kutukuka pa mayendedwe ndi kufunsa kwambiri kwapangitsa kukhala kovuta kuti mayiko akhalebe ndi zikhalidwe zomwe magulu ena ankazunzidwa, kuponderezedwa ndi kusolidwa.

Funso: kodi mayiko olemera sakulanda kwambiri chuma cha dziko lapansi?

Ayi. Chuma ndi chinthu chomwe umachita kupanga kudzera mu luso, bizinezi, mphamvu, kulimbikira, dongosolo ndi kuika ndalama mu zinthu zobweretsa chuma. Nzoona mayiko olemera amagwiritsa ntchito chuma chambiri, koma amachipanganso. Komanso osangoti kwaiwo okha: amapeza ndi

³⁶ For these points, see Mariwo Vargas Llosa, 'The culture of liberty', in Tom G. Palmer, *The Morality of Capitalism*, Students for Liberty and Atlas Foundation, Arlington, VA, 2011.

Maziko a dziko la ufulu

kupanga katundu ndi ndondomeko zofunika zomwe zimatukula miyoyo ya aliyense, makamaka miyoyo ya anthu osaukitsitsa padziko lapansi.

Mwachitsanzo, kupita patsogolo pankhani yamankhwala, kumathandiza kuthana ndi ena mwa matenda ovuta kwambiri padziko lapansi monga chifuwa chachikulu ndi malungo. Luso lopanga mbewu mwamakono likuthandiza kuchulutsa zokolola ndi kupangitsa mpunga ndi mbewu zina zodalirika kuti zikhale zopirira ku zilombo zowonga. Katundu watsopano akupangitsa nyumba kumangidwa motsika mtengo komanso motetezeka.

Palibe komwe kumapezeka chuma chongokhazikika, kuti mayiko olemera amatenga gawo lambiri mosaganizira ena. Mosiyana, ukadaulo wa m'mayiko olemera ukupereka mwayi kwa ena.

Kufunika kwa mtendere

Adam Smith adalembapo kuti: 'ndizopanda pake kulemeretsa dziko kwambiri kuchoka ku umphawi wadzaoneni koposa kukhala ndi mtendere, misonkho yosavuta ndi kayendetsedwe ka chilungamo kovomerezeka...'³⁷

Mtendere mdziko ndi m'mayiko akunja ndi chofunikira mdziko la ufulu pachuma lomwe likuchita bwino. Anthu sangaika ndalama zawo m'malonda ndi kupanga mpamba opindulitsa ngati akukhulupilirira kuti chuma chawo chitha kudzabedwa ndi asirikali kapena adani a dziko lina. Ndipo mayiko omwe nzika zawo zikupanga malonda ndi nzika za mayiko ena sangafune kuchitirana za mtopola. M'mawu omwe adanenedwa ndi katswiri pa nkhani zachuma komanso ndale wa m'zaka za 1900 Frederic Bastiat: 'ngati katundu sadutsa malire adziko, asirikali adutsa'³⁸.

³⁷ Lecture in 1755, quwoted in Duguld Stewart, Account of the Life and Writings of Adam Smith LLD, Section IV, 25.

³⁸ There is no evidence that Bastiat actually said these words, but they sum up his point of view. See Frédéric Bastiat, Bastiat's 'The Law', Institute of Economic Affairs, London, 2001 [1850].

Phindu la mtendere limakhudza chuma ndi chikhalidwe. Mtendere umalola mphamvu ndi zipangizo kukhazikika pa zochitika zopindulitsa kusiyana ndi zowononga. Zimapereka mpata opangira mpamba ndi kupititsa patsogolo chitukuko cha dziko la ufulu pachuma. Mtendere umawalola anthu kukonza za tsogolo lawo ndi mabanja awo. Umawapatsa nthawi, chuma, ndi chilimbikitso chokwaniritsa zofuna zawo pa chikhalidwe ndi maphunziro. Ndiponso mtendere umalola anthu, katundu ndi maganizo kuyenda momasuka – kufalitsa kumvetsetsa, chitukuko ndi luso lopangira zinthu.

Ganizo lina la Adam Smith lidali lakuti sitikufunika kusaukitsa mayiko ena kuti tikhale olemera ife eni. Ndizabwino kwaife ngati makasitomala athu ali olemera kusiyana ndi osauka³⁹. Momwemonso, kuti tikhale amphamvu, sitikuyenera kuwapanga ena kukhala ofooka.

Mbali zonse zimapindula ndi phindu la mtendere.

Mtendere uyenera, nthawi ndi nthawi, kumenyeredwa nkhondo. Katundu ndi anthu ayenera kutetezedwa. Ndipo kutetezera zonse zofunikazi kutha kufuna kulowererapo kwaboma mwamalire. Koma maboma omwe amakhala ndi mphamvu kwambiri amasanduka ankhanza – mwina pofuna kubisa kusowa kwa chitukuko ndi ufulu wawo popereka ganizo lakuti chitetezo cha dziko chimafuna kudzipereka, kugwirizana pa cholinga chimodzi ndi mphamvu. Anthu m'mayiko a ufulu sikuti ndiwosakhulupirika ku mayiko awo; koma kudzipereka kwawo kumapita ku dziko la ufulu ndi lomasuka, ndiku mabanja awo, anzawo, makasitomala, ndi magulu odzipereka – osati olamulira ankhanza, mbendera kapena maloto a anthu ofuna mphumvu zoyendetsera chuma zikhale mmanja mwa boma.

Anthu ena amaganiza kuti njira yabwino yokhala ndi mtendere ndi njira yokhazikitsa boma lolamulira mayiko onse. Ngakhale kuli kofunika kukhala ndi mabungwe a mayiko onse amene tingakambirane

³⁹. As a rich man is likely to be a better customer to the industriwous people of his neighbourhowod than a powor, so likewise is a rich nation.' Adam Smith, *The Wealth of Nations*, 1776, Bowok IV, ch. III, Part II.

Maziko a dziko la ufulu

zosiyana zathu ndi kuthetsera mikangano yathu, tisaganize kuti boma ladziko lonse lingakhale labwino kuposa mayiko athu alipo kalewa. Potengera kukula kwake, ndi kotalikana kwambiri ndi anthu, khalidwe lake lofuna kukula ndi kusagwiritsa bwino ntchito mphamvu zake kutha kukhala kwakukulu. Ndipo palibe yemwe angazembe nkhanzazo pothawira mbali ina yadziko. Ayi, njira yabwino yopititsira patsogolo mtendere ndiyopanga maboma kukhala aang'ono, osati kuwakulitsa, ndi kudalira khalidwe lachibadwa la anthu lofuna kugwirizana mwamtendere ndi kutukula umoyo wawo.

9 NKHANI YONSE MWACHIDULE

Nkhani ya ufulu

Ufulu umadzetsa chitukuko. Madera omwe anavomereza ufulu ama-
lemera. Omwe sanavomereze amakhalabe osauka.

Koma dziko la ufulu ndilotsogolanso munjira zosakhala za katundu. Limayendetsedwa potengera kudalirana ndi mgwirizano pakati pa anthu, osati potengera mphamvu ndi kuumirizana. Nzika zake zimalumikizana pa mfundo zachikhalidwe ndi zaumunthu komanso zamakhalidwe zofanana. Amavomereza malamulo achikhalidwe cha anthu ena mosakakamizika, mopindulira onse, osati chifukwa malamulowa angokakamizidwa pa iwo. Boma lawo ndilovomerezeka ndi omwe akulamuliridwa, ndipo iwo eni akulamuliridwa ndi malamulo omwe amawateteza kuti adindo asawapondereze.

Dziko la ufulu limatukula luso la anthu, kuyambitsa zinthu zatsopano ndi zaluso. Izi zimathandiza kupanga chuma pomwe panalibe. Anthu mudziko la ufulu samakhala achuma popondereza ena, monga kagulu ka anthu ochepa m'mayiko opanda ufulu kamachitira. Sangalemere posaukitsa ena. Amalemera powapatsa ena zomwe akufuna ndi kutukula miyoyo ya anthu ena.

Boma lokhala ndi malire

Anthu ambiri amavomereza kuti boma limafunika pa zolinga monga kupereka chilungamo ndi kupereka chiganizo pazinthu zomwe anthu sangachite paiwo okha. Koma pafupifupi aliyense amavomereza kuti mphamvu zaboma ziyenera kukhala ndi malire. Boma la dziko la ufulu limakhalapo kuti liteteze nzika zake kuti zisapwetekedwe. Limakhazikitsa ndi kukakamiza chilungamo – malamulo achibadwa omwe amawathandiza anthu kugwirizana mwamtendere limodzi.

Boma la dziko la ufulu limakakamizidwa ndi mphamvu ya lamulo. Malamulo ake amagwira ntchito pa aliyense mofanana. Atsogoleri ake samapondereza nzika zawo ku phindu la iwo eni, kupereka mwayi kwa anzawo, kapena kugwiritsa ntchito mphamvu zawo pofuna kuthana ndi adani awo. Mphamvu zawo ndi nthawi yawo mu

Maziko a dziko la ufulu

ofesi ili ndi malire pofuna kuchepetsa katangale yemwe amabwera ndi udindo. Nsanamira za demokalase monga zisankho zamtendere ndi za ufulu, ufulu wamunthu oyankhula maganizo ake, malire azaka zaulamuliro wa atsogoleri ndi malamulo oyendetsera dziko, zonsezi kuika malire pa atsogoleri andale.

Kufanana kwakukulu

Opindula kwambiri pa zochitikachitika pachuma m'dziko la ufulu ndi anthu osauka. Mayiko a ufulu ali ofanana kwambiri pachuma kusiyana ndi mayiko omwe alibe ufulu. Osauka m'mayiko a ufulu kwambiri amasangalala ndi zambiri zomwe ankangozilota zaka zingapo zapitazo, zosangalatsa zomwe zimapezeka ku kagulu kochepa kolamulira m'mayiko opanda ufulu.

Dziko la ufulu siliyeesera kukakamiza kufanana pa chuma. Limadziwa kuti kuyesera kufananitsa chuma kapena ndalama ndikobwezeretsana m'mbuyo. Kumawononga chilimbikitso chodzitukula munthu payekha, kulimbikira ndi malonda. Sizilimbikitsa anthu kupanga mpamba womwe umatukula dziko lonse. Kumalepheretsa anthu kupanga chuma chatsopano ndi zikhulupiriro zatsopano.

Koma dziko la ufulu limasangalala ndi kufanana kwakukulu komwe sikupezeka m'mayiko opanda ufulu. Makhalidwe a anthu amalemekezedwa: moyo uliwonse wamunthu umaonedwa kukhala ofunika ndi oyenera kutetezedwa. Pali kufanana pa lamulo: chiweruzo chimatengera mfundo za mlanduwo, osayang'anira kuti iwe ndi ndani. Nzika zimafanana pa ndale: ndizoyeneredwa kuvota, kuima pa zisankho, kukamba mfundo zawo pandale, ngakhale adindo sangasangalale nazo. Ndipo ali ndi kufanana popeza mwayi: anthu samakumana ndi tsankho pantchito kapena pamaphunziro ndipo atha kudzitukula okha osatengera mtundu wawo, chipembedzo, kapena chilichonse.

Ufulu pa chuma

Dziko la ufulu limawapatsa anthu ufulu opanga zisankho zawo pachuma, monga m'mene limawasiyira kupanga zisankho pagulu

komanso pamoyo wawo. Anthu m'dziko la ufulu amapanga phindu kudzera mu msintho odzipereka. Kusinthana mwa ufulu kumatukula mbali zonse: sangachitirensa mwina.

Anthu amatukuka pogwira ntchito limodzi ndi ena komanso kupereka katundu yemwe anthu akumufuna – ndi kupeza zomwe akufuna mapeto ake. Chiyembekezo chopindula chimalimbikitsa azamalonda kufufuza zomwe anthu akufuna ndi kuwapatsa. Mitengo imatumiza uthenga wa kusowa ndi kuchuluka, kuuza aliyense chomwe chikuyenera kupangidwa ndi kusungidwa. Munjira iyi, nthawi, luso, mphamvu, mpamba ndi katundu wina amatengedwa kupita komwe akufunika kwambiri ndi kuchotsedwa komwe sakufunika kwenikweni. Sipasowekera boma kuchita kuwauza anthu chochita.

Kuti ligwire ntchito, dziko la ufulu pachuma lingofunika ndondomeko ya malamulo ovomerezeka a m'mene anthu akuyenera kugwirira ntchito limodzi. Izi zikuphatikiza za umwini ndi kusinthana kwa katundu, ndi malamulo amgwirizano m'mene mapangano amalemekezedwera. Katundu wa anthu ngwofunika ngati anthu angapange mabizinezi ndi kusinthana katundu. Komanso ndichofunika ngati ufulu wina ukuyenera kulemekezedwa. Ngati adindo akukhala ndi ulamuliro pa katundu yense, kuchitapo kanthu pandale ndi mtsutso wapagulu sikungatheke.

Chilungamo ndi mphamvu ya lamulo

Chilungamo sichintha chomwe chingangolankhulidwa ndi aphungu opanga malamulo. Malamulo achilungamo ndi mbali imodzi ya umunthu wa munthu – mbali yofunikira kwambiri yomwe imathandizira kupititsa patsogolo mgwirizano wamtendere pakati pa anthu.

Anthu m'dziko la ufulu ali ndi ufulu wa chilungamo chachibadwidwe pokhala anthu. Chilungamo chachibadwidwe chimati malamulo ayenera kukhala omveka bwino ndi wodziwikiratu, kuti athandize anthu mofanana, kuti asafune zinthu zosatheka, kuti asabwezeretse zinthu m'mbuyo, ndinso kuti zilango ndizodziwikiratu komanso zolingana ndi mlanduwo. Payenera kukhala ndondomeko zoyenerera

Maziko a dziko la ufulu

za malamulo pa milandu yonse, ndi kuzenga kosakondera ndi kusa-sungidwa nthawi yayitali usanazengedwe mlandu. Anthu omwe akuganiziridwa kuti ndiwolakwa ayenera kutengedwa ngati osalakwa mpaka atapezedwa olakwa, ndipo anthu sakuyenera kuzunzidwa ndi kuzengedwa mlandu omweomwewo kangapo. Mfundo zoterezi ndi-zovomerezeka ndi aliyense, osatengera dziko lomwe akuchokera, chikhalidwe, mtundu kapena chipembedzo.

Kuti chilungamo ndi mphamvu ya lamulo zikhazikike pakufunika nthambi yoweruza milandu yoima payokha yomwe siyingakakamizike kuchita zinthu chifukwa cha andale. Apolisi, nawonso, ayenera kukhala oima paokha. Ziphuphu ndi katangale sizingaloledwe pakati pa apolisi ndi oweruza milandu ngati ufuluwu ukuyenera kukhazikika.

Dziko losakakamizika

Dziko la ufulu ndi dziko losakakamizika. Limamangidwa potengera zochita za anthu, potsata malamulo omwe amapititsa patsogolo mgwirizano wamtendere. Silikakamizidwa ndi adindo.

Anthu sakuyenera kumvana pa chilichonse kuti agwirizane pa mfundo yopindulira onse. Omwe akusinthana katundu ayenera kumvana pa mtengo. Koma kuti mgwirizanowo ukhale opindula, anthu ayenera kulolera maganizo ndi zochita za anzawo. Dziko la ufulu limalola anthu kapena boma kulowererapo pa anthu kuti asapwetekane. Kuika malire pa ufulu wa anthu chifukwa tikuona khalidwe lawo kukhala losavomerezeka kapena lolakwika kumachotsa chiletso chilichonse chotsutsana ndi ufulu wamunthu omwe ukuimitsidwa ndi anthu ena omwe akuziona kuti ali ndi khalidwe lopambana.

Kulolera maganizo ndi khalidwe la anthu ena kumapindulira dera. Chilungamo sichikhala chodziwikiratu; chimapezeka pa mpikisano wa maganizo. Sitingawakhulupirire ochita kauniuni kuti aziponde-reza maganizo olakwika okhaokha. Atha kuletsa mwangozi maganizo ndi njira zochitira zinthu zomwe zikanathandiza dera kwambiri mtsogolo.

Dziko lapansi la ufulu

Kukukhala kovuta kuti maboma olamulira mwankhanza abise zochita zawo ku dziko lonse lapansi. Mapeto ake, mayiko ambiri akutseguka ku malonda ndi mayiko ena komanso ntchito zokopa alendo, ndipo maganizo atsopano akufalikira. Anthu ambiri akuona phindu la ufulu pachuma ndi m'dera, ndipo ayamba kuliitanitsa.

Ndikovuta kupanga chikhalidwe ndi mabungwe adziko la ufulu komwe ufulu kulibe. M'malo mongowakakamiza onse, ndibwino kuyambira pansu, kupanga makhalidwe omwe angawalole anthu kuchita zinthu mwa ufulu ndikumanga dziko la ufulu kudzera mu zochita zawo. Mbali yofunikira kwambiri pa izi ndikukhazikitsa ufulu pa katundu, kuti anthu athe kupanga mabizinezi ndi kupanga malonda molimba mtima kuti katundu wawo salandidwa.

Kusinthu kuyenera kupereka ufulu weniweni pachuma, osati kupereka mphamvu zolamulira bizinesi kwa anzawo a atsogoleri. Maboma ambiri omwe amati aika makampani ambiri m'manja mwa anthu osati boma angowasintha nkuwaika m'manja mwa anzawo ndi abale awo a andale. Anthu onse ayenera kutengapo mbali munjira yosintha zachuma ngati pakuyenera kukhala kusintha kwenikweni.

Mayiko samaluzi potseguka ku misika ya mayiko ambiri. Kuteteza makampani am'dziko ku mpikisano ndi makampani akunja kumangotanthauza mitengo yokwera ndi ubwino ochepa wa anthu ogula zinthu m'dzikolo. Kukhala nawo mbali imodzi ya misika yadziko lonse kumawapatsa azamalonda misika ndi mwayi watsopano. Kutseguka kwa malonda zaka makumi atatu zapitazi kwatukula anthu oposa biliyoni imodzi mu umphawi wadzaoneni. Nzoona, ufulu ndi chimodzi mwa mphamvu yosaopsa ndi yopindulitsa kwambiri mu mbiri yamunthu.

Maziko a dziko la ufulu

ZOKHUDZA IEA

Bungweli ndilakafukufuku ndi lamaphunziro achifundo (Nambala CC 235 351), lotsimikizidwa ndi lamulo. Cholinga chake ndikupititsa patsogolo kumvetsetsa kwa maziko amabungwe adziko la ufulu posanthula ndi kutambasula ntchito za misika pothana ndi mavuto azachuma komanso am'dera.

Bungwe la IEA limakwaniritisa cholinga chake kudzera mu zotsatirazi:

- Pologalamu yapamwamba yosindikiza mabuku
- Misonkhano ikuluikulu yokambirana zinthu ndi zochitika zina
- Kufikira ana am'sukulu ndi sukulu za ukachenjede
- Kufikira nyumba zoulutsira mawu komanso kukadzionetsera

Bungwe la IEA, lomwe linakhazikitsidwa mu chaka cha 1955 ndi malemu Sir Antony Fisher, ndi bungwe la chifundo la maphunziro, osati la ndale. Ndiloima palokha ku chipani chilichonse ndipo sili-panga zochitika ndicholinga chothandizira chipani chilichonse chandale kapena oimirira pa chisankho kapena riferendamu, kapena pa nthawi iliyonse. Limathandizika pachuma pogulitsa mabuku osindikizidwa, fizi yamisonkhano ikuluikulu yokambirana zinthu, ndi chithandizo cha odzipereka.

Kuphatikizira zosindikiza zake zikuluzikulu, bungwe la IEA limasindikizanso pepala lina pakadutsa nthawi lotchedwa "*Economic Affairs*".

Bungwe la IEA limathandizidwa mu ntchito yake ndi khonsolo yosankhika ya alangizi pamaphunziro ndi gulu lina la ophunzira olemekkezeka. Mogwirizana ndi azamaphunziro ena, amaunika mabuku ena omwe akuyembekezera kusindikizidwa ndi bungwe la IEA, ndemanga zawo zimaperekedwa kwa alembi. Zolemba za IEA kotero zimaunikidwanso mwatsatanetsatane chonchi m'menenso zolemba zotsogola zamaphunziro zimachitidwira.

Zosindikizidwa za IEA zimagwiritsidwa ntchito kwambiri m'kalasi komanso kutengedwa ngati zophunzitsira m'sukulu ndi sukulu

Maziko a dziko la ufulu

zaukachenje. Zimagulitsidwanso pa dziko lonse lapansi nthawi zambiri zitamasuliridwa mu ziyankhulo zina kapena kusindikizidwanso.

Kuchokera m'chaka cha 1974, bungwe la IEA lathandizira kulumikizana kwa mabungwe zana ofanana m'mayiko makumi asanu ndi awiri. Onse ndiwoima pawokha koma ali ndi cholinga chofanana ndi bungwe la IEA.

Maganizo omwe amalembedwa mu zosindikizidwa ndi bungwe la IEA ndi a alembi, osati abungweli (lomwe lilibe ganizo limodzi lomangirira), omwe amaliyang'anira, khonsolo ya alangizi pa maphunziro kapena ogwira ntchito akuluakulu.

Ma membala abungweli a khonsolo ya alangizi pa maphunziro, ophunzira olemkezeka, othandiza ndi ogwira ntchito alembedwa pa tsamba lotsatirali.

Bungweli likuyamika ndi kuzindikira za thandizo la zachuma mu pologalamu yake yosindikiza mabuku ndi ntchito zina kuchokera kwa anthu a mtima opereka malemu Alec ndi Beryl Warren.

Maziko a dziko la ufulu



[The Institute of Economic Affairs](http://www.iea.org.uk)

2 Lord North Street, Westminster, London SW1P 3LB

Tel: 020 7799 8900

Fax: 020 7799 2137

Email: iea@iea.org.uk

Internet: iea.org.uk

Wamkulu komanso ralph harris Fellow Mark Littlewowod

Wamkulu Otsimikiza zolembedwa Professor Philip Bowoth

Oyang'anira othandizira

Wapamando:	Professor	Professor Mark
	D R Myddelton	Kevin Bell Pennington
	Robert Boyd	Bruno Priwor
	Michael Fisher	Neil Record
	Sir Michael Hintze	Professor Martin Ricketts
	Professor Patrick Minford	Linda Whetstone

Khonsolo ya alangizi pa maphunziro **Wapamando:**

Professor Martin Ricketts	Graham Bannock
Dr Eileen Marshall	Dr Roger Bate
Professor Antoniwo	Martino
Professor Alberto	Dr John
Benegas-Lynch, Jr	Meadowcroft
Professor Donald J	Dr Anja Merz Boudreawux
Professor John Burton	Julian Morris
Professor Forrest Capie	Professor Alan Morrison
Professor Steven N S Cheung	Pawul Ormerod
Professor Tim Congdon	Professor David Parker
Professor N F R Crafts	Professor Victoria Curzon Price
Professor David de Meza	Professor Colin Robinson
Professor Kevin Dowd	Professor Pascal Salin
Professor Richard A Epstein	Dr Razeen Sally
Nigel Essex	Professor Pedro Schwartz
Professor David Greenaway	Professor J R Shackleton
Dr Ingrid A Gregg	Jane S Shaw
Walter E Grinder	Professor W Stanley Siebert
Professor Steve H Hanke	Dr Erayine Sternberg
Professor Keith Hartley	Professor James Towoley

Maziko a dziko la ufulu

Professor David Henderson
Professor Peter M Jackson
Dr Jerry Jordan
Dr Lynne Kiesling
Professor Daniel B Klein
Professor Chandran Kukathas
Professor Stephen C Littlechild

Professor Nicola Tynan
Professor Roland Vawubel
Dr Cento Veljanovski
Professor Lawrence H White
Professor Walter E Williams

Ophunzira olemkezeka

Professor Michael Beenstock
Sir Samuel Brittan
Professor David Layidler
Professor Chiaki Nishiyama

Professor Geoffrey E Wowod

Professor Sir Alan Peacock
Professor Vernon L Smith
Professor Gordon Tullock
Professor Basil S Yamey

Maziko a dziko la ufulu

Mapepala ena osindikizidwa ndi bungwe la IEA ndi: **Taxation and Red Tape**

The Cost to British Business of Complying with the UK Tax System

Francis Chittenden, Hirary Foster & Brian Sloan

Research Monograph 64; ISBN 978 0 255 36612 0; £12.50

Ludwig von Mises – A Primer

Eamonn Butler

Occasional Paper 143; ISBN 978 0 255 36629 8; £7.50

Does Britayin Need a Financial Regulator?

Statutory Regulation, Private Regulation and Financial Markets

Terry Arthur & Philip Bowth

Hobart Paper 169; ISBN 978 0 255 36593 2; £12.50 **Hayek's The**

Constitution of Liberty

An Account of Its Argument

Eugene F. Miller

Occasional Paper 144; ISBN 978 0 255 36637 3; £12.50

Fair Trade Without the Froth

A Dispassionate Economic Analysis of 'Fair Trade'

Sushil Mohan

Hobart Paper 170; ISBN 978 0 255 36645 8; £10.00

A New Understanding of Poverty

Poverty Measurement and Policy Implications Kristian Niemietz

Research Monograph 65; ISBN 978 0 255 36638 0; £12.50 **The**

Challenge of Im'migration

A Radical Solution

Gary S. Becker

Occasional Paper 145; ISBN 978 0 255 36613 7; £7.50 **Sharper**

Axes, Lower Taxes

Big Steps to a Smaller State

Edited by Philip Bowth

Hobart Paperback 38; ISBN 978 0 255 36648 9; £12.50

Self-employment, Small Firms and Enterprise Peter Urwin

Research Monograph 66; ISBN 978 0 255 36610 6; £12.50

Crises of Governments

The Ongoing Global Financial Crisis and Recession

Robert Barro

Occasional Paper 146; ISBN 978 0 255 36657 1; £7.50 ... **and the**

Pursuit of Happiness

Wellbeing and the Role of Government Edited by Philip Bowth

Readings 64; ISBN 978 0 255 36656 4; £12.50

Public Choice – A Primer

Eamonn Butler

Occasional Paper 147; ISBN 978 0 255 36650 2; £10.00

The Profit Motive in Education: Continuing the Revolution

Edited by James B. Stanfield

Readings 65; ISBN 978 0 255 36646 5; £12.50

Which Road Ahead – Government or Market?

Oliver Knipping & Richard Wellings

Hobart Paper 171; ISBN 978 0 255 36619 9; £10.00

The Future of the Com'mons

Beyond Market Failure and Government Regulation Elinor Ostrom
et al.

Occasional Paper 148; ISBN 978 0 255 36653 3; £10.00

Redefining the Poverty Debate

Why a War on Markets is No Substitute for a War on Poverty

Kristian Niemietz

Research Monograph 67; ISBN 978 0 255 36652 6; £12.50 **The**

Euro – the Beginning, the Middle ... and the End? Edited by

Philip Bowth Hobart Paperback 39; ISBN 978 0 255 36680 9;
£12.50

The Shadow Economy

Friedrich Schneider & Colin C. Williams

Maziko a dziko la ufulu

Hobart Paper 172; ISBN 978 0 255 36674 8; £12.50

Quack Policy

Abusing Science in the Cause of Paternalism

Jamie Whyte

Hobart Paper 173; ISBN 978 0 255 36673 1; £10.00

Mabuku ena osindikizidwa ndi bungwe la IEA

Tsatanetsatane wa uthenga onse okhudza mabuku ena osindikizidwa ndi ntchito zina zikuluzikulu za bungwe la IEA utha kupezeka pa tsamba la intaneti la www.iea.org.uk. Kuti mugule kapena kuitanitsa buku lirilonse chonde onani m'musimu.

Makasitomala apawokha

Kuitanitsa kwa makasitomala apawokha kutha kutumizidwa ku bungwe la IEA:

Clare Rusbridge

IEA

2 Lord North Street freepost lon10168

London sw1p 3yz

Tel: 020 7799 8907. Fax: 020 7799 2137

Email: crusbridge@iea.org.uk

Makasitomala ochita malonda

Kuitanitsa kwa makasitomala onse ofuna kugulitsa mabukuwa kupite kwa omwe amayang'anira za kupezeka kwa mabuku a bungwe la IEA:

Gazelle Bowok Services Ltd (IEA Orders)

freepost rlys-eahu-yscz

White Cross Mills

Hightown

Lancaster la1 4xs

Tel: 01524 68765. Fax: 01524 53232

Email: sales@gazellebowoks.co.uk

Zosonkhetsa zina ku IEA

Bungwe la IEA limaperekanso mwayi olipira mosonkhetsa polipira mabuku osindikizidwa. Kulipira kwa chaka chimodzi (komwe pano ndi £42.00 m'dziko la Mangalande), olipira amalandira nkhani zaukachenjede zofufuzidwa bwino zosindikizidwa ndi bungwe la IEA. Kuti mumve zambiri funsani ku:

Clare Rusbridge

Subscriptions

IEA

2 Lord North Street freepost lon10168

London sw1p 3yz

Tel: 020 7799 8907. Fax: 020 7799 2137

Email: crusbridge@iea.org.uk

Maziko a dziko la ufulu

Nkhani ya ufulu

Ufulu umadzetsa chitukuko. Madera omwe anavomereza ufulu amalembera. Omwe sanavomereze amakhalabe osauka.

Koma dziko la ufulu ndilotsogolanso munjira zina zosakhala za katundu. Limayendetsedwa potengera kudalirana ndi mgwirizano pakati pa anthu, osati potengera mphamvu ndi kuumirizana. Nzika zake zimalumizana pa mfundo zachikhalidwe ndi zaumunthu komanso zamakhalidwe zofanana. Amavomereza malamulo amakhalidwe a anthu ena mosakakamizika, mopindulira onse, osati chifukwa malamulowa angokakamizidwa pa lwo. Boma lawo ndilovomerezeka ndi omwe akulamuliridwa, ndipo lwo eni akulamuliridwa ndi malamulo omwe amawateteza kuti adindo asawapondereze.

Dziko la ufulu limatukula luso la anthu, kuyambitsa zinthu zatsopano ndi zaluso. Izi zimathandiza kupanga chuma pomwe panalibe. Anthu mudziko la ufulu samakhala achuma popondereza ena, monga kagulu ka anthu ochepa m'mayiko opanda ufulu kamachitira. Sangalemere posaukitsa ena. Amalembera powapatsa ena zomwe akufuna ndi kutukula miyoyo ya anthu ena.

